

# CHIBVUMBULUTSO, MUTU FORO GAWO III



Zikomo inu M'bale Neville. Ambuye akudalitseni inunso.

Ndipo mmawa wabwino, kalasi ya Baibulo. Ndipo aliyense akumverera bwanji mmawa uno? Bwino, ine ndikuyembekeza. Ameni. Tinakhala ngati...ichi chinali ngati chidziwitso chapafupi chomwe ife tinali nacho chonena kuti ife tikhala pano mmawa uno, chifukwa ine ndinalibe...mayendedwe anga okonzedweratu apobe a mmene ine ndiyendere. Ndipo izi tsopano kuti zapangidwa kwa miyezi sikisi ikubwerayi, chabwino, ndiye, ine ndinaganiza kulibwino tikhale ndi msonkhano mmawa uno chifukwa papita kanthawi ine ndisanabwerere konse, monga momwe ine ndikudziwira; mwina chilimwe ichi.

<sup>2</sup> Ndipo ndidza...ife tizinyamuka tsopano sabata ikubwerayi kupita ku Beaumont, Texas, kumene ife tidzayambira kumeneko sabata yotsatira ndi kudutsa pafupifupi msonkhano wa masiku eyiti kapena teni kumeneko ndi mgwirizano wa—wa odziyimira pawokha ndi mipingo yosiyana. Iyo ndi yothandizidwa kwenikweni ndi mipingo ya *Jesus Name* uko ku Beaumont, Texas, kumene ife tinali ndi msonkhano waukulu nthawi ina yapitayo, chithunzi *ichi* chitangojambulidwa kumene. Ndipo iwo...Ine ndikudziwa iwo amayendetsa kochi kupita kumeneko ndi, ine ndikukhulupirira, makochi twente seveni...kapena sitima yokhala ndi makochi twente seveni pa iyo, kubwera ku msonkhano ku Beaumont. Kumeneko ndi kumene meya wa tauniyo anali ndi perete ndi kumadutsa m'misewu, ndi onse a iwo. Tinali ndi nthawi yabwino ku Beaumont, ndipo ife tikubwerera sabata yamawayi. Ndiyeno ndimayembekezera San Antonio, koma sindikhala ndi nthawi yokwanira ya uko, pokhapokha pobwerera.

<sup>3</sup> Ndipo ife tipita kuchokera kumeneko kupita ku Phoenix, Los Angeles, kumusi ku Long Beach. Ndipo kenako ife tibwerera, Ambuye akalola, kubwerera ku Gombe la Kummawa, kubwerera ku Virginia ndi South Carolina. Kubwerera kenako ku Bloomington, Illinois. Ndipo kuchokera kumeneko kupita ku Lane Tech High School, sabata yatha mu Epulo, Amuna amalonda Achikhristu. Ndipo kenako ine ndichoka kumeneko kupita kumpoto kwa British Columbia, kumtunda chaku Alaska, ndi kukakhala mmenemo mpaka Juni. Ndipo, ndiye, ife tikuyembekeza kukakhala ndi nthawi yopambana.

<sup>4</sup> Kupemphera ndiye ngati kufufuza kwa...komwe ndakhala

ndiri nako kwa kanthawi ndi msonkho wa ndalama, zokhudza mpingo kuno, zidzakhala zitatha pofika nthawi imeneyo. Ndipo kenako tidza. . . Ine ndidzakhoza kupita kutsidya kwa nyanja ndiye ngati izo ziri, cha mu Juni, zomwe zidzapangitse izo kukhala zoyenera basi ku Africa; kwa Juni, Julayi, ndi Ogasti, mu—mu Africa. Kotero ine ndithudi ndikusowa mapemphero anu.

<sup>5</sup> Ndipo ife tikuyembekezera kudza kwa Ambuye. Zinthu zonsezi ziri “ngati chiri chifuniro cha Ambuye,” mwaona. Ife sitikudziwa, Iye akhoza. . . Izi sikutsogolera ndendende, ife tangotenga zoyitanidwa zonse pamodzi ndipo tazipempherera izo, kuwafunsa Ambuye, “Kodi tiyenera kupita njira iti?” Ndipo—ndipo zinkawoneka ngati, ndiye, ine sindimazisiyira izo zonse kwa ine ndekha, ine ndimalola ena aganize pa izo, kuzipempherera izo. Ndiyeno zinkawoneka ngati kuti ife tonse tinkawoneka ngati tikumverera kutsogozedwa kupita chakumadzulo, kummwera ndi kumadzulo pa nthawi imeneyi. Kotero ndiye ife tinali ndi kuyitanidwa pozungulira ponse, kotero ife tinangoyambira kumunsi konko. Ndipo malo oyamba anagwera pa mtima wanga anali mwina Beaumont kapena San Antonio. Kotero ife tinayang’ana, ndipo ife tinali ndi kuyitanidwa m’ malo onse awiri. Ndipo a. . .

<sup>6</sup> Ife tinayimbira mmodzi ku Beaumont. Ndipo pokhala kuti iwo anali nayo mipingo forte thuu mu mgwirizano, a United Pentecostal ndi ena otero, ife tinaganiza ndi holo yaikulu zikanakhala bwino kuti tiwapatse iwo, pafupifupi masiku teni mmalo mopereka faivi ndi faivi kumalo aliwonse. Ine ndikuganiza ngati inu mutaziyika izo pakatikati monga choncho nzabwinoko. Ndiye, kuli ochuluka a—a anthu osowa kuzungulira mu Beaumont ndi kudutsa chigawo cha mafuta chimenecho cha Texas uko, ndipo kotero ife tikuyembekezera nthawi yopambana mu Beaumont.

<sup>7</sup> Ndipo, tsopano, ife sitimayesera konse kupita kumene kuli mabwalo aakulu ndi malo aakulu. Koma ife timayesera kupita monga Ambuye atitsogolera ife kuti tizipitira, ziribe kanthu ndiochepa bwanji kapena ndiaakulu bwanji, basi bola ngati Ambuye akutsogolera. Tsopano, pa nthawi iliyonse, Iye akhoza kutipatsa ife kuitana kwa ku *Makedoniya* ndipo ife tingachoke mmunda nthawi iliyonse ku chirichonse chimene Iye angatiyitanire ife kuti tichite, kulikonse.

<sup>8</sup> Ndipo ife ndithudi tasangalala nayo nthawi iyi ya chiyanjano mozungulira Mawu a Mulungu ndi inu anthu abwino. Ine ndikudalira kuti mukhala okhulupirika tsopano ndi kubwera ku tchalitchi ndi kumvera ziphunzitsa za Baibulo kudzera mwa m’bale wathu wolimba pano, M’bale Neville, yemwe ine ndikumuyamikira kwambiri ngati wantchito wa Ambuye Mulungu, ndi kumasuntha mwakuya ndi mwakuya

ndi Mulungu, ndipo ndine wokondwa kwambiri chifukwa cha zimenezo.

<sup>9</sup> Ndipo mpingo wawung’ono, ine ndikukulimbikitsani inu mu Dzina la Ambuye Yesu kuti mukule mu chisomo cha Mulungu, dzikhazikitseni nokha ndi kuyang’ana ku Kalvare nthawi zonse, kuchotsa mizu yonse ya kuwawidwa kuchoka mu mtima mwanu ndi mu solo, kuti Mulungu akhoze kukugwiritsani inu ntchito pa nthawi iliyonse. Ngati inu mukumverera kuti muchite chinachake, kapena vumbulutso kapena chinachake chikabwera kwa inu mwachirendo, chinachake chochenjeza kapena chinachake, khalani osamala! Satana ndi wotheyathyalika ndi wochenjera monga momwe iye angakhalire. Mukuona? Ziyikeni izo pamodzi ndi Mawu a Mulungu ndipo funsani abusa anu. Mukuona?

<sup>10</sup> Ndipo inu mumapeza mphatso ndi zina zotero zikukwawira mu mpingo, ndi kachitidwe ka mphatso zimenezi. Musanazilole izo kuti ziyambe kugwira ntchito ndi zinthu, choyamba... Muzimverere izo zikukanikiza pa mtima wanu... Tsopano, mdaniyo ndi wochenjera kwenikweni. Mukuona? Ndipo ndizo basi zomwe zimang’amba mipingo mzidutswa nthawi iliyonse, ndi mphatso yowona yoyendetsedwa molakwika. Mwaona? Chinachake chimene Mulungu akuyesera kuchita, ndipo nkuchitidwa molakwika, icho chidzango—icho mophweka chidzango... Osati kungokupwetekani inu, koma izo zidzawung’amba mpingo wonsewo. Mukuona? Zifufuzeni izo, zitengereni izo modutsa ndi kudzera mu Baibulo, ndiye ziyeseni izo ndi kuwona ngati ali Mulungu kapena ayi. Zingopitirirani kuziyesa izo ndi kuyesera, muwone ngati ziri zangwirowo pansu pa mzere ndi zolondola ndi Mawu. Ndiye inu muli bwino, mwaona.

<sup>11</sup> Bola ngati Mawu anena kuti izo zikanadzakhala pano, zikanadzagwira ntchito mwanjira inayake iyi, khalani nayo iyo. Musachokepo konse, ziribe kanthu zomwe aliyense angachite, momwe izo zikuwonekera kukhala zenizeni. Ngati izo sizikunyezimira mu Malemba kuchokera ku Genesis mpaka Chivumbulutso, zisiyeni izo zokha. Musatengere mwayi ayi, ife tiri m’masiku otsiriza pamene Satana ali wonyenga basi monga momwe iye angakhoze kukhalira.

<sup>12</sup> Ndikhululukireni ine ngati ndikuyesera kutenga malo a bwana; Sindine bwana. Koma ine ndikumverera kwa inu monga Paulo ananenera kumbuyo uko za osonkhana ake kamodzi, “Inu ndinu nyenyezi mu korona wanga.” Pamene ine ndidzawoloka dziko uko kutsidya linalo, ndi kudzakumana nanu inu mu chikhalidwe chaulemerero chimenecho, Ine ndikufuna inu mudzayime pamenepo kuti muwale ngati nyenyezi mu korona wanga. Mukuona? Ndipo ine—ine ndikufuna kuti inu mukakhaleko, ine ndikufuna kukakhala kumeneko.

<sup>13</sup> Ndipo ine ndikukumbukira mu masomphenya anga pamene

ine ndinawona Kukhalapo kwa Ambuye, kapena anthu Ake mu Dziko laulemerero kutsidya uko, Ine ndinayang'ana pozungulira, ndinawauza iwo...Ndipo iwo anandiuza kuti Iye akanati andiweruze ine poyamba ndi Uthenga umene ine ndimalalikira. Ine ndinati, “Ndendende basi momwe Paulo analalikirira Iwo!”

<sup>14</sup> Ndipo mamiliyoni awo a anthu anakuwa, “Ife tikupumula pa zimenezo!” Mukuona? Mwaona. Tsopano, ine ndikufuna kuti izo zikhale choncho. Ndipo ife tidzakumana kumeneko tsiku lina.

<sup>15</sup> Ndipo Mulungu sanatume konse M'bale Neville ndi ine kuti tidzakhale mabwana, osati konse. Ndife basi abale anu, inu mukuona, alangizi mu Uthenga. Kotero tiyeni tonse tigwire ntchito limodzi.

<sup>16</sup> Ndipo nthawi zina ngati—ngati chinachake chikugwira ntchito chiyenera kutchulidwa kapena—kapena kunena kanthu za icho, kutchulidwa kapena chinachake pa dongosolo limenelo, ndipo munthu yemwe ali nayo mphatso imeneyo nkuzikana izo, ingokumbukirani...kuzikana izo, kumbukirani, mphatsoyo sinali yolondola. Sanali Mulungu kuyamba nkuyamba. Mzimu wa Mulungu nthawizonse umakhala wokonzekera kukonzedwa, wokoma ndi wodzichepetsa, wololera. Mwaona. Ngati uyimilira ndi kunena “Ine ndichita izo mulimonse,” inu mukudziwa momwe nthawi ina...Ingokumbukirani, mizimu yodzikuza si ya Mulungu. Mwaona? Kotero mutengeranji choloweza mmalo pamene chirichonse, dziko lonse lapansi, ladzaza ndi Ulemerero wa Mulungu, inu mukuona, mphamvu yeniyeni ya Mulungu. Chifukwa chiyani ife tikutenga choloweza mmalo? Ife tachedwa kwambiri mu tsikuli tsopano; koma, kumbukirani, Baibulo lanena kuti iye adzabweramo monga a...mochenjera basi monga iye akanakhoza kukhalira, ndi kudzanyenga Osankhidwa omwe ngati nkotheke. Mukuona?

<sup>17</sup> Ndipo, tsopano, nthawizina ife timaganiza kuti ndife Osankhidwawo, ndipo ine ndikuyembekeza ife tiri, koma tiyeni tikhale molunjika kumene ndi Baibulo. Ndipo ndiye ngati chirichonse chiri cholondola ndi Lemba, ndi dongosolo mu Lemba, kubweretsa Ulemerero kwa Mulungu ndi ulemu wa mpingo, ndi zina zotero, ndiye ife timadziwa kuti izo ndi za Mulungu chifukwa Baibulo limaikira izo kumbuyo. Koma malingaliro athu okha sangayikire izo kumbuyo, izo sizingachitire ubwino, icho chimagwapo.

<sup>18</sup> Kotero ndiye ngati chinachake chatikhudza ife, ziribe kanthu momwe chikuwonekera chenicheni, ngati sichiri cholondola, chosakhala Mwamalemba, chichotseni icho pakali pano; chifukwa pali—pali Chimodzi chenicheni chikudikira, inu mukuona.

<sup>19</sup> Kotero, pempherani tsopano. Ndipo nthawizonse, ndipo chirichonse chimene inu muchite, mundipempherere ine.

Mundipempherere ine chifukwa ife tsopano tikukakhudza minda kwa nthawi zotsiriza, mwa lingaliro langa. Ife tsopano tikupita . . .

<sup>20</sup> Ndipo, kumbukirani, zinthu zazikulu zikuchitika, izo sizikudziwika pakati pa dziko. Yesu anabwera, anakhala moyo, anafa, ndipo anapereka nsembe, anabwerera ku Ulemerero, ndipo mamilioni sankadziwa nkomwe kalikonse za izo. Mukuona? Siziri zamaluwa, zopambana, zazikulu; ndi “Iye anabwera kwa Ake Omwe,” mwaona. Ndipo a . . . “Iye amene ali nalo khutu amve chimene Mzimu anena kwa mipingo.” Osati kunja, “kwa Mpingo.” Ndi Mpingo umene umapeza kugwedeza Kwake.

<sup>21</sup> Ine ndinkakonda kuganiza mosiyana ndi zimenezo kufikira tsiku lina Iye anayankhula kwa ine; anandipangitsa ine kuti ndibwerere mu Mawu ndi kuganiza za momwe kuti aneneri onse ankayankhula pamene Yohane anabwera, anati, “Malo okwera adzatsitsidwa, ndipo malo otsika adzakwezedwa.” Ndi momwe mphamvu ya Mulungu ikanadzagwirira ntchito! Ndipo a—a . . . “Mapiri onse akanadzadumpha ngati ana a nkhosa, ndipo masamba akanadzawomba m’manja.” Chabwino, izo zinkawoneka ngati chinachake kwenikweni chinali choti chichitike. Mukuona? Ndipo pamene izo zinatero, nchiyani chinachitika? Munthu wachikulire anatuluka m’chipululu, mwinamwake ndevu zitakula ponsepo ndi chidutswa chakale cha chikopa chankhosa chitakulungidwa pa iye. Kunalibe zabwino kunja uko mu chipululu. Iye anali kumeneko kuyambira pamene iye anali usinkhu wa zaka naini, ndipo iye anali ndi sarte pamenepo. Anabwera akuyenda kuchokera m’chipululu, kuthamangira kunja, akulalikira kulapa, atayima m’matope mpaka m’maondo ake, mwinamwake, m’mphepete mwa Yordano. Ndipo ndi pamene malo okwera anatsitsidwa ndi malo otsika anakwezedwa. Mukuona? Ndi . . .

<sup>22</sup> Inu muyenera kukhala nako kumvetisa kwauzimu. Kumbukirani, Mulungu sanachitepo ndipo sadzatero konse, pa dziko lapansi lino, kukhala mu kukongola. Iye amatsutsana nazo. Iye sadzatero konse . . . Mauthenga aakulu sadzakhala konse “kupanga zazikulu *zakuti-ndi-zakuti* ndi *zakuti-ndi- . . .*” Izo sizimachita mwanjira imeneyo. Atumiki ake samagwira ntchito mwanjira imeneyo. Kukongola kwake ndi ulemerero ndi zakumwamba.

<sup>23</sup> Dzulo, kapena masiku awiri apitawo, ndikupita ku Kentucky, uko mu Kentucky ndi mzanga wabwino, M’bale Banks Wood, apo panali wapolisi wamkazi atayima kunja uko, ndipo iye anati, “Mnyamata, ife kulibwino tichepetse liwiro,” anati, “ndi wankhanza.”

<sup>24</sup> Ndipo ine ndinati, “Eya, ndiko kulondola.” Ine ndinati, “Fuko likafika pomwe anthu mamiliyoni ambiri alembedwa

ntchito ndipo iwo akuyenera kutenga akazi, kuwapanga apolisi aakazi ndi kuwatumiza iwo kunjja uko, ndi oyendetsa galimoto ndi zinthu monga izo, ndi chimodzi mwa madontho aakulu pa fuko lathu.” Iye basi ali ndi zochita zochuluka kunjja uko monga a—monga kalulu ali nazo mu ketulo ya mafuta. Mukuona? Iwo basi—iwo basi—si malo ake. Ndipo ine ndinati, “Izo zinkandivutitsa ine moyipa kwambiri, koma tsopano ndikuyamba kukumbukira, ‘Bwanji, nzosadabwitsa, uwu ndi—uwu si ufumu wathu, sitiri a dziko lapansi lino.” Iwo atero... inu... .

<sup>25</sup> Bwanji akazi (akazi athu) samakhala nalo lawo—tsitsi lawo lalifupi, ndi zopakapaka, ndi magwedemula, ndi zinthu zonse izi? Bwanji, anthu amapita ku mipingo wamba ndi zinthu, kumaganiza, “Izo ndi zabwino.” Chifukwa chiyani? Iwo... iwo—iwo ndi Achimerika; iwo ndi Achimerika, ali ndi mzimu wa Chimerika. Iye sitiri Achimerika, ndife Akhristu. Tikukhala moyo... mzimu wathu ndi wa Ufumu wina. Ngati mzimu wathu ukanakhala wa ufumu uwu ndiye ife tikanapembedza ndi zinthu izi, ndiye ife tikanapembedza nyimbo zonse zonyansa izi ndi kupembedza gwedemula yense uyu. “Kulikonse kumene kuli mtima wako, komweko kuli chuma chako.” Ndipo chuma chatu chiri kumwamba. Kotero choncho ife tikupita ku Ufumu.

<sup>26</sup> Kuno si kwathu, ife tikungoyendayenda kuno kuyesetsa kuti titulutse nzika zina kuchoka mumdima. Ndi kupita mu mzinda ndipo mwinamwake ine ndimakhala ndi msonkhano wa mzinda wonse, ndimangogalauza kwa sabata kapena masiku teni, kwa moyo umodzi wa mtengo wapatali kunjja uko; mmodzi, mmodzi yekha atakhala kunjja kumeneko.

<sup>27</sup> Inu mukhoza kunena, “Msonkhanowo unali wopambana kwambiri, faivi sauzande anabwera ku guwa”; pakhoza kukhala popanda mmodzi wa iwo wopulumutsidwa, popanda mmodzi wa iwo. Mwaona? Ndipo pakhoza kukhala... Inu mukhoza kuganiza pamenepo, “Anthu awiri okha ndi amene anabwera pa guwa”; koma mmodzi wa iwo akhoza kukhala ngale. Iye basi timangowedza mu mtsinje. Mulungu amasankha nsombayo, Iye amadziwa imene ili nsomba ndi yomwe siili.

<sup>28</sup> Kotero, mukuona, ife tikungolalikira. Ndipo kumbukirani kuti inu mukuchita chinthu chomwecho mu kachisi muno. Koma kumbukirani izi nthawi zonse, “Nkhosa Zanga zimadziwa Liwu Langa.” Ndipo Liwu la Mulungu ndi Mawu Ake.

<sup>29</sup> Ine ndinali kuganiza tsiku lina momwe anthu awa amene amanena kuti sipanakhalepo... Gulu lina la mipingo likunena kuti, “Machiritso Auzimu sanali olondola. Palibe aliyense amene anapatsidwa mphatso ya machiritso Auzimu koma Paulo Woyera kapena atumwi, thwelovuwo m’chipinda chapamwamba. Iwo anapatsidwa mphatso ya machiritso Auzimu, ndipo izo zinali zonse. Izo zinakhazikitsa icho.”

<sup>30</sup> Koma, inu mukuona, kudzera mu chojambula chodabwitsa ichi chimene M'bale Willie, cha apa, modabwitsa kwambiri anatikonzera ife, ulusi wawung'ono uwo wakhala ukudutsa m'mipingo njira yonse. Ine ndikudabwa chimene chipembedzo chomwecho chikunena za mbiriyakale ya mpingo, za Ireniyasi, za Marteni Woyera? Ndipo ofera onse awo kudutsa mu m'badwo, kwa ma handiredi a zaka pambuyo pa imfa ya atumwi, anayankhula m'malirime ndi kuchiritsa odwala ndi kuwukitsa akufa ndi kuchita zozizwitsa, mpingo wonse. Ndikudabwa nanga bwanji iwo, ngati izo zinali kwa atumwi okha?

<sup>31</sup> Mwaona momwe ziliri zopapatiza? Iwo alibe kumvetsa kwauzimu, ndizo zonse. Mwaona, "Akhungu! Akufa mu tchimo ndi mphulupulu!" *Tchimo* limatanthauza "kusakhulupirira." Chirichonse mu kusakhulupirira ndi tchimo. Ngati munthu ali ndi u—udindo wautali *choncho* (wa D.D., ma L awiri., Ph.D., L.L.D.) ndipo nkumati "palibe chinthu chotero monga machiritso Auzimu kapena ubatizo wa Mzimu Woyera," munthuyo ndi wakufa mu tchimo. Iye akhoza kufotokoza mitundu yonse ya zinsinsi za m'Baibulo, koma moyo wake womwe (umboni wake) umatsimikizira kuti iye ndi wakufa. Iye ndi wakufa mu tchimo ndi mphulupulu chifukwa iye ndi wochimwa.

<sup>32</sup> Tchimo ndi kusakhulupirira. Aliyense ayenera . . . Tchimo, sikuchita chigololo ndi kusuta ndudu ndi kuvina ndi—ndi kumapitiriza monga choncho. Ilo si tchimo, ndizo zikhalidwe za kusakhulupirira. Koma a—wokhulupirira . . . Ziribe kanthu ngati munthu samamwa, samasuta, samachita zinthu izi, sananene konse mawu oyipa, amasunga Malamulo Khumi onse, iye akhoza kukhalabe wochimwa wakuda, mwaona, udindo basi monga iye angakhoze kukhalira. Ngati iye akana chirichonse cha mphamvu ya Mulungu, iye ndi wochimwa! Mawu akuti *tchimo* ndi "kusakhulupirira." Tsopano, inu mungopeza, muwone ngati izo ziri zolondola kapena ayi. Wosakhulupirira mu Mawu a Mulungu, iye ndi wochimwa ndipo sangalowe mu Ufumu wa Kumwamba.

<sup>33</sup> Tsopano, oh, ine ndinaganiza ndiye mmawa uno, kudzitengera izo pa inemwini mwa chifuniro cha Ambuye, mwa kulamalira kwa Mzimu Woyera, kuti ndibwere ku kachisi kachiwiri ndipo mwinamwake ndikusungeni inu nonse maora awiri kapena atatu. Koma ine ndikufuna kuti nditsirize bukhu la mutu wa 4 wa Chivumbulutso ndisanapite. Ndipo tsopano ine ndikuyembekeza izo sizotopetsa kwa inu, ine ndikuyembekeza ndi—ndi ulemerero kwa inu. Ine ndikuyembekeza kuti ndi chinthu chomwe chidzakuchitireni inu ubwino ndi kukuthandizani inu m'masiku akudzawa.

<sup>34</sup> Ndipo tsopano mwinamwake . . . Ine ndinamuza Billy kuti abwere kuno mmawa uno ndi kudzapereka makadi a pemphero ngati panali alendo aliwone pakati pathu, chifukwa ife tikhala

tikuchoka, ndipo...tsopano, ndipo sindikudziwa kuti ife tidzabwerera liti. Mulungu yekha akudziwa zimenezo. Ndipo ine ndimafuna...ndinaganiza mwinamwake msonkhano womaliza ngati...ndipo pamene iye anandiyimbira ine pamenepo pafupifupi—pafupifupi naini koloko ndipo anati, “Adadi, pali anthu ena kumeneko oti apemphereredwe. Ine ndinawafunsa iwo, koma” anati, “ndi anthu amene—ndi anthu amene amabwera ku tchalitchi nthawi zonse.”

<sup>35</sup> Ine ndinati, “Ndiye usapereke makadi apemphero aliwonse, mwaona.” Ine ndinati, “Chifukwa ndi anthu...Ngati ife tiri ndi pemphero la odwala mwawa uno, ife tiwayitana anthuwo ndi kuwapempherera iwo.” Koma ine ndinati, “Ngati iwo—ndi anthu amene amabwera ku kachisi amene ife timawadziwa...Ayi, ine ndikufuna mlendo winawake.”

<sup>36</sup> Ndipo iye anati ndiye, iye anabwera kunja uko maminiti pang’ono apitawo pamene iye anakumana nane nditayima kunja uko, anati, “Chabwino, ine ndinapereka makadi ena apemphero.” Anati, “Ochepa okha mmenemo, ine ndinapereka makadi apemphero.” Anati, “Inu mukhoza kuchita chirichonse chomwe inu mukufuna.”

<sup>37</sup> Ine ndinati, “Chabwino, ife tiona momwe uthengawo utayendere, tiona pamene ife tiri, ndiyeno ife tipita. Ine...”

<sup>38</sup> Iye anati, “Chabwino, ambiri a anthu amafuna makadi apemphero, ndithudi, koma” anati “iwo anali anthu amene ali mmenemo mu tchalitchi.” Mukuona?

<sup>39</sup> Chabwino, ife tikudziwa kuti Mulungu ndi Mulungu. Ndipo, mai, zinthu basi zimene Iye amachita! Bwanji, a—foni imalira nthawi zonse, ya anthu a zinthu zosiyanasiyana, za zinthu zazing’ono kwambiri nthawizina, ndi momwe Mulungu amayankhira pemphero!

<sup>40</sup> Ine ndikudabwa ngati dona wamng’ono uyo kapena mwamuna wake ali pano kuchokera uko ku New Albany, amene anabweretsa mwana wamng’ono wotsamwitsidwa uja usiku wina, ali ndi chibayo, mnyumba mwanga pafupifupi thwelovu, wani koloko? Apo, chabwino. Mwanayo ali bwanji? [M’bale akuti, “Ali bwino.”—Mkonzi.] Ali bwino, zabwino, chabwino.

<sup>41</sup> Ingondilolani ine ndikuwonetseni inu, mwaona, kuti ndi chinachake chimene inu simungachidziwe, izo sizimapitirira pamene Mzimu Woyera uyankhula. Fred Sothmann, m’bale wathu wofunika, Fred; Ine ndinamumva iye akunena “Ameni” kanthawi kapitako, koma ine sindinathe kumuzindikira iye. Iye ali pati? Kodi iye ali pano? Apa, pomwe pano, M’bale Fred Sothmann. Ndipo kusonyeza momwe ziliri zophweka... Iye anali nawo abwenzi ena akubwera, amene anali M’bale Welch Evans, ine ndikupenekera, sindikudziwa. Iwo anali ndi ngolo kumeneko; iwo anali atatseka zitseko ndipo Fred



anataya makiyi, ndipo anakhala akuyang'ana paliponse ndipo sanawapeze iwo paliponse. Ndipo M'bale Welch anali akubwera apo pomwe. Kotero tsiku linafika lomwe iye amayenera kuti afike ndi zinthu, iwo sanapeze makiyi paliponse, kotero iye anangoyimbira kunyumba, anati, "M'bale Branham, ali kuti makiyi? Kodi ife tingawapeze kuti iwo?"

<sup>42</sup> Tsopano, izo zikhoza kupunthwitsa ena a inu, kuti munthu afunse funso monga choncho. Koma dikirani miniti yokha, mukukumbukira ana aamuna a Jesse akufunafuna mphongolo? "Kotero ngati ine ndikanakhala ndi mphatso mdzanja langa, ndikanaitsitsa ndi kuyiwonetsa. . . kufunsa, kuyipereka iyo kwa mneneri, ndipo mwinamwake akanatiuza ife kumene mphongolo izo zinali." Mukukumbukira zimenezo?

<sup>43</sup> Ndipo pamene iye anali kuyenda mu msewu iwo anakumana ndi mneneri. Iye anati, "Inu mukufunafuna mphongolo zimenezo." Anati, "Uko, inu bwererani kunyumba," anati, "izo zabwerera kale." Ndi kulondola uko?

<sup>44</sup> Ine ndinapemphera. Fred anapita ndipo anakatenga makiyi. Ndi zimenezo. Mukuona?

<sup>45</sup> M'bale Ed Daulton, inu muli pati? Ed Daulton ali pati? Ine ndikudziwa iye ali pano penapake, ine ndinamuwona iye kanthawi kapitako. Oh, kumbuyo mkati. . . apo iye ali. Iye anandimva ine kudzera pa foni kapena polankhula ndi anthu. Usiku wina foni inabwera ndipo M'bale Ed anali mu vuto lalikulu. Ine ndinkafuna kuti ndimuthandize iye. "Ayi," anati, "Ine ndikungofuna kuti inu mumupemphe Mulungu." Ine ndinamupempha Ambuye kuti amuthandize iye. Ndipo tsiku lotsatira mkazi wake anayimba, winawake anabwera kudzamuthandiza. Chabwino. Ndi kulondola uko, M'bale Ed?

<sup>46</sup> Mwaona, Iye ndi Mulungu basi. Ndizo zonse, Iye ndi Mulungu basi. Mwaona, Iye basi. . . Zimakhala nthawi zonse mosalekeza kuchokera ku malo amodzi kupita ku ena, malo amodzi kupita ku ena. Ziribe kanthu kuti ndi vuto lanji, Iye ndi Mulungu. Ife sitimayenda mozungulira, nkumadzitamandira ndi zinthu zimenezo, ife sitiyenera kutero. Musalole kuti dzanja lamanja kapena lamanzere lidziwe zomwe dzanja lamanja likuchita. Ife timayankhula izo pakati pathu koma ife sitimiziphulitsa izo kwinakwake. Chifukwa ndiko kudzikiza, monga, "Mulungu akanakhoza kuchita izo kwa munthu mmodzi yekha." Iye akanachita izo kwa aliyense amene angafune—amene amukhulupirira Iye. Ndi kukhulupirira, chikhulupiriro! Chirichonse—chirichonse chimene inu mukufuna kuchita, chirichonse chimene malingaliro anu ali, chitengereni icho kwa Mulungu. Iye—Iye—Iye—Iye amapereka chirichonse. Kodi si kulondola uko? Kotero Iye amayankha pemphero. Iye ndi. . . Mulungu ndi Atate woyankha pemphero.

<sup>47</sup> Tsopano, choncho kotero mkati . . . Ine ndinaganiza, kutseka mu misonkhano yotsiriza iyi ndi zina zotero, monga ife tinali . . . momwe ife tikuchitira, ife tikhoza—ife tikanakhala mwinamwake ndi kuzindikira zam'mitima kwina pa mapeto pa msonkhano, ngati Ambuye alola, ndipo mwinamwake mu nthawi ya msonkhano. Ife sitikudziwa basi chimene Iye ati achite. Ine ndimazikonda izo mwanjira imeneyo. Musayike chinthu china chake, mungomulola Iye kuti achite monga Iye akufunira kuti achitire.

<sup>48</sup> Tsopano, tengani mutu wa 4 wa Bukhu la Chivumbulutso, ndipo imitsani kolokoyo.

<sup>49</sup> [M'bale akuyankhula kwa M'bale Branham—Mkonzi.] Inde. Inde, m'bale. [M'baleyo akupitiriza kuyankhuala. Malo osajambulidwa pa tepi.] Ndithudi, ine ndikukhulupirira zimenezo. Mwamtheradi, ndikukhulupirira zimenezo.

<sup>50</sup> Pano, M'bale Welch Evans, ine ndikuganiza ndi iye wakhala kumbuyo uko. Ndiloleni ine . . . Pamene ife tikutembenezira ku Chivumbulutso 4.

<sup>51</sup> Kuno osati kale kwambiri, inu nonse munamva ndi kuwerenga mmapepala za gulu ili ku Louisville lomwe limaba magalimoto awa, amawatengera iwo ku Kentucky kwinakwake, mwamsanga kwenikweni. Ndipo ku Kentucky simusowa kukhala ndi udindo, iwo amakupangani inu kukhala mmodzi ku Kentucky. Kotero inu basi . . . chinthu chokhacho chimene inu muyenera kuchita kuti muyitengere iyo kumeneko ndi kukayigulitsa iyo. Kotero iwo amatenga magalimoto awa ndi kuwapititsa iwo mkati ndi kuwapentanso iwo kachiwiri, ndi kubweretsa magalimoto amenewo ndi kuwagulitsa iwo. Zonse zomwe inu muyenera kukhala nazo ndi nambala yanu ya buloko yanu ndipo iwo—iwo adzakupangirani inu dzina. Kotero iwo amangoyichotsa galimotoyo mumsewu ndi kuyichotsa mofulumira kwenikweni ndi kuyilowetsa mu sitolo ina kwinakwake, kungosintha chinthu chonsecho palimodzi, mwaona, ndi—ndi kuyipentanso iyo ndi chirichonse, kuyitulutsa ndi kuyigulitsa. Pali chimpwiriti cha izo, ndipo makamaka kulikonse mu United States, ndipo zazikulu—zochulukana za izo ziri ku Kentucky. Ine ndinawerenga nkhani mu pepala kuno osati kale kwambiri za izo.

<sup>52</sup> Chabwino, wamkulu, wamtima wabwino, M'bale Evans wofunika ndi banja lake, akuyendetsa njira yonse kuchokera ku Macon, Georgia, kubwera kuno Lamlungu lirilonse kuti adzamve Uthenga. Oh, okhulupirika bwanji, ndipo ndi abwenzi enieni otani! Kenako iye amapita ku Cafeteria ya Miller komwe . . .

<sup>53</sup> Ine sindikuchemerera ya a Miller, koma ine ndithudi ndikuganiza kuti iwo ali ndi chakudya chapamwamba kwambiri mu Kentucky; Louisville, Kentucky, mulimonse.

Mpaka pano...Ine sindikutanthauza inu nyumba zapadera zomwe ine ndadyeramo uko, tsopano, ine ndikutanthauza kwa (inu mukudziwa) kunjako. Ndipo ine ndimadya kumeneko, inenso. Ine ndikhoza kudyetsa banja langa kumeneko motchipa kuposa momwe ine ndingawadyetsere iwo kunyumba. Uko nkulondola.

<sup>54</sup> Kotero ndiye ine ndimapita kumeneko, ndipo kotero M'bale Evans iye amalowa mmenemo ndipo iye amamupezera chinachake choti adye ndikuyimitsa galimoto yake kunja uko. Pamene iye anatuluka (ndi zovala zake zonse) ndi banja ndi onse a iwo, iye analibe galimoto kapena kalikonse. Zonse zinali zitapita. Chabwino, munthu wosauka, M'bale Evans ndi mwamuna monga ife tonse, iye ali ndi kabizinesi kakang'ono kumeneko, iye amagwira ntchito zamagalimoto, amagula zowonongeka ndi kuzikonza izo. Iye ndi munthu wosauka, ndipo amawononga ndalama zake kubwera kuno chifukwa iye amakhulupirira mu mtundu uwu wa Uthenga. Ine ndikupemphera kuti Mulungu awatumizire iwo mtumiki kumeneko kwinakwake, kuti akawathandize iwo uko mu dziko limenelo.

<sup>55</sup> Tsopano, M'bale Evans anabwerapo, kotero iye sankadziwa choti achite. Iye anawadziwitsa apolisi ndipo iwo sanakhoze kuipeza iyo. Kotero iye anadutsira kunyumba, iye ndi M'bale Fred ndi iwo, ife tinakhala mu chipinda ndipo tinayankhula za izo. Ine ndinati, "Tsopano..." Umo ndi momwe ife timachitira, ife timakhala mu chipindacho, kupeza chimene chitachitike, ndiyeno ife timapita kwa Mulungu. Kotero pamene ife tinampempha Ambuye, "Kuti amutembenuze munthu yemwe anali ndi galimotoyo, kumutembenuza iye ndi kumubweza iye, kulikonse kumene anali."

<sup>56</sup> Kawirikawiri amawathawitsira ku Bowling Green kapena kwinakwake, kuwachotsa iwo pamalo oti azionedwa pomwe pano, inu mukuona, kotero iwo akanakhoza...mpaka iwo atawapentanso iwo ndi kuwakonza. Iyi inali galimoto yabwino, ine ndikuganiza station wagon. Ndi kulondola uko, M'bale Evans? Iyo inali a—station wagon.

<sup>57</sup> Kotero, ndipo kotero chimene chinachitika, ife tinagwada pansu ndi kupemphera. Ndipo a—Ambuye anatipatsa ife umboni, zonse zinali bwino, chirichonse chinali bwino. Kotero ndiye mphamvu ya Ambuye inadza nafe. M'bale Evans anatuluka kunja ndi kukayamba kupita, anatsogozedwa kuti apite kumusi njira inayake.

<sup>58</sup> Iye anabwerera komwe kuno mu Jeffersonville. Galimotoyo inabedwa ku Louisville; apa panali galimoto yake itakhala pamenepo ili ndi pafupifupi mafuta okwanira oti ayitengere iyo...oh, kuchokera mmenemo, kuti nkuyitengera iyo kumunsi pafupifupi kumayandikira kwambiri ku Bowling Green ndi

kubwererako. Iwo anatuluka mu galimoto, anayiyimitsa galimotoyo, anasiya makiyi momwemo, anangochokapo ndi kuyisiya ili pamenepo, komwe kuno mu Jeffersonville kumene iye akanakhoza kuyipeza iyo; osati Louisville, kuno mu Jeff., anayibweretsa iyo njira yonse kubwerera.

<sup>59</sup> Inu mukudziwa, Ambuye akhoza kupangitsa mbalame kumumvera Iye, Iye akhoza kupangitsa anthu kumumvera Iye, Iye akhoza kupangitsa mdani wake kumumvera Iye. Iye . . . Inde, bwana, Iye ndi Mulungu. Apa panali galimoto yake popanda kanthu kamodzi katachotsedwa, pafupifupi basi theka la tanki la mafuta pomwe iye anali atatsala pang'ono kufika ku Bowling Green, ndipo Mzimu Woyera uyenera unati “Tembenuka! Bwerera kumbuyo uko ndipo uyitengere galimoto imeneyo ku Jeffersonville. Ikhazike pomwepa pamsewu, ndipo uyiyimitse iyo *pompano*, (chifukwa ine ndimutumiza iye mozungulira njira *iyi* ndi kumtunda njira *iyi* kuti adzayipeze iyo).” Ndi kulondola uko, M'bale Welch? Ndiko kulondola. Mwaona.

<sup>60</sup> Iye ndi Mulungu! Iye amayankha pemphero, M'bale Roy. Iye basi . . . Ndicho, M'bale Slaughter, ndicho chinthu chomwecho, Iye anachiza kagalu kanu kakang'ono. Ndipo ine ndikudziwa kuti Iye amachiritsa, Iye amayankha pemphero, Iye amachitabe zozizwitsa, Iye akadali Mulungu, Iye nthawizonse anali Mulungu, Iye nthawizonse adzakhala Mulungu!

Iye—Iye ndi Mulungu padenga la nyumba,  
(Ndi chiyani icho, m'bale ameneyo amayimba  
pano pa tchalitchi?)

Mulungu kukhitchini, Mulungu kunjira uko  
kumunda,

Mulungu mu galimoto, Iye ndi Mulungu  
kulikonse,

Iye ndi Mulunguponse—kudutsaponse ndi  
monse, Mulungu.

<sup>61</sup> Oh, zopambana bwanji! Iye tiyamba kulalikira pakapita nthawi ndipo osalowa mu phunziro ili.

Chabwino, tiyeni tiweramitse mitu yathu mphindi yokha kwa pemphero.

<sup>62</sup> Atate Akumwamba Achisomo, ife timakonda Mawu Anu Oyera mpaka mitima yathu imangotentha mkati mwathu, pamene ife tidziwa kuti Mzimu Wanu watsika pakati pathu, ndipo pamenepo kuyankhula ndi ife, ndipo mitima yathu nkufikirira ndi kuwugwira Iwo. Ndipo ife tikungowoneka kuti tikumverera bwino kwambiri pa Iwo, Ambuye.

<sup>63</sup> Ndipo kudziwa kuti mu ora lamdima ili momwe muli chisokonezo chochuluka . . . Monga mneneri ananena, “M'wasiku otsiriza kudzakhala njala,” chinachake cha dongosolo ili, “osati ya mkate ndi madzi, koma ya kumva kwa Mawu owona a Mulungu; ndipo anthu akanadzayenda

kuchokera kummawa kupita kumadzulo, kumpoto ndi kummwera, kufunafuna kuti apeze Mawu owona a Mulungu.” Mawu! Mawu ndi chiyani? Yesu ndiye Mawu, “Mawu anapangidwa thupi ndipo anakhala pakati pathu.” Kuwona mawonetseredwe a Mawu enieni a Mulungu akuwonetseredwa molingana ndi Malemba ndi kukwaniritsidwa, kuti, momwe anthu azidzayendera ndi kufunafuna ndipo azidzalephera kuwapeza Iwo. O Mulungu, ndife okondwa kwambiri, okondwa kuti tinamupeza Iye zaka zapitazo, wantengo wapatali ku mtima wathu, ndi kuona kuti ife sitiri osokonezeka mpang’ono pomwe.

<sup>64</sup> O Mulungu, Inu munati, “Iwo amene adzadziwa Mulungu wawo adzachita zoposa mu tsiku limenelo.” Ndipo pano ife tiri m’masiku otsiriza, powona zinthu zonse zimene Yesu ananena kuti zikanadzachitika, zikuwonetseredwa pakati pathu pomwe. Zizindikiro zomwezo, zodabwitsa, zozizwitsa zinachitidwa, kuchita izo basi momwe Iye ankachitira izo. Monga Iye anati, “Monga izo zinali mu masiku a Sodomu, kotero izo zidzakhala choncho pa kudza kwa Mwana wa munthu.”

<sup>65</sup> Ndipo, Ambuye, Inu mutilole ife, mwa Mzimu Woyera, kuti tifique mu Mawu amenewo ndi kutenga zinthu zenizenizo ndi kuzimangiriza izo mu Kalvare, mwa Mawu, ndi kuwona kuti mwa Iye ife tiri nacho chidzalo. Ndipo chuma ndi madalitso ndi ulemerero ndi zonse zipite kwa Iye Amene ali woyenera, amene anabwera kudzatenga Bukhu kuchokera mu dzanja lamanja la Iye amene anakhala pa Mpandowachifumu, ndi kukhala pansa pa Iwo Iyemwini, pakuti Iye anaphedwa kuyambira maziko a dziko lapansi.

<sup>66</sup> Ife tikuyankhula za Iye mmawa uno, Atate. Ife tikupemphera kuti Inu mudalitse mitima yathu. Lolani Mzimu Wake uyende pakati pathu ndi kutidalitsa ife, ndi kulemeretsa zotichitikira zathu, ndi kuchiza matenda pakati pathu, ndi kutipatsa ife chisomo chogonjetsa.

<sup>67</sup> Ndipo, Mulungu, pamene ine ndikupita kunja uko mmunda kukakumana ndi mdani, mulole ndizindikire kuti ndine wotetedwa ora lirilonse mwa pemphero. Oh, momwe ine ndimadalira chitetezero chimenecho, mdani akuyandikira, koma kudziwa kuti chitetezero chikugwira chifukwa amayi ndi abambo, ndi anyamata ndi atsikana, Akhristu, obadwanso mwatsopano okhala ndi chowachitikira, anthu opita Kumwamba ali pa mawondo awo akupemphera, “O Mulungu, perekani chiwombolo!” Ndipo, Atate, ife tikupemphera kuti Inu mutilole ife tipite m’malire a mdani kutali uko ndi kugonjetsa moyo uliwonse wantengo wapatali umene ukudikira. Chitani, Ambuye, ndi kuwatulutsa iwo mu mdima ndi kuwalowetsa mu Kuwala. Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amen.

<sup>68</sup> Tsopano, mu mutu wa 4 wa Bukhu la Chivumbulutso. Ife

tinamaliza mutu wa 3, ndipo tiyeni tikhale molemekeza ndipo ine ndiyesetsa kuti ndisakusungeni inu motalika kwambiri. Koma mu mutu wa 3 uwu, Mpingo unapita mmwamba monga choyimira, pamene Yohane anatengedwera mmwamba. Mpingo unakwera mmwamba, ndipo kuyambira nthawi imeneyo mpakana ukuchita ndi Israeli, mpaka Kudza kachiwiri. Kodi simukuwona momwe izo ziliri? Anthu lero, momwe iwo aliri, “Chinachake chachikulu chitha kugwedeza dziko lonse lapansi ndi chirichonse.” Zimenezo sizamalemba! Ayi, bwana. Chinthu chotsatira mu dongosolo ndi kupita kwa Mpingo. Werengani mu mibadwo ya mpingo, inu muona chimene . . .

<sup>69</sup> Tsopano, zinthu zina izi zomwe ziti zichitike, ndi nthawi ya Mwambo wa Ukwati pamene Mpingo uli mu Ulemerero. Mulungu akubwereranso ndi zodabwitsa zazikulu zoti achite, zozizwitsa zapadziko lonse ndi zinthu, ndi Ayuda, osapita ku Mpingo konse.

<sup>70</sup> Pa mutu wa 3 ukutsirizitsa m’badwo wa Mpingo. Uko nkulondola. Ndipo m’badwo wa Mpingo ukutuluka ndi apang’ono ochepa kwambiri omwe ife tikuwapeza . . . Ingomvetserani apa. Ine—ine ndinawerenganso izi mmawa uja, izo zinali pafupifupi kuding’amba ine mzidutswa, malo ndi machitidwe a Khristu pa mapeto a m’badwo wa Mpingo, zopezeka kuchokera ku ndime ya 20 mpaka ndime ya 22 ya Chivumbulutso 3. Taganizani za izo Khristu, pa mapeto, pamene Iye ali! Kodi Iye ali kuti pa mapeto a m’badwo wa Mpingo? Kunja kwa Mpingo Wake, atakankhidwira kunja ndi zipembezidwe ndi zikhulupiriro. Machitidwe Ake ndi otani? Kuyesera kuti abwerere mkati. Chimenecho ndi chikhaliidwe chomvetsa chisoni!

<sup>71</sup> Ndiye ife tikupeza apa, “zitatha zinthu izi,” iye anamva Liwu limene linali kuyankhula kwa iye kuti . . . Oh, chinali chiyani icho? Mzimu unachoka pa dziko lapansi. “Zitatha zinthu izi,” kuyambira mutu woyamba, kapena—kapena ndime 1:

*Zitatha izi ndinapenya, ndipo, tawonani, khomo  
linatsegulidwa kumwamba. . . .*

<sup>72</sup> Chivumbulutso 4:1, Mpingo utachoka, ndiye Chi—Chitseko chinatsegulidwa. Ndipo ife tadutsa mu zonse izo ndi kupeza kuti ameneyo anali Khristu, anali Khomo. Ndipo Liwu lomwelo limene linali kuyenda pakati pa zoyikapo nyali zisanu ndi ziwiri zagolide linalinso Liwu lomwelo limene iye analimva Kumwamba, likunena, “Kwera kuno.” Yohane anakwera mmwamba. Izo zinkayimira Mpingo kupita mu Mkwatulo.

<sup>73</sup> Yohane anakwera mmwamba mu Mzimu, anatengedwa kupita Kumwamba ndipo anawoneratu zinthu zonse zimene Mulungu analonjeza ndipo ananena kwa ophunzira, “Kuli chiyani kwa inu ngati iye adikira kufikira Ine nditabwera?” Iye

anawona kudza kwa Ambuye ndi zimene zikanati zidzachitike. Iye anawona pa dziko lapansi zomwe zikanadzachitika pa dziko lapansi mpaka Mkwatulo wa Mpingo, ndipo anatengedwera mmwamba ndi kuwonetsedwa mpaka mmusi mpaka kupitirira Zakachikwi. Oh, kodi izo sizopambana?

<sup>74</sup> Tsopano, ife tinamusiya iye Lamlungu latha pa mutu wa 4 ndi ndime ya 4.

*Ndipo pozungulira mpandowachifumuwo panali mipando foro ndi twente: ndipo pa mipandoyo ndinaona akulu foro ndi twente atakhala, atavala zovala zoyera; ndipo pa mitu pawo panali akorona agolide.*

<sup>75</sup> Tsopano, ife tinapeza kuti awa anali akulu. *Mkulu* samayimira konse Mngelo kapena Chinthu chirichonse. Ndi munthu wowombedwa, akulu! Chifukwa iwo... Mipandoyachifumu, akorona, ndi ulamuliro sizimatchulidwa konse kwa, kwa Angelo. Koma akorona ndi mipandoyachifumu, ndi zina zotero, zokhudza anthu. Ndipo akulu awa anavekedwa akorona ndipo anavekedwa zovala ndi kukhala pa mipandoyachifumu. Ndipo ife tinawapeza iwo ku mbali zina za Lemba kuti iwo anali atumwi thwelovu ndipo iwo anali mbadwa thwelovuzo. *Twente ndi foro* a iwo, zimene zikutanthauza “twente foro”: atumwi thwelovu, mbadwa thwelovu.

<sup>76</sup> Ndipo, ife tinapeza, ngakhale mzinda umene ukutsika kuchokera kwa Mulungu kuchokera Kumwamba... Dziko likatha kuphulika ndipo zonse zitakhala mzidutswa ndipo popanda chirichonse chotsala padziko lapansi koma phulusa la chiphalaphala (ndizo zonse zidzasiyidwe), sipadzakhalanso nyanja. Nyanja idzauma.

<sup>77</sup> Monga ine ndimayankhula usiku watha kwa winawake, kapena dzulo, kwina kwake, dziko lapansi kamodzi linayima monga *chonchi*, pompo, mozungulira dzuwa, kutentha kofanana njira yonse mmwamba ndi pansu. Kumwamba mu malo achipale a ku Britain, inu mukhoza kukumba pansu pamenepo mapazi faivi handiredi ndi kupeza kanjedza. Izo zinadza mwadzidzidzi, nkumuwumitsa iye ngati firiji tsopano. Monga *kuchepa madzi mthupi* lanu, ndi zina zotero, ndi *kuzizira* kwanu ndi kuzizira kwakuya komwe kumasunga nthudza ndi zinthu kwa zaka ndi zaka ndi zaka zikubwerazi. Mukuona? Ndi momwemonso momwe izo zinaliri mu nthawi imeneyo. Mwamsanga apo panadza chiwonongeko cha chigumula ndipo chinasefukira dziko lonse lapansi. Ndipo pamene izo zinatero, mphamvu za atomiki zinaligwedezeka ilo kuchoka mu njira yake, ndipo ilo linawuma ndipo apo ilo linali. Mukuona? Kumbani pansu ndipo inu mukhoza kuyipeza iyo, kumtunda kuzungulira madera akumtunda ndi zinthu, mitengo ya kanjedza ndi zina zotero.

Zimasonyeza kuti nthawi ina munkakhalamo anthu mokongola, yokhazikitsidwa. Koma tsopano lagwedezekanso.

<sup>78</sup> Tsopano, kumene ine ndikuganiza Mulungu anawatenga madzi amenewo, pamene Genesis ankayamba, Genesis 1, “Dziko lapansi linali lopanda maonekedwe, ndi lopanda kanthu, ndipo madzi anali pa kuya. Mzimu wa Mulungu unkayenda pamadzi ndipo unati, ‘Pakhale Kuwala.’” Mulungu kenako analekanitsa dziko lapansi ndi madzi, zimene zinapanga dziko lapansi. Koma dziko lonse lapansi linakutidwa. Tsopano, chimene Iye anachita, Iye basi... kudutsa mu milengalenga, Iye basi... mlengalenga ndi... Milengalenga ndiyodzazidwa ndi haidrojini ndi okosijeni, ndi zina zotero. Ndiye Iye anangoyinyamula iyo pa dziko lapansi ndi kuyilekanitsa iyo. Panalibe nyanja pa dziko lapansi panthawiyo. Mulungu ankathirira dziko lapansi, ngakhale mvula inali isanagwe. Iye ankathirira ilo kudzera mu akasupe ndi zinthu, ulimi wa mthirira. Ndiye pamene Iye... Chinthu chokhacho chimene Iye ankachita panthawiyo...

<sup>79</sup> Pamene munthu analitulutsa ilo mu njira yake, kupita ku mbali imodzi, chinachitika nchiyani? Izo zinaliponyera ilo mmbuyo mu... kutentha pansi *apa*, ndi kuzizira kumtunda *uko*. Ndipo kutentha ndi kuzizira, zimasonkhanitsa chiyani? Tikuzimvera izo kuno pa mazenera amenewo pakali pano, kutentha mkati muno ndi kuzizira kunjako. Mwaona thukutalo? Ndipo mvula si kanthu koma thukuta, chitungwi. Ndipo madzi ndi phulusa. Ndipo kotero ndiye pamene izo...

<sup>80</sup> Ine ndimayikonda nyimbo imeneyo:

Inu munaika dzanja Lanu, Ambuye wofunika,  
pa chidikha,  
Munaika dzanja lanu lodabwitsa pa mapiri;  
Ambuye, Inu munatsanulira kasupe,  
Munakweza phiri,  
O Ambuye, sungani dzanja Lanu la mtengo  
wapatali pa ine.

Inu munapanga mitambo, munapanga  
mitambo imene imapanga mvula,  
Kuchokera ku mvula anapanga nyanja,  
Kuchokera ku nyanja munabweretsa mitambo  
Kuti mutipatse ife moyo wochuluka;  
Inu mumagwira dziko lapansi ndi thambo mu  
ulamuliro Wanu, Ambuye,  
Oh, Chonde sungani dzanja Lanu lamtengo  
wapatali pa ine. (Oh, wamkulu bwanji! Inde,  
Mulungu wa Kumwamba.)

<sup>81</sup> Ndiye mu nthawi yayikulu iyi, ikutsamira mmbuyo monga *chonchi* tsopano, ndipo Iye anatipangira ife lonjezo, “Palibenso madzi, koma moto nthawi ino!” Mmalolo moliponya ilo... Iwo analiponyera dziko lapansi kutali ndi dzuwa, ndithudi, ilo



linazidwa. Ngati inu muliponya ilo padzuwa, lidzayaka. Ndipo monga momwe Iye analiwononga ilo ndi madzi ndi kuyika utawaleza m'mwamba, Iye "sadzachitanso izo konse," tsopano, Iye anapereka lonjezo loti Iye akanati "aliwotche ilo!" Kotero apo inu mumabwera pamene tchimo ndi kukongola konse ndi zonyansa zonse. . .

<sup>82</sup> Ndipo osati kale kwambiri ine ndinkakwera motsika chidikha. Ndiri mnyamata wamng'ono ine ndinkakonda kuganiza, kutenga mabuku anga a mbiriyakale ndi jogalafe ndi kumaganiza za zigwa zazikulu zakumadzulo. "Tsiku lina," Ine ndinati, "Ine ndidzakhala kumeneko mwamtendere komanso mwabata kumene kulibe tchimo, ndipo ine ndidzayendayenda m'minda ndipo ine ndidzasaka ngati Mmwenye. Ndipo ndidza—ndidzakhala kumeneko, moyo wamtendere, masiku onse a moyo wanga." Koma tsopano ndi. . . mzungu anapitako kumeneko. Kumene mzungu amapita, tchimo liri naye iye. Iye ndiye wakupha wamkulu ndi wakupha anthu onse padziko lapansi, ndi mzungu. Iye ndi wopanduka wamitundu yonse!

<sup>83</sup> Kuno osati kale kwambiri mu pepala (M'bale Thom pano, waku Africa), Ine ndinawona chidutswa mu pepala masabata awiri apitawo, ine ndikukhulupirira icho chinali, ndipo iye anati. . . iwo anati, "Ngati Achimerika akuloledwabe kupita ku Afrika, mu zaka teni kuchokera pano mkango waukulu wa ku Africa udzakhala utatha, njovu." Zigawenga zikuwombera paliponse pamene zingakhoze. Chithunzi cha amuna awiri akuluakulu akuyesera kunyamula mwamuna wovulala. Zimaoneka ngati misozi imatuluka mmaso mwawo. Iwo samafuna. . . yayimuna siyimafuna kuti yayikazi izifa. Ndipo aliyense atamugwira iye m'mbali mwake, monga *chonchi*, kumusunga iye kuti asagwere kwa iye. . . pansi. Unangowomberedwa mzidutswa. Munthu yemwe amawombera chirichonse monga choncho sakuyenera kukhala ndi mfuti mmanja mwake. Uko nkulondola. Mulibe mphamvu zokwanira kuti muyigwiritse ntchito iyo.

<sup>84</sup> Tsopano, zaka zingapo zapitazo, ndikuyesera kukusira gulu lina, la mbawala, kwa mzanga wabwino, M'bale Roy Roberson ndi iwo kumbuyo uko, pamene ine ndinali kuwalondolera uko mu Colorado; tinkadziwa kuti ife tinali ndi gulu lanyama labwino. Jeff ndi ine takhala tiri nazo kumeneko kwa zaka ndi zaka, pafupifupi eyite za mbawala mu gululo. Iwo amalola ena a anyamata akuofesi awa ochokera ku Denver kubwera kumeneko atavala mathalauza awa, ndi mwendo wa chilesi. Iwo ndi alenje. Hmm! Apa iwo anabwera uko, gulu, mu ma jeep ndi zinthu monga choncho, anabwerera mu malire athu kumeneko.

<sup>85</sup> Ndipo ine ndinali kuzikusira mbawala izi kuwoloka phiri kumbuyo kwawo, pafupifupi mailo kapena awiri, ndipo izo zinali kuyenda motsatira. Inu mumayenera kuzichepetsa izo, atonde aakulu akale ndi zinthu; ngati simutero, inu muwononga

khola lanu. Izo ziri ngati kuweta ng'ombe kapena chirichonse. Nyama zakuthengo zikhaleenso chimodzimidzi kwa ife. Si chandamale. Ngati inu mukufuna kuwombera chandamale iwo ali ndi malo oti aziwomberepo izo pamenepo. Uko nkulondola. Ndi chamanyazi kupha zinthu ngati zimenezo. Ndi uchimo, si zaumulungu!

<sup>86</sup> Ndipo ine ndinawerenga kuwombera handiredi ndi twente firii kuchokera mu mfuti zamakina, monga, kuwombera izo kuchokera pa mapewa awo. Ndipo mmawa wotsatira, M'bale Banks Wood pano ndi ine, tinakwera pamwamba pa phiri, ine ndinawerenga mabedi naintini amagazi. Samadziwa kanthu za kusaka; inu mukhoza kuwombera chinyama chachikulu monga choncho, inu mukhoza kuchimenya mokuya kwambiri kuti muchiphe icho. Ndipo iwo anangoyisiya, “phaa, phaa, phaa,” kuwombera imodzi kenako inzake. Bwanji, izo zifa. Ndipo nchiyani chiti . . . Pamene malungo ayamba mwa izo, ngati inu mutazipeza kuti si zabwino, iwo amaziwononga nthawi yomweyo; ndipo zosakaza, nkhandwe ndi zinthu, zimazidya izo. Mabedi naintini a magazi, atonde aakulu, ziboda zazikulu *choncho* kuzungulira, ndipo magazi akutuluka mapazi awiri pamene iyo inaboledwa monga choncho ndi mfuti izo. Iwo sayenera kumulola wopanduka ngati ameneyo kukhala ndi mfuti mmanja mwake. Uko nkulondola. Iye alibe mphamvu yogwira mfuti. Oh, ndi wopambana, uchimo kuchita monga choncho.

<sup>87</sup> Ndi zowopsa, koma ndiye Wachimerika. Canada, anthu ofunika inu ochokera ku Canada! Ngati Amerika ipitirirabe, Canada ikhala yotsika ngati Amerika, pakapita kanthawi. Yendani kuzungulira malire a Canada kulikonse, ndipo muli ndi chikhaliwe cha Chimereka chimenecho. Amerika uyu ndi hule la mafuko. Ndizo ndendende zomwe iye ali, ndipo akhala oyipitsitsa kuposa kale lonse tsopano. Iye akufika ku mapeto ake! Baibulo limayankhula za chiwonongeko chake, limafotokoza momwe iye ati adzakhaliwe. Amerika: wotsika pansu, wowola, wanyansi, palibe chabwino. Ndizo ndendende kulondola. Iye wakhala fuko lalikulu. Iye wanyamula Uthenga. Nchiyani chimamupangitsa iye kukhala momwe iye aliri? Chifukwa iye waukana Uthenga, ndipo wakana Zoonadi. Iye ndi woopsa. Iye zikumubwerera, musadandaule. Ine ndinaziwona izo mu masomphenya monga PAKUTI ATERO AMBUYE! Zikubwera. Iye adzalipira chifukwa cha tchimo lake.

<sup>88</sup> Kale pamene Amerika anali Amerika, iye anali fuko lopambana. Lopambana lomwe dziko lapansi linayamba ladziwapo kuyambira Israeli, linali Amerika, koma iye ndithudi wadziyipitsa yekha tsopano. Iye wawukana Uthenga. Iye sanatenge kalikonse koma basi . . . Tsopano iye wadziyeza yekha . . . Inu mukhoza kuwona pomwe iye ali tsopano. Aliyense akudziwa zimenezo, mu chisankho chapitachi chikusonyeza

kumene mayimidwe ake auzimu ali. Uh-huh. Iye sakudziwa.

<sup>89</sup> Tsopano, akulu awa atakhala pa mpandowachifumu ndi korona wake. Tsopano, ndime ya 5, ife tiyamba:

*Ndipo kuchokera pa mpandowachifumuwo kunatuluka mphezi...mabingu...malivu: ndipo apo panali nyali seveni pa moto zikuyaka patsogolo pa mpandowachifumu, imene ili Mizimu seveni ya Mulungu.*

<sup>90</sup> Oh, ine ndikuzikonda izi! Sichoncho inu? Oh, ine ndikungomverera ngati chikhotho changa chikundikwanira ine, inu mukudziwa. Ine basi...pamene...Oh, ine ndikutanthauza mu chikhotho chazimu, ndithudi, inu mukudziwa. Chabwino.

<sup>91</sup> “Kuchokera ku Mpandowachifumu.” Tiyeni tiyankhule za Mpandowachifumu umenewu tsopano kwa maminiti pang’ono. Uwu siunali Mpando wachifundo. Mpandowachifumu wa Chifundo watha; palibenso chifundo, ndi popanda chifundo. Ife tikuyenda bwanji...Momwe mpando wachiweruzo udzakhala mpando wachiweruzo wa Khristu, mpando wachiweruzo, Chiweruzo cha Mpando Wachifumu Woyera? Kodi padzakhala chifundo panthawiyi? Palibe gawo limodzi lachifundo lomwe lidzaperekedwe. Pa Mpandowachifumu wachiweruzo inu mukhoza kufuula “chifundo” mpaka inu simungathenso kufuula, ndipo ndi, inu mukhoza kungofuulira mu mlengalenga kwinaakwake, chifukwa kulibenso chifundo.

<sup>92</sup> *Tsopano* ndi tsiku la chifundo! Tsopano, tiyeni tibwerere mmbuyo mu Chipangano Chakale apa pang’ono pokha ndi kupeza chomwe chifundo chiri. Tibwerere mmbuyo ndi kuona zomwe zinachitika ku Mpandowachifumu uwu. Mpandowachifumu uwu, ndithudi, ndiwo—mpando wachiweruzo. Ndipo kukhala...chifukwa chimene lero kuti pali chifundo, ndi chifukwa chakuti mpando wachifundo wawazidwa ndi chitetzero. Magazi! Ndipo bola ngati Magazi akadali pa mpando wachiweruzo ndiye si chiweruzo panonso, ndi chifundo, chifukwa Chinachake chinafa kuti chiyimitse chiweruzo. Ngati inu mukuchiona icho, nenani “Ameni.” [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] Bola ngati Magazi akadali pa mpando wachifundo, zinkasonyeza kuti Chinachake chinafa kuti chiyimitse chiweruzo. Koma pamene Mpingo ukwatulidwa, mpando wachifundo umasandulika mpando wachiweruzo!

<sup>93</sup> Uko, inu mukudziwa, mu Chipangano Chatsopano kunonso, “Ndi malo opatulika.” Ndiko kumene—oweruza...mu malo opatulika, woweruza ali pa mpando mu malo opatulika. Tsopano, mpando wachiweruzo uwo mu malo opatulika anakhala odzaza ndi utsi. Chinali chiyani icho? Monga Phiri la Sinai, chiweruzo! Chifundo chinali chitachoka pa—pa

Mpandowachifumu wa Mulungu. Mulungu adzaweruza dziko lapansi popanda chifundo. Ndi angati akudziwa zimenezo?

<sup>94</sup> Chinthu chimodzi chokha chimene Iye ati adzachizindikire mu tsiku limenelo, ndi chiyani Icho? Magazi. Ndi chinthu chokhacho chimene chinakondweretsa Mulungu wokwiya.

<sup>95</sup> Adamu ndi Eva anapanga thewera labwino basi monga wa Methodisti, Baptisti, Presbateria, kapena Wachipentekoste aliyense akanakhoza kupanga, ilo linkaphimba umaliseche wawo. Koma Mulungu amakhoza kuwona kudutsa mu ilo, kotero Iye anapha chinachake ndipo anatenga zikopa zakufa za—zikopa za nyama yakufayo ndi kuphimba iwo. Magazi anayenera kutenga malo ake. Izo zinayimitsa mkwiyo Wake, Iye anawona magazi ndipo anachoka kwa iwo, chifukwa chinachake chinali chitataya moyo wake. O Mulungu!

<sup>96</sup> Taganizani za izo! Chinthu chokhacho chimene chingamubweze Mulungu ndi Magazi. Ndipo pali Magazi amodzi okha omwe Iye ati abwerereko, ndipo ndiwo a Mwana Wake Yemwe. Pamene Iye awona kuti awo ndi Magazi a Mwana Wake Yemwe, Iye adzabwerera m'mbuyo. Chifukwa ndiyo mphatso yomwe ili. . . Mulungu anapereka kwa Mwana Wake, kuti awombole iwo amene Iye anawadziwiratu, ndipo izo zimamubweza Mulungu ku chiweruzo Chake. Koma pamene Magazi amenewo achotsedwa, ndipo onse omwe anadziwidwiratu ayitanidwa kulowa mu Thupi lofunikalo, Mpingo Wake wakonzekeretsedwa ndipo watengedwera mmwamba, ndiye mkwiyo wa Mulungu uli pa anthu.

<sup>97</sup> Oh, m'bale, musamafune konse kuyima pamenepo! Ndiloleni ine ndiime patsogolo pa mfuti ya makina, ndiloleni ine ndidulidwe mzidutswa, ndiloleni ine ndichekedwe inchi ndi inchi, mulole chirichonse chichitike (monga lumbiro la Knights of Columbus), aloleni atsegule mimba yanga, ndi kutentha sulufure ndi zonse ziri mwa ine, ndi manja anga ndi miyendo yanga idulidwe, chirichonse chomwe chingakhale, koma musandilole *konse* ine ndiyime pa Chiweruzo cha Mpandowachifumu Woyera uwo pamaso pa Mulungu.

<sup>98</sup> Oh, ndiloleni ine nditenge mpandowachifumu wawung'ono uwu *pano* pamaso pa mpando wa Khristu ndi kuvomereza Magazi Ake. Palibe kalikonse mmanja mwanga kamene ndikubweretsa, Ambuye.

Palibe kasupe wina yemwe ndikumudziwa,  
Palibe koma Magazi a Yesu. (Ndizo zonse  
zomwe ndikuzidziwa.)

Ichi ndi chiyembekezo changa chonse ndi  
kukhala,

Palibe china koma Magazi a Yesu.

<sup>99</sup> Nzosadabwitsa Eddie Perronet. . . anasiyidwa pa nyimbo zake. Pamene iye anali Mkristu, Mkristu wokhazikika,

iwo sanafune kugula nyimbo zake. Tsiku lina iye anati, “Ine ndidzalemba imodzi, ndipo tsiku lina...imene iwo adzalandira.” (Ndipo anthu anali kufuna chinachake chamakono kwambiri mu nyimbo zachipembedzo.) Tsiku lina kumeneko Mzimu Woyera unagwira, ndipo iye anatenga cholemberacho ndipo analemba:

Nonse yamikani mphamvu ya Dzina la Yesu!  
 Lolani Angelo agwe modzilambatitsa;  
 Bweretsanipo nduwira yachifumu,  
 Ndi kumuveka korona Iye Mbuye wa ambuye.  
 Pakuti pa Khristu, Thanthwe lolimba, ine  
 ndaima;  
 Maziko ena onse ndi mchenga wotitimira,  
 Maziko ena onse ndi mchenga wotitimira.

<sup>100</sup> Kaya ndi mpingo, kaya ndi bwenzi, kaya ndi mdani, kaya ndi fuko, kaya ndi chuma, kaya ndi umphawi, kaya ndi chabwino, kapena chirichonse chimene chiri, maziko ena onse ndi mchenga wotitimira! Ndi chinthu chokhacho, pamapeto pake chidzachoka. Koma:

... Khristu, Thanthwe lolimbalo, ine ndayima;  
 Maziko ena onse ndi mchenga wotitimira.  
 (Kumbukirani zimenezo.)

<sup>101</sup> Zindikirani! Tiyeni tipite ku Levitiko 16, ndipo tiwerenge kuseri, kumbuyo komwe kuseri kwa Baibulo tsopano, mu malamulo Achilevi, ndi kuwona apa wa Levitiko—Levitiko mutu wa 16. Ndipo kuyambira ndi ndime ya 14 ya mutu wa 16. Oh, ine—ine ndimakonda kutenga nthawi yanga pa zinthu izi, kuzitulutsa izo kunja. Levitiko fo-... kapena Levitiko 16:14.

*Ndipo iye adzatengako magazi a ng’ombe yamphongoyo, ndi kuwaza ndi chala chake pa mpando wachifundo* (Pa mpando wachifundo! Penyani, ife tilowa mu izi pakapita kanthawi)... *chakummawa*;...

<sup>102</sup> Musaiwale mawu amenewo “Kummawa”! Kodi Yesu akuchokera kuti? Kummawa, mu mtambo wa Ulemerero. Kodi d-z-u-w-a limatulukira kuti? Kummawa. Kodi M-w-a-n-a adzawuka kuchokera kuti? Kummawa. Kodi mpando wachifundo unali pati? Chakummawa. Chifukwa chiyani ine ndakukhazikani inu nonse *chonchi* cha kummawa? Chifukwa chiyani? Guwalo liri kummawa. Ife tizona izo pakapita kanthawi, mokongola bwanji, ine ndizijambula izo. Ine ndinapempha ochuluka momwe ine ndikanathera kuti abweretse mapepala ndi zina zotero, kuti nditenge mapu awa mu maminiti pang’ono. Chabwino:

... *kuwaza iwo...chakummawa; ndi pamaso pa mpando wachifundo iye awaza...magazi ndi chala chake ka seveni.*

103 Oh, kodi izo si zokongola? “Ka seveni kulowera kummawa.” Ndi chiyani icho? Mibadwo Isanu ndi iwiri ya Mpingo idzaphimbidwa ndi Magazi. Aleluya! Magazi a Yesu Khristu okwanira basi mmenemo, dzulo, lero, ndi kwanthawizonse, ndi kwa m’badwo uliwonse, kupulumutsa wochimwa aliyense, kuchiritsa munthu wodwala aliyense, kubweretsa chozizwitsa chirichonse, chizindikiro chirichonse kuti chichitike. “Ka seveni,” kutali komwe mu Chipangano Chakale, zaka fortini handiredi ndi nainte Khristu asanabwere. Taganizani za izo! Chizindikiro, “ka seveni zidzatero . . .”

*Ndiye iye adzapha mbuziyo . . . nsembe ya tchimo, ndiyo ya kwa anthu, ndipo adzabweretsa magazi ake pamodzi ndi . . . mu chotchinga, kuti chichite ndi magazi amenewo monga iye anachitira ndi magazi a ng’ombe yamphongo, . . . kuwawaza iwo pa mpando wachifundo, ndi pamaso pa mpando wachifundo:*

*Ndipo iye adzapanga chitetezero cha malo opatulikawo, chifukwa . . . a . . . cha kudetsedwa kwa ana a Israyeli, ndi chifukwa cha zolakwa zawo mu machimo awo onse: ndipo iye adzateronso ku kachisi wa osonkhana, amene atsala mwa iwo amene ali pakati pa—pa kudetsedwa kwawo.*

104 Chinali chiyani icho? “Mpando wachifundo.” Ali kuti tsopano? Ndipo mkati mwa likasa munali chiyani? Chilamulo. Ndipo chilamulo, kuphwanya lamulo limodzi kunali kufa popanda chifundo. Koma pokhala kuti inu mukanakhoza kukhala ndi chifundo, magazi ankayenera kukhala pa guwa. Iwo ankawaza mpando wachifundo. Ndipo mpando wachifundo ndi guwa limene inu mumagwada ndi kupempha chifundo. Mulungu aletse kuti ife tilichotse konse ilo ku mipingo yathu, guwa lachikale lomwe anthu angakhoze kugwada ndi kuyitanira pa Mulungu kuti awachitire chifundo. Ndipo chifundo ndi cholemera, ndipo chikuyenderera mwaufulu kuchokera ku Magazi a Ambuye Yesu. Tsopano, aponso, ndicho chifundo. Ndiwo mpando wachifundo.

105 Koma inu mukuzindikira mkati umu, iwo siunali mpando wachifundo, pakuti umu munali “mphezi ndi mabingu ndi maliwu.” Palibe mphezi ndi mabingu pa chifundo. Ndicho chiweruzo.

106 Tiyeni titembuzire ku Eksodo, mutu 19 wa Eksodo ndi ndime ya 16. Eksodo, mutu 19 wa Eksodo, ndipo tiyeni tiyambire ndi ndime ya 16:

*Ndipo zinachitika . . .*

Mvetserani chimene . . . pamene Mulungu anakwera pa Phiri la Sinai:

*Ndipo zinachitika pa tsiku lachitatu m’mawa, kuti kunali mabingu . . . mphezi, ndi mtambo wokhuthala pa*

phiripo, *ndipo liwu la lipenga lokweza kwambiri*; (Kodi liwu la lipenga ndi chiyani? Ndi mngelo wamkulu.) *kotero kuti anthu onse... (Mvetserani!)... anthu onse... anali mu msasa ananjenjemera.*

107 “Chiweruzo!” Fyuu! Iwo anali ataguba kunja uko ndipo Mulungu anali atawapatsa iwo chisomo choti azidutsapo, koma iwo anali atafuna lamulo. Iwo... Mulungu ankafuna kuti iwo akhale azipembedzo zosiyanasiyana; iwo ankafuna kuti apange chipembedzo pa icho, chinachake chimene iwo angatsutsane nacho, mmalo mongotsatira Mulungu ndi kukhala pansu pa ulamuliro Wake, pansu pa mphamvu Yake. Chisomo chinali chitapereka mneneri, chisomo chinali chitapereka chitetezero (mwanawankhosa), chisomo chinali chitapereka zinthu zonse izi, ndipo komabe iwo ankafuna chiweruzo. Iwo ankafuna chinachake chimene iwo akanachita.

108 Mulungu anati, “Asonkhanitse iwo pamodzi, Ine ndiwadziwitsa iwo chomwe chiri. Ine ndiwawonetsa iwo chomwe chiri.” Werengani! Mvetserani! Ndipo liwu la lipengalo linakulira ndi kukulirabe mpaka linagwedeza nthaka. Inu mukuona chomwe chiweruzo chiri. Ine sindikufuna zimenezo. Ndipatseni ine chifundo!

109 [M’bale Fred akuti, “M’bale Branham?—Mkonzi.] Ndipo... [M’bale Branham?”] Inde? [“Chimenecho chinali chiyani—Lemba lotsiriza lija munaliwerenga?”] Ameneyo anali Eksodo, mu—mu—mutu wa 19 ndi ndime ya 16, M’bale Fred. Eksodo 19:16.

110 Tsopano, zindikirani ndime ya 17:

*Ndipo Mose anawatulutsa anthu kunja kwa msasa kuti akakumane naye... Mulungu;* (Oh, mai! Ine ndikufuna kuti ndidzakumane naye Iye mu mtendere, osati monga choncho.) *ndipo iwo anaima pansu pa phiri.* (Kutali kumbuyo.)

111 Kumbukirani, phiri limenelo linali ndi mizere itajambulidwa mozungulira ilo. Ngakhale ngati ng’ombe itakhudza phiri limenelo, iyo inkayenera kuti ifere pomwepo, siingabwere mu Kukhalapo kwa Mulungu. Ndipo Mulungu... “Ndipo Mose anawabweretsa anthuwo.”

112 Tsopano, ndime ya 18, ndime yotsatira:

*Ndipo phiri la Sinai linakhala lonse... mu utsi, chifukwa AMBUYE anatsikira pa ilo mu moto:... (Likungofuka ndi kuyaka ngati ng’ango.)*

113 Kodi Iye anatsitsa chiyani? Osati mu Ulemerero Wake wa Shekinah, koma mu mkwiyo wa ziweruzo Zake.

*... ndipo utsi wake unakwera ngati utsi wa ng’ango, ndi phiri lonse linagwedezeka kwambiri.* (M’bale, ine sindikufuna kuti ndikakhale kumeneko!)

*Ndipo pamene liwu la lipenga linkawomba motalika, ndi kumakulira ndi kukulirabe, Mose anayankhula, ndipo Mulungu anamuyankha iye ndi liwu. (Mose anayankhula; osati anthuwo, iwo anali kugwedezeke mpaka ku zidutswa.)*

*Ndipo a—ndipo AMBUYE anatsikira pa phiri la Sinai, pamwamba pa phiri: ndipo AMBUYE anamuyitanira Mose mpaka pamwamba pa phiri; ndipo Mose anakwera.*

*Ndipo AMBUYE anati kwa Mose, Tsika pansi, ndipo uwalamulire anthu, kuchitira kuti iwo angabowoleze mpaka kwa AMBUYE kuti amuone, ndi ambiri a iwo nkuwonongeka.*

<sup>114</sup> [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.] Anthu amakhala kumbuyo kwa tchalitchi ndi kumaseka winawake akuyankhula ndi malirime, kapena kuvina mu Mzimu; anapita, anachitira mwano Mzimu Woyera, anasindikizidwa kwanthawizonse! “Aliyense amene anganene mawu motsutsa Mzimu Woyera sadzakhululukidwa m’dziko lino, ngakhale m’dziko liri nkudzalo.” Musayang’ane pa Iwo! Khalani kutali ndi Iwo kapena mwina muulandire Iwo!

<sup>115</sup> Ife kulibwino tilisiye Lemba limenelo. Werengani izo mopitiriza, zonse za izo, muwone zomwe Mulungu ananena. Ndipo anthu anati, “Oh, Mose, iwe yankhula. Usalole kuti Mulungu ayankhulenso! Ife tikukhumba tsopano tikanapanda kupempha izi.” Mukuona? “Tikulola iwe uziyankhula kwa ife, Mose. Mulungu akayankhula, ife tonse tifa.” Mwaona, Mulungu anali atapanga chitetezero.

<sup>116</sup> Tsopano, “Liwu la Mpandowachifumu.” Zindikirani mu Mpandowachifumu uwu, “patsogolo pa Mpandowachifumu panali nyenyezi seveni,” Liwu la nyenyezi. “Maliwu,” inu mukuona. Munali zinanso mu Chivumbulutso 4 apa, kapena 5, ife tikupeza, “Ndipo kuchokera mu Mpandowachifumu munatuluka mphezi, mabingu, ndi maliwu.” Osati liwu *limodzi*; “maliwu,” ambiri. Chinali chiyani icho? Mulungu akuyankhula kwa Mpingo, akudzinyezimiritsa Yekha kudzera mu Mizimu seveni. Pamene wodzozedwa woona wa Mulungu ayankhula, ndi Liwu la Mulungu! Kulikana Ilo ndi kuchotsa choyikapo nyali. Mukuona? “Maliwu,” Liwu la Mibadwo Isanu ndi iwiri ya Mpingo (cha apa pa ngodya), maliwu akuyankhula ndi bingu ndi mphezi.

<sup>117</sup> Masiku ano ziri choncho, “Chabwino, ife sitimakhulupirira mu kunena ‘gehena’ pa guwa.” Oh, chifundo! Kotero mwakuti! Hmm! Ife tikufuna amuna a Mulungu, amuna amene sangaleke!

<sup>118</sup> Tsopano, aliyense sangakhale mlaliki, koma inu muli ndi liwu. Ndipo ngati inu simungakhoze kuwalalikira anthu ulaliki. . . Ngati ndinu mlaliki, inu munayitanidwa ku guwa kuti mukalalikire. Ngati inu simuli, inu ndinube mlaliki,



koma *muzikhala moyo* ulaliki kwa anthu. Lolani ulaliki wanu *ukhalidwe moyo*, ndipo ndi Liwu la Mulungu limene liti lidzabweretse chitonzo kwa iwo amene alikana Ilo. Iwo amati, “Palibe amene angaloze chala pa moyo wake. Iwo ndi okoma, amoyo...Iwo...Ngati panayamba pakhala munthu wa Mulungu, ndi mwamuna uyo kapena mkazi uyo.” Mwaona, zikhalani moyo maulaliki anu. Musayesere kuwalalikira iwo ngati inu simunayitanidwe kuti mukhale mlaliki; inu mumazisokoneza, mulimonse, ndi kusokonezeka, ndipo inu mumasokoneza anthu, ndipo inu simudziwa... Chabwino, inu— inu mudzawawononga iwo ndi inueni, nanunso. Ingokhalani moyo ulaliki wanu!

<sup>119</sup> Mlaliki amayitanidwa kuti azilalikira wake, ndi kukhala moyo wa iwonso. Ngati inu simungakhoze kukhala moyo Iwo, ndiye inu musiye kuwulalikira Iwo. Koma inu mukuyenera kuti muzikhala moyo maulaliki anu.

<sup>120</sup> Chabwino, apa panali “maliwu.” Oh, momwe ife tikufunira mu Jeffersonville masauzande a maliwu okhalidwa moyo, bingu la Mulungu likubangula mu kukoma ndi chiyero, ungwiro, miyoyo yosadetsedwa, akuyenda kuzungulira padziko lero, opanda chilema. Inde, bwana, Akhristu enieni, ndilo bingu motsutsa mdaniyo. Mdierekezi samasamala mochuluka bwanji momwe inu mungafuwulire; mdierekezi samasamala kuchuluka kwa momwe mungalumhire kapena kuchuluka kwa momwe mungachitire *izi* kapena kufuula. Koma chimene chimamupweteka mdierekezi ndi kuwona woyeretsedwa, moyo woyera woperekedwa kwa Mulungu; nenani chirichonse kwa iye, kumutcha iye chirichonse, mokoma basi monga izo zingakhoze kukhalira ndi kumapitirirabe nazo. Oh, mai! Izo zimamutayira iye kutali, ndilo bingu limene limamugwedeza mdierekezi.

<sup>121</sup> Basi monga, “Chabwino,” inu mukuti, “ngati iye akanakhoza kulalikira monga Billy Graham kapena Oral Roberts, kapena winawake, woyankhula wachikoka wamkulu, iye akanakhala...” Oh, ayi! Nthawi zina mdierekezi amangoseka pa zimenezo. Iye samasamala mochuluka za izo kuposa kalikonse. Inu mumapeza fiyoloje yonse—fiyoloje yomwe inu mumafuna ndi maphunziro onse a seminare, ndipo mdierekezi amangokhala kumbuyo ndi kuseka pa izo. Koma pamene iye awona Moyo umenewo!

<sup>122</sup> Tayang’anani pa ophunzira amenewo kumusi uko, mwana wamisala uja tsiku lija ali ndi khunyu, akuti, “Tuluka mwa iye, mdierekezi! Tuluka mwa iye, mdierekezi! Tuluka mwa iye, mdierekezi!”

<sup>123</sup> Mdierekezi atakhala pamenepo, anati, “Tsopano, kodi inu simukudzichitira manyazi kwambiri inueni? Tsopano, inu mukuona zomwe inu mukuchita? Yesu anakuuzani inu, Iye

anakulamulirani inu, kuti mupite mundithamangitse ine. Palibe mmodzi wa inu angakhoze kuchita izo.”

<sup>124</sup> Koma, m’bale, pamene iwo anamuona Iye akubwera, Wina akubwera akuyenda mwakachetechete. Uh-huh. Oh, mai! Iye sanayenera kunena kanthu. Mdierekezi ameneyo anali atachita kale mantha nthawi yomweyo. Iye anadziwa kuti iye ankayenera kuti achoke, kulondola, chifukwa apo panadza Moyo; osati ulaliki wokha, koma Moyo. Anati, “Tulukani mwa iye.” Oh, mai! Izo zachita zimenezo! Mwakachetechete; Iye ankadziwa chimene Iye anali kuchiyankhula, Iye ankadziwa chimene Iye anali kuchita.

<sup>125</sup> Tsopano, “Maliwu,” maliwu a malipenga seveni, anali maliwu a nyenyezi seveni, amithenga seveni. Koma tsopano yang’anani apa:

. . . *ndi . . . nyali*                      *seveni . . . pamaso*                      *pa*  
*mpandowachifumu, imene ili Mizimu seveni ya*  
*Mulungu.*

<sup>126</sup> “Nyali seveni.” Tiyeni tijambule pang’ono pokha apa, Mpandowachifumu, malo overa, osonkhana. Ndipo pomwe *pano* panali (wani, thuu, firii, foro, faivi, sikisi, seveni) nyenyezi seveni, nyali seveni, atumiki seveni, Mizimu seveni; osati zonse kutanthauza kuti Mulungu ali mu Mizimu seveni, koma “mawonetseredwe seveni a Mzimu Woyera womwewo.”

<sup>127</sup> Mzimu Woyera uli kuti? Pano pa Mpandowachifumu, ukuwalira mu m’badwo wa mpingo uliwonse. M’badwo wa mpingo *uwu* ukunyezimiritsa mmbuyo mwanjira *iyi*, maliwu a Mulungu, Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi nthawizonse. Mwaona, seveni, analipo “maliwu.” “ndi nyali seveni zoyaka moto,” Mizimu seveni, “yomwe ili Mizimu seveni ya Mulungu.”

<sup>128</sup> Mukukumbukira ma Lamlungu angapo apitawo ife tinafika kwa izo, diamondi yaikulu? Koma amadulidwa mnjira zosiyanasiyana kuti anyezimiritse moto ndi magetsi kuchokera pamenepo. Ndiyo njirayo, “Yesu Khristu ndi chiyambi cha chirengedwe cha Mulungu,” Chivumbulutso 1. Ndi kulondola uko? Ndiye kodi Mulungu analengedwa liti? Iye ndi chiyambi cha chirengedwe cha Mulungu. Ndipo Mulungu ndi Wamuyaya. Ndi kulondola uko? Koma pamene Mulungu analengedwa . . . pamene khanda laling’ono limene linayembekezedwa m’mimba ya mayi, namwali. Ndipo iye anayamba kupanga makhungu amenewa mkati mwake kuti abale khanda laling’ono ili, chimenecho chinali chiyambi cha chirengedwe cha Mulungu, “Pakuti Mulungu anapangidwa thupi ndipo anakhala pakati pathu, nakhala *Emanueli*, ‘Mulungu nafe,’ chiyambi cha chirengedwe cha Mulungu.”

<sup>129</sup> Ndiye mu Ngale yaikulu iyo imene inachokera ku dothi . . . chifukwa Iye anapangidwa ndi dothi. Ndi kulondola uko? Iye amadya chakudya monga ine ndimachitira, Iye amadya

chakudya monga inu mumachitira. Chimene, dothi la thupi, Iye anakhala kashiamu, potashi, petroleamu, kuwala kwa kozimiki, koma mwa Iye munakhala Kuwala Kwamuyaya. Nzosadabwitsa anzeruwo anati kwa Nyenyeziyo, “Tilondolereni ife ku Kuwala kwanu kwangwiro.”

<sup>130</sup> Iwo anali kungonyezimiritsa Kuwala kwa Kuwala Kumodzi kwangwiro. Ndipo apo Iye anali, Kuwala kwangwiro kwa Mulungu, chiyambi cha chirengedwe cha Mulungu. Tsopano, mmenemo munali Iye. . .

<sup>131</sup> Kodi Iye anakhoza bwanji kudzinyezimiritsa Yekha m'mbuyo ku nyenyezi Zake za dziko lapansi, anzeru aja atamuwona Iye Kumwamba, ndipo iwo anakhala mizimu yotumikira pano pa dziko lapansi? “Iye anavulazidwa (Daimondi wamkulu, wodulidwa) chifukwa cha zolakwa zathu, anatunduzidwa chifukwa cha kusaeruzika kwathu, chilango cha mtendere wathu chiri pa Iye, ndi mikwingwirima Yake ife tinachiritsidwa.” Kodi Iye anali kuchita chiyani? Kunyezimiritsa!

<sup>132</sup> Munthu aliyense amene amadzinenera kuti ndi wantchito wa Mulungu, yemwe amakana machiritso Auzimu ndi mphamvu Yake, samapeza kuwala kwake kuchokera kwa Daimondi ameneyo, samatenga kuwala kwake kuchokera ku Mpandowachifumu umenewo. Chifukwa Iko kumanyezimiritsa Iye yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse kudzera mwa nyenyezi seveni ndi Mibadwo Isanu ndi iwiri ya Mpingo.

<sup>133</sup> Oh, mayamiko akhale kwa Mulungu! Ndikuganiza nkoyenera kwa mtumiki kupembedza Mulungu pa guwa, ndi kuperekamathokozo ndi matamando ndi ulemu ndi mphamvu. Oh, zenizeni bwanji, momwe izo zimangosangalatsira moyo wanga mpaka ine ndimamverera ngati ndingakhoze kufuula, ndi kuthamanga ndi kulumphira m'mwamba momwe ine ndingakhoze kulumphira, chifukwa pali Chinachake mwa ine chimene chandisinthia ine kuchokera ku chimene ine ndinali. Ine sindiri chimene ndikuyenera kuti ndikhale, ndipo osati chimene ine ndikufuna kuti ndikhale, koma ndikudziwa ine ndasinthidwa kuchokera ku chimene ine ndinali. Chinachake chachitika, chinachake chachitika!

<sup>134</sup> Ndipo imani apa ndi kuwona Mawu Amuyaya awa omwe akugwedeza mkuntho uliwonse! Pamene iwo ankayesera kuwotcha Mabaibulo ndi chirichonse, Iwo anagwedezeka mopitirira chimodzimidzi basi, chifukwa Iwo anati, “Miyamba ndi dziko lapansi zidzapita, koma Mawu Anga sadzapita.”

<sup>135</sup> Kumtunda kuno pafupi ndi Chicago tsopano, ndipo a—Baibulo liri pa guwa la mpingo. Kale kwambiri Nkhondo Yoyamba Yapadziko Lonse isanachitike, mmishonare anali nayo ndipo munthu wina anatembenezidwa, ndipo iye ankafuna kuti amupatse mmishonare Baibulo lake, anati, “Ine

sindingakupatseni ili, amayi anga anandipatsa ine limeneri.” Anati, “Ine, ndikafika kunyumba, ndikutumizirani limodzi.”

<sup>136</sup> Iye anayamba kubwerera kuwoloka nyanja ndipo sitima yapansi pamadzi yaku Germany inaphulitsa nga—ngalawayo. Iwo sanapeze konse chidutswa cha iyo. Ndipo zaka ziwiri patsogolo pake, kutali komwe ku gombe, iwo anawona bokosi likuyandama. Ena a iwo ankaganiza kuti icho chikanakhala chinachake chomwe chinamira, ndipo kotero iwo anatulutsa bokosilo ndi kulitsegula ilo, anthu awiri akuyenda nalo. Ndipo mmenemo, chinthu chokha chimene chinapulumuka icho, mmuni Baibulo lija limene iye ankalityumiza kubwerera kwa mmishonareyo. Ilo liri pa guwa kuno pafupi ndi Chicago lero, mu mpingo wa Methodisti. “Miyamba ndi dziko lapansi zidzapita, koma Mawu Anga sadzapita.”

<sup>137</sup> Pa nthawi ya chigumula kuno, mu 1937, tchalitchi chaching’ono chakale ichi, pamene pansu pa matope ndi zina zotero zomwe zinali mmenemo, ife tinkakhoza kukwera pamwamba pake apa mu a—bwato lopalasa. Madzi osekukira anakwera. Ndipo, chabwino, usiku umenewo pamene ine ndinali nditalalikirira Uthenga ndipo ndinalisiya Baibulo langa liri lotsegula pa guwa pamene ine ndinapita kunyumba; kuneneratu kuti chigumula chidzabwera, Ine ndinati, “Ine ndinamuwona iye akuyeza mapazi twente thuu pa Spring Street kumusi kuno.”

<sup>138</sup> M’bale Jim Wiseheart wokalamba ndi iwo anandiseka ine. Inu mukukumbukira zimenezo, M’bale George? Ine ndinati. . . Iye—iye anati, “Oh, Billy, mu ’84 zinali pafupifupi mainchesi sikisi okha pa Spring Street.”

<sup>139</sup> Ine ndinati, “Ine ndinaona munthu akutsika kuchokera kumwamba, ndi kutenga ndodo yoyezera ndi kuyimatirira iyo pa Spring Street, anati mapazi twente thuu.”

Iye anati, “Iwe wangotengeka.”

Ine ndinati, “sindinatengeke! Ndi PAKUTI ATERO AMBUYE!”

<sup>140</sup> Afunseni iwo kuti anali mapazi angati pa Spring Street. Mapazi twente thuu kupita ku—ku inchi! Ndendende.

<sup>141</sup> Ndipo Baibulo lakale lija pamene ilo linalalikiidwa usiku umenewo. . . Kunayamba kugwa mvula, madzi osekukira akutulukira ndi zina zotero, ndipo mpingo wakale uwu. . . Mipando inakwera molunjika mpaka ku denga, Baibulo linapita molunjika mpaka ku denga, kutsuka apa ndi madzi onsewo kulikweza ilo m’mwamba. Guwa linapita molunjika kumene m’mwamba. Iwo anatsika pansu pomwe; ndipo mpando uliwonse unakhala mu malo omwewo, ndipo Baibulo linakhala momwemo mu malo omwewo, ndipo madzi onse awo, ndipo likadali chitsegulire, mutu womwewo pa malo omwewo.

142 “Miyamba ndi dziko lapansi zidzatha, koma Mawu Anga sadzatha konse.”

143 Baibulo ilo linayandama chotani nanga m’madzi amchere amenewo kwa zaka ziwiri popanda ngakhale kudetsa mawuwo pa Ilo! Mawu a Mulungu ndi owona. Amen.

144 Ine ndikukumbukira pambuyo pake, M’bale Jim Wiseheart wokalamba anali wokhutitsidwa ndi zimenezo, nthawi zonse iye amamva ululu pa mkono wake. . . Iye anakhala ngati anali ndi vuto pamene iye anafika pafupifupi usinkhu wa zaka sevente faivi, iye anali ndi nyamakazi. Ululu unkafika pomupweteka *apa*, iye ankathamanga kukatenga Baibulo, ndi kulitsegula ilo, kuliyika pamenepo, kuwawa kwina pansi *apa*. Ine ndinabwera kumeneko tsiku lina ndipo iye anali ndi Mabaibulo ochuluka kwambiri pa iye moti sindinathe kumuwona M’bale Jim, iye anali atangokhala ndi Mabaibulo paliponse pa iye! Iye anati, “Ndi lonjezo la Mulungu!” Ndi zimenezotu.

145 “Miyamba ndi dziko lapansi zidzapita, koma Mawu Anga sadzapita konse.”

146 Kumbukirani munthu wachikulire uja anakakonda kubwera ndi kudzandiwona ine. Ndipo palibe aliyense wa anthu ake pano ine sindikuganiza. Ndipo ine ndinkakonda kumuthandiza iye pang’ono, inu mukudziwa, motsatira, chifukwa iye anali wokalamba ndipo ankasowa ndalama ndipo iye ankabwera kumeneko. Iye anatero. . . Tsiku lina ndinali kupita ku Canada, ndinatembenuka, ndinangotuluka pa chipata, ndipo iye anati, “Billy, mwana wanga, limodzi la masiku awa iwe udzabweranso ndipo Amalume okalamba a Jim sadzakhala akuyenda njira iyi kenanso.” Imeneyo inali nthawi yomaliza. Pamene ine ndinali ku Canada, ine ndinalandira telegalamu; iye anali atafera komweko mu mikono ya Mlongo Morgan. Iye anali ndi vuto la mtima, ndipo iwo anathamangira naye ku chipatala, anayang’ana mmwamba pa iye ndipo anafa.

147 Mlongo Margie, kodi iye ali pano mmawa uno? Nthawi zambiri iye amabwera. Inu nonse mukudziwa. Limodzi la vuto lalikulu la khansa limene kutsidyako mu Chipatala cha Baptisti iye wakhala wakufa kwa zaka seventini, pa Chipatala Chaching’ono uko pa zolembedwa, za “okufa ndi khansa,” zaka seventini zapitazo. Iye amakhala ku 412 Knobloch Avenue, kuchita unamwino mchipatala kunja kuno. Oh, chisomo chodabwitsa, kukoma kwake!

148 Jim Tom Robertson, woyimira mlandu ku Louisville, ndipo ife tonse timamudziwa Jim Tom. Ndicho chimene chinamupangitsa iye kuti akhulupirire Uthenga uwu, iye anapita kumeneko. Ndipo abambo ake ndi mmodzi wa atsogoleri a antchito awo ku chipatala kumeneko. Iye anapita uko ndipo anakafufuza zimenezo, kuti akapeze ngati izo zinali zoonza kuti iye anali kufa ndi khansa, ndipo anaperekedwa ndipo

anatumizidwa kwawo, ndipo anaganiza monga momwe iwo amadziwira kuti iye anali atafa kale. Ndipo abambo ake anazifufuza zonse, ndipo icho ndi chowonadi. Ndipo Jim Tom anati, “Ndi bodza; iye wakhala pomwe pano tsopano, ine ndikhoza kukutengerani inu kwa iye.”

<sup>149</sup> O, O, Iye—Iye ndi Mulungu weniweni, si choncho Iye? Ndine wokondwa kuti Iye akhoza kuyang’ana pa zolakwa zathu, sichoncho inu? Zimatipangitsa ife kumukonda Iye ndi mtima wathu wonse.

<sup>150</sup> Mipandoyachifumu, mphezi...Chiyani? “Nyali seveni,” kapena nyali, kapena nyenyezi seveni, zotchedwa “Mizimu seveni,” kutanthauza mawo-...mawonetseredwe seveni a Mzimu Woyera a Mibadwo Isanu ndi iwiri ya Mpingo pa mipando seveni ya chifundo kwa anthu. Apa izo ziri: mipando seveni yachifundo, mipando seveni, mipingo seveni, nyenyezi seveni, mawonetseredwe seveni, Mizimu seveni, nyali seveni. Oh, mai, momwe Mulungu aliri wangwiro kwambiri! Aliyense. . .

<sup>151</sup> Zinali pamenepo mu manambala a Baibulo; manambala a Baibulo ndi chinthu changwiro kwambiri chomwe chilipo pa dziko lapansi. Inu simungapeze chilema chimodzi kuchokera ku Genesis mpaka Chivumbulutso, mu manambala a Baibulo. Osati buku lina lolembedwa lomwe inu simungapeze cholakwika inu musanawerenge ndime zitatu; koma osati mu Bai- . . .

<sup>152</sup> Iwo akhala akuyesera kwa zaka zopitirira thu handiredi kuti awonjezere chiganizo chimodzi ku Pemphero la Ambuye, kapena kuchotsapo chimodzi kwa Ilo. Ndi langwiro! Simungathe kuwonjezera zina kapena kuchotserapo kwa Ilo. Iwo akhala akuganiza kuti alipanga pempherolo kukhala labwinoko pang’ono. Iwo amayesa kutambasula *izi* mwa Ilo, ndi kuyika *izo* mwa Ilo, kapena kuchotsa *izi* mwa Ilo; izo siziri zolondola basi. Mwaona, Ndi zangwiro! Njira zonse za Mulungu ndi zangwiro.

<sup>153</sup> Chotero ndife opanda ungwiro, koma Iye anati “Chotero khalani inu angwiro monga Atate wanu wa Kumwamba ali wangwiro.” Kodi ife tingakhale bwanji? Kudzera mu Mwazi wantengo wapatali wa Yesu Khristu, kudziyiwala ife tokha ndi kungokhala mwa Iye. Ndi inu apo. Ndi wofunika bwanji Iwo!

<sup>154</sup> Chabwino, ndime ya 6 tsopano ngati ife titi tilowe mu iyo. “Nyali seveni.”

*Ndipo patsogolo pa mpandowachifumu...panali nyanja yamandala yofanana ndi krustalo: ndipo pakati pa mpandowachifumuwo, ndi pozungulira mpandowachifumuwo, panali zamoyo zinayi zodzala ndi maso kutsogolo ndi kumbuyo. (Oh, mai! Tayang’anani pa izi!)...zamoyo zodzala ndi maso—zodzala ndi maso kutsogolo ndi ku-... (Tsopano, dikirani.)...patsogolo pa mpandowachifumu...*

*panali nyanja yamandala yofanana ndi krustalo: ndipo pakati pa mpandowachifumuwo, panali zinayi... ndi pozungulira...pampandowachifumuwo, panali zamoyo zinayi zodzala ndi maso kutsogolo ndi kumbuyo.*

<sup>155</sup> Tsopano, a “nyanja ya mandala.” Inu amene muti mu... ndine...Ichi si mwa chizindikiro mochuluka apa, koma ine ndikufuna kuti ndifufute izi kwa miniti. Tsopano, tsopano ife tikufuna kuti tiphunzire apa pang’ono pokha. Nyanja yamandala imayimiridwa mu kachisi wakale, pakuti Mose analumulidwa ndi Mulungu kuti amange kachisi pa dziko lapansi monga iye anaziwonera Izo mu miyamba. Aliyense amadziwa zimenezo. Chabwino.

<sup>156</sup> Ndipo ndiloleni ine ndingojobwala pang’ono pokha apa tsopano, ndikunena, *apa* panali chombo mu Chipangano Chakale, chabwino, chinthu chotsatira, icho chinkatchedwa “Oyeretsesa a oyera.” Ndipo malo otsatira apa anali guwa, limene linali kutchedwa “malo oyera.” Ndipo pomwe *pano* panali “nyanja yamkuwa,” inkatchedwa. Mu kunena kwina, anali malo amene nsembe...nsembe zinkatsukidwa—zinkatsukidwa apa izo zisanalandiridwe...pa guwa; pa guwa la mkuwa, kapena guwa lamkuwa limene nsembe inkawotchedwa.

<sup>157</sup> Tsopano, ife tikufuna kuti tiwone izi tsopano pamene... kumene kunali. Ndipo, tsopano—tsopano, mu nyanja ya mandala iyi...inali patsogolo pa Mpandowachifumu ndi patsogolo pa malo woyera. Basi...Tsopano kumbukirani, zoyikapo nyali seveni zagolide zitayikidwa *apa* monga chonchi, ndipo zinabwera mu mphika. Mukuona? Tsopano, izo ndi zomwe zikunyezimiritsa kuwala kuchokera ku malo oyera mpaka *kuno*. Tsopano, ngati inu...ayi, inu simukuyenera kulemba izi pokhapokha inu mwangofuna kuteru, koma ndizo...Ine ndiri ndi chinachakenso apa chimene ine ndinachijambula ndekha, chimene ine ndimafuna kuti ndichitengere kwa inu. Koma tsopano, inu mukuona, *iyi* inkatchedwa nyanja ya mkuwa; sichinali chachikulu chotero, icho chinakhazikitsidwa mochuluka kapena mocheperapo mu kachisi. Iyo inali pafupifupi monga *chonchi* apa, inali nyanja yamkuwa, unali mphika wopangidwa ndi mkuwa kumene iwo ankatsukamo nsembe. Nsembezo zisanaotchedwe kapena kulandiridwa, izo zinkayenera kuti zitsukidwe.

<sup>158</sup> Oh, kodi izo sizingapange ulaliki pakali pano, Dokotala. Oh, mai! Zimenezo sizikanati—zimenezo sizikanatero basi... Izo zangondikhudza ine, “ankazitsuka izo.” Nsembe iliyonse isanalandiridwe kwa Mulungu, iyo imayenera kutsukidwa poyamba. Motani? Osati motentheka, koma kutsukidwa ndi Mawu. Tsopano, ife tikhoza kubwerera ndi kukafika pamene mphunzitsi Wachiyuda uyu...pamene ine ndinali kulalikira pa ulaliki umenewo wa madzi olekanitsa, ng’ombe yamphongo

yofiira, madzi omwe ankasungidwa, kuti iwo ankapangidwa kukhala madzi olekanitsa. Ndipo ife tisanati tibwere konse kwa Mulungu ndi chikhulupiro chowona, ife choyamba timayenera kubwera mwa madzi olekanitsa. Inde, bwana. Inu mumayenera kubwera mwa chiyani? Mawu!

<sup>159</sup> Oh, ndiloleni ine ndingowona ngati ine ndingakhoze kuyankhula basi kuti inu mutero...aliyense amvetse izo. Tsopano valani kuganiza kwanu kwauzimu. Chotsani chigoba chankhondo ndipo muvale kuganiza kwanu kwauzimu tsopano, chifukwa apa pakubwera chinachake. “Kutsukidwa iyo isanalandidridwe pa guwa,” choyamba iyenera kutsukidwa ndi madzi olekanitsa.

<sup>160</sup> Tsopano, tembenuzani nane mofulumira ndithu ku Aefeso 5, ingogwirani malo anu ndi kubwerera mmbuyo, masamba ochepa chabe mmbuyo, ku Aefeso mutu wa 5 ndi ndime ya 26:

*Kuti iye akayiyeretse ndi kuyitsuka iyo... (Mpingo, iye akuwukamba.)*

<sup>161</sup> Mwaona, tsopano, ndiloleni ine ndibwerere mmbuyo patsogolo pang’ono kuposa apo. Bwererani mmbuyo pafupifupi ndime ya 21, pamene inu mukuyang’ana:

*Dziperekeni nokha kwa wina ndi mzake mu kuopa Mulungu.*

<sup>162</sup> “Dziperekeni nokha.” Osonkhana, dziperekeni nokha kwa abusa anu. Abusa, dziperekeni nokha kwa osonkhana anu. Ngati kagulu kakang’ono kadzukapo, musakhale mbali iliyonse, dziperekeni nokha ku mpingo wonse. Mpingo, ngati inu muyamba kagulu, dziperekeni nokha kwa abusa anu mu kuopa Mulungu. Mukuona? Oh, m’bale! Hmm!

*Akazi, dziperekeni nokha kwa mwamuna wa inu eni, monganso kwa Ambuye, (Chifukwa iye ndi mbuye wanu.)*

<sup>163</sup> Ndi angati akudziwa zimenezo, akazi inu? Ndizo ndendende kulondola. Baibulo linanena chomwecho pachiyambi. Izo zikadali momwemo.

*Akazi, dziperekeni nokha kwa mwamuna wa inu eni, monga kwa Ambuye.*

*Pakuti mwamuna ndi mutu wa mkazi, ngakhale monga Khristu ali mutu wa mpingo: ndipo iye ndi mpulumutsi wa thupilo.*

<sup>164</sup> Momwemonso ali mwamuna. Inu nonse mukudziwa zimenezo, inu anthu okwatira ndi achikulire, kapena ana okulirapo mokwanira kuti adziwe njira ya moyo. Chabwino.

*...monga kwa Ambuye.*



*Pakuti mwamuna ndi mutu wa mkazi, ngakhale monga Khristu ali mutu wa mpingo: ndipo iye ndi mpulumutsi wa thupilo.*

*Kotero monga mpingo umamvera Khristu, koteronso akazi akhale kwa amuna awo a iwo okha mu zonse.*

*Amuna, kondani akazi anu, ngakhale monga Khristu nayenso anawukonda mpingo, ndipo anadzipereka iyemwini chifukwa cha iwo; (Musamuponde iye! Ngati inu muchita zimenezo, inu simuli woyenera kukhala mwamuna. Uko nkulondola!)*

*Kuti iye akhoze . . .*

Mvetserani, ndi izi apa! Mumve izo pano:

*Kuti akaliyeretse ndi kulisambitsa ndi kutsuka kwa madzi mwa . . . [Osonkhana akuti, “Mawu.”—Mkonzi.] Hmm!*

<sup>165</sup> Ndiye, wopembedza aliyense amene adzapeza mwayi mu Izi ayenera kubwera mwa Mawu. Pali ambiri omwe amabwera mwanjira ina. Ine ndimakhulupirira mu nkhani zazing’ono ndi zinthu, zokhudza “amayi anamwalira zaka zambiri zapitazo ndipo akukuyembekezerani Kumwamba,” izo zimachita bwino *pambuyo* pogwiritsa ntchito Mawu. Anthu ambiri amabwera ku guwa chifukwa iwo amafuna kuti akakomane ndi amayi awo Kumwamba. Izo ndizabwino, inu muyenera kuchita zimenezo, koma chimenecho si chifukwa chimene inu mumabwerera ku guwa. Inu mumabwera ku guwa mukuvomereza machimo anu chifukwa Khristu anafa mmalo mwanu, mwa Mawu!

<sup>166</sup> Ndiye, nsembe iliyonse yosabwera molingana ndi Mawu ndi yosalandiridwa ndiye. Ndi kulondola uko? (Oh, m’bale, ine ndimadana nazo kunena izi. Oh, ine ndimadana nazo kuzinena zimenezo. Ndikhululukireni ine chifukwa chonena zimenezo.) Ndicho chifukwa chimene Machitidwe 19 amaima mu Baibulo, “Kodi inu munalandira Mzimu Woyera kuchokera pamene inu munakhulupirira?”

Iwo anati, “Ife . . . kaya unalipo . . .”

Anati, “Ndiye, inu munabatizidwa bwanji? Chifukwa chiyani inu simunalowe Munu?”

<sup>167</sup> Iwo anabwera mwanjira ina pambali pa Mawu! Anati, “Oh, ife tinadutsa kudzera mu njira, ife tinabatizidwa . . . Yohane.”

Iye anati, “Izo sizingagwire ntchito. Yohane ankabatiza kwa kulapa kokha, osati ku chikhululukiro cha machimo.”

<sup>168</sup> Ndipo pamene iwo anamva Izi, iwo anabatizidwanso. Bwanji? Mwa Mawu! “Kutsukidwa ndi madzi a Mawu.” Mawu anati, “Dzina la Yesu Khristu!” Chirichonse chomwe chimayika china chirichonse pa Icho ndi chabodza!

<sup>169</sup> Tsopano, m'bale wanga wofunika, ine ndikudziwa kuti iyi ndi tepi nayonso. Tsopano, musatengeke. Ndiloleni ndinene izi ndi chikondi chaumulungu, ora layandikira pamene ine sindingathe kukhalabe chete pa zinthu izi kenanso, pafupi kwambiri ndi Kudza. Mukuona? “Utatu ndi wa mdierekezi!” Ine ndikunena zimenezo PAKUTI ATERO AMBUYE! Yang'anani kumene izo zinachokera. Izo zinachokera ku Bungwe la Nicene pamene mpingo wa Katolika unakhala mu ulamuliro. Mawu akuti “utatu” Sanatchulidwe nkomwe mu Bukhu lonse la Baibulo. Ndipo kunena za Milungu *itatu*, ndizo zochokera ku gehena. Pali Mulungu mmodzi. Ndizo ndendende kulondola.

<sup>170</sup> Tsopano, kodi inu mukuti ndiye, “Kodi inu mukukhulupirira kuti anthu onse awa amene—amene ali a utatu ndi akugehena?” Ayi, bwana. Ine ndikukhulupirira iwo ndi Akhristu. Koma oralo likuyandikira, m'bale, pamene iwo akulakwitsa mowonamtima.

<sup>171</sup> Munthu aliyense, kulikonse, nthawi iliyonse, yemwe akufuna kuti ayankhule pa phunziroli, abwere kwa ine; mtumiki aliyense, bishop, alikibishop, chirichonse chimene inu mungakhale. Ndipo izi zikujambulidwa, zidzapita kuzungulira dziko lapansi. Ine ndikupempha mu chikondi chapaubale, kwa munthu aliyense amene ati andimve ine pa tepi iyi kuzungulira dziko lapansi, amene adzabwere kwa ine ndi kundiwonetsa ine mutu umodzi wa Lemba kapena ndime imodzi mu mbiriyakale iliyonse (iyo ndi mbiri yowona) kumene kuti munthu aliyense anayamba wabatizidwapo mu dzina la “Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera” kufikira iwo atachita bungwe ndi mpingo wa Katolika, ine ndisintho chiphunzitsa changa. Munthu aliyense anabatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu! Ndipo abale anga ofunika, maso anu achititsidwa khungu ku zinthu zimenezo. Pempherani Mulungu akupatseni inu Kuwala!

<sup>172</sup> Tsopano, ngati inu muli ndi Lemba lothandizira izo, ine ndikhala ndikukufunani inu kapena kumvetsera ku telefoni yanu. Ndinu...inu...Kupitirira tepi iyi, inu mukuyenda mwadala mu umbuli wauzimu ngati inu simunditsutsa ine pa zimenezo. Ngati inu mukufuna kudziwa Kuwala ndi chiyani ndipo mdima ndi chiyani, tiyeni timufunse Mulungu. Kumbukirani, ine ndikuti PAKUTI ATERO AMBUYE! Ngati inu mukundikhulupirira ine kukhala wantchito Wake...Ndipo ngati izo sizinali molingana ndi Mawu, izo zikanakhala zolakwika. Ndiye ngati izo siziri molingana ndi Mawu, ndi uindo wanu kuti mubwere mudzandiwongole ine, uh-huh, muwone chimene chichitike. Uh-huh. Ndi kulakwitsa!

<sup>173</sup> Ine ndikukhulupirira kuti masauzande ambiri a anthu a utatu amene amakhulupirira mwa Milungu itatu amapulumsidwa, chifukwa iwo samadziwa kusiyana kulikonse. Ife tifika ku izo mpaka mmusi mu uthenga.

<sup>174</sup> Tsopano, inu nonse musayimitse tepi yanu ndi kutuluka

mnyumbamo, inu abale a utatu; mvetserani kwa Ichi. Koma inu mungokhazikikabe mphindi zochepa. Inu muli ndi ngongole kwa inumwini. Muli ndi ngongole ku mpingo wanu. Mukuona? Musasiye kutenga matepiwo, ingokhalani nawo Iwo. Fufuzani Izo ndi Mawu ndi kuwona ngati Izo ziri zolondola. Baibulo linati, “Tsimikizirani zinthu zonse.”

<sup>175</sup> Ine ndikudziwa kuti ndizosatchuka, Yesu analinso choncho, Uthenga unalinso choncho, nthawizonse. Munkandikonda ine pamene ndinkabwera ndi kudzachiritsa odwala ndi osautsika pakati panu, inu munkaganiza kuti izo zinali zazikulu, makamu aakulu ndi kuwumanga mpingo. Tsopano, Yesu anachita chinthu chomwecho mpaka tsiku lina Iye ankayenera kufika ku Choonadi. Ndipo pamene Iye anatero, ngakhale sevente anachoka kwa Iye. Ndipo Iye anatembenukira kwa otsalawo, thwelovuwo, ndipo anati, “Kodi inunso mupita?”

Ndipo Petro ananena mawu odziwika aja, “Ambuye, kodi ife tingapite kwa ndani, pakuti Mawu Anu okha ndi Amuyaya?”

<sup>176</sup> Ndipo Mawu a Mulungu okha ndi Amuyaya! Ndipo mundipezere ine paliponse pamene Mulungu anayamba wakhalapo naye aliyense yemwe anabatizidwa mu dzina la “Atate, Mwana, Mzimu Woyera.”

<sup>177</sup> Inu mupite ku Mateyu 28:19, “Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera,” pamene Mateyu anati, “Pitani inu kotero, ndi kukaphunzitsa mafuko onse, kuwabatiza iwo mu Dzina la Atate, Mwana, Mzimu Woyera”? Ndipo aliyense amene amaganiza kuti “Atate, Mwana, Mzimu Woyera” ndi dzina, zikusonyeza kuti pali chinachake cholakwika ndi maphunziro awo. (Tsopano, kwa wophunzira wa giredi seveni kuti azinena zimenezo kwa mabishopu amene akumvetsera kwa *Izi*.) *Atate* si dzina, *Mwana* si dzina, ndipo *Mzimu Woyera* si dzina. Iwo ndi *maudindo* amene amapita ku *Dzina* (la Atate, Mwana, Mzimu Woyera), limene liri Yesu Khristu.

<sup>178</sup> Kumbukirani, izo siziri mu mkwiyo, izo zikunenedwa mu chikondi ndi ulemu waumulungu, ndi chikondi ndi kulingalira kwa Thupi lathunthu la Khristu kumene ine ndayitanidwa ndi abale anga a utatu (ndi pa dziko lonse lapansi) kuti ndibwere ndi kudzalalikira mu mpingo wawo. Koma ine sindimazitchula konse izo pamene ndiri pakati panu. Ndikufuna kuti ndikhale. . . Pokhapokha mutandifunsa inueni, ndipo ndidzapita nanu ku parishu ndi kukayankhula nanu za izo. Koma pamaso pa mpingo wanu, izo zingawatakase iwo. Ndi malo anu kuti mutenge Vumbulutso ndi kupita kukaphunzitsa nkhosazanu, ndinu m’busa wa nkhosazo. Ine ndikuyankhula kwa atumiki. Ngati inu simukumvetsa, bwerani, tikhale ndipo tikambirane pamodzi. Baibulo linati, “Tsimikizirani zinthu zonse, ndipo gwiritsitsani ku chomwe chiri chabwino.”

179 “Nyanja ya mandala,” kumene nsembe inkatsukidwa... Ndipo ife tatsukidwa... Oh, musaiwale izo, ife tikubwerera ku zimenezo pakapita kanthawi, “Kutsukidwa ndi madzi a Mawu.” Ndiye inu mumayenera kumva Mawu musanalowe mmenemo, chifukwa njira imodzi yokha imene mungafikire kwa Mulungu, ndiyo mwa chikhulupiriro. Ndi kulondola uko? “Chikhulupiriro chimadza pa kumva, kumva kwa Mawu,” kutsuka chikumbumtima chathu. Osati kuti tikumane ndi munthu, osati kuti tikumane ndi abambo, osati kuti tikumane ndi amayi, osati kuti tikumane ndi khandanda (zonsezo nzoona, ife tichita zimenezo), koma chinthu choyamba chimene ife tiyenera kubwerako ndi njira ya Mulungu ya kafikidwe; ife tidzatsukidwa pamene timva Mawu a Mulungu.

180 Mwa chikhulupiriro ife tikuyenda. *Chisomo*, “chimene Mulungu anakuchitirani inu.” Uko nkulondola. Inu mumakhulupirira Mulungu, inu mumakhulupirira pa Mulungu; ndipo mwamsanga pamene inu mwapepesa, inu mwakhululukidwa kale.

181 Pamene ine ndinali kuyankhula kwa m’bale dzulo, ndinakhala ngati ndinasokonezeka pang’ono pa izo, ndipo ine ndinati, “Taonani, m’bale, ngati inu munanena chinachake chomukhumudwitsa mkazi wanu, mwamsanga inu mungamumvere chisoni iye, inu mumapepesa kuti munachita icho, inu mwalapa kale mu mtima mwanu. Ndiko kulondola. Koma inu mumayenera kuti mupite mukamuze iye za izo. Inu mumayenera kupita ndi kuti, ‘Wokondedwa, ine—ndikupepesa kuti ndinanena zimenezo.’ Ndiye inu mwalapa kotheratu.” Tsopano, umo ndi momwe ziliri ndi Mulungu.

182 Munthu amene angapite ndi kuti, “Ndapweteka kumverera kwake, sizimapanga kusiyana kulikonse, ndimuwuza iye kuti ndikupepesa, koma kwenikweni ine sindikutero,” ndiwe wachinyengo. Mukuona? Ndiko kulondola. Zimenezo sizidzalandidwa konse ndi Mulungu.

183 Muyenera kumva chisoni kotheratu ndi machimo anu. Ndiye pamene inu mukudziwa kuti muli achisoni chifukwa cha machimo anu, ndiyeno “Lapani, ndi kubatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhululukiro cha machimo anu, ndipo inu mudzalandira chikhululukiro, mudzalandira Mzimu Woyera.” Mwaona, mophweka basi, Mulungu wazipanga izo mophweka kwambiri.

184 Apa ti...tikuzindikira apa mu “nyanja ya mandala,” inkafanizidwa ndi krustalo. Tsopano, nyanja ya mandala ikuphiphiritidwa, kuyimiridwa ndi nyanja yamkuwa. Iyi ndi nyanja ya mandala, Kumwamba. Mose anayiona iyo ngati nyanja yamandala ndipo anapanga chimene chinkatchedwa “nyanja yamkuwa,” guwa lamkuwa, nsembe yamkuwa... guwa lamkuwa, kani.

185 Inu mukudziwa mkuwa umakamba za chiyani mu Baibulo? Chiweruzo. Iye anapanga njoka ya mkuwa. Kodi *njoka* imatanthauza chiyani? Chizindikiro cha *njoka* chinkatanthauza “tchimo loweruzidwa kale,” m’munda wa Edeni, pamene, “chidendene chako chidzavulaza mutu wake; mutu wake udzavulaza chidendene.”

186 Ndipo *mkuwa* umayimira “Chiweruzo cha Mulungu,” guwa la mkuwa, kumene nsembe inkawotchedwa; mphika wa mkuwa, kumene iwo unkatsukidwa ndi madzi a Mawu. Mukuona? Mo-. . . Eliya, mu masiku ake, anatuluka ndipo anayang’ana m’mwamba, ndipo anati, “Kumwamba kukuwoneka ngati mkuwa.” (Chiweruzo Chauzimu pa fuko lokanidwa.) Oh, mai! Mkuwa, kwa mkuwa!

187 Tsopano ife tiri pa “mphika.” Ndipo munaona kuti mphika uwu unalibe kanthu ndipo unali wowala ngati krustalo. Chifukwa chiyani? Mpingo unali utawomboledwa kale!

188 Tsopano, tsopano, ife tikuzindikira patsogolo pang’ono, ngakhale, pamene oyera a Chisawutso akubwera, ife tikupezanso itadzala ndi moto. Kodi inu mumadziwa. . . Kodi inu mungakonde kuwerenga zimenezo? Tiyeni tipite ku Chivumbulutso tsopano, mutu wa 15, ndime ya 2, ndipo tiwerenge pamene ife tikuona moto wamkuwa uwu kachiwiri. Chabwino:

*Ndipo ndinaona mngelo wina. . . Ine ndinawona chizindikiro china kumwamba, (Kulondola.) aakulu ndi odabwitsa, angelo seveni ali nayo. . . miliri seveni yotsiriza; pakuti mwa iwo ndi modzala ndi mkwiyo wa Mulungu.*

Tsopano “mkwiyo” wa Mulungu. Penyani:

*Ndipo ine ndinawona ngati iyo inali nyanja yamandala yosakanikirana ndi moto: (Tsopano, penyani.) ndi iwo amene anakhala nacho chigonjetso pa chirombocho, ndi pa fano lake, ndi pa chilembacho, ndi pa chiwerengero cha dzina lake, anayima pa nyanja yamandala, ali nawo. . . azeze a Mulungu.*

*Ndipo iwo anayimba nyimbo ya Mose mtumiki wa Mulungu, . . .*

189 Oh, inu mukuziona izo? “Nthawi ya chisautso.” Oh! Kodi inu muli pa changu? [Osonkhana ayankha, “Ayi.”—Mkonzi.] Chabwino, mvetsarani, tiyeni tizindikire chinachake apa.

190 Ife timabwera bwanji? Ife tikuyenera kubwera (Mpingo wa Amitundu uwu) ku Mawu awa, nyanja ya mandala, madzi, madzi a Mawu (Ndi kulondola uko?), zindikirani Mawu momwe Iwo analembedwera. Ndiye nsembeyo imalandiridwa ndi kudzazidwa ndi Mzimu Woyera kuchokera mkati, kuwalira kupyolera mu Kuwala kwa m’badwo umenewo. Kuchokera pa

izi... Apa Iko kukutuluka mu malo opatulika kulowa *muno*, kuchokera mu nyenyezi kulowa *muno*. Mukumvetsa izo?

<sup>191</sup> Zindikirani, tsopano, pa mapeto a m'badwo uwu, Yohane, pamene iye anawona nyanja ya mkuwa pamenepo, iyo inali "yowala ngati krustalo." Chinali chiyani icho? Mawu anali atachotsedwa pa dziko lapansi, atakwatulidwa mu Mpingo, ndipo iyo inali "yowala ngati krustalo," kunalibenso Magazi, m'badwo wa Mpingo unali utatha.

<sup>192</sup> Tsopano, mu Chivumbulutso 15, otsalira a Mbewu ya mkazi, omwe anali oyera a Chisawutso amene anadutsa mu Chisawutso, anapezeka (Taonani!) atayima pa nyanja iyi. Ndipo iyo inadzazidwa ndi moto, magari, malawi ofiira akuyaka, moto wa Mulungu. Iwo anali atachigonjetsa chirombo (Roma), apo pa chiwerengero chake, pa chilembo cha dzina lake, ndi pamwamba pa fano lake (Mgwirizano wa Mipingo), ndipo anali atatuluka. Ndipo kudzera mu kulalikira kwa Mose ndi Eliya, aneneri awiri aja amene ati adzawonekere kwa Israeli kuti akatulutsemo... gulu ili la anthu, oyera a Nthawi ya Chisawutso amenewo, m'mbuyo mu nthawi imeneyo amene ati adzabweretsedwemo, anali...

<sup>193</sup> Mwaona, Mpingo wakwatulidwa tsopano, koma kumbukirani Mkazake ali pa Mpandowachifumu. Nthawi ya Chisawutso... Anakhala mu maufumu, kunja, ndipo anabweretsa mafumu awo onse ndi ulemu wawo ndi ulemerero mu Mzinda. Pamene ife tifika mmusi mu Chivumbulutso 22, inu muziwona izo. Ngati inu mukulemba izi ndi kuzigwira, ife tikafika ku izo muwona zomwe ife tikutanthauza. Ife tiribe nthawi yoti tingogwira kanthu kakang'ono kalikonse ndi kumaziyendetsa m'mbuyo ndi mtsogolo, koma kukhudza malo ofunikira ake. Ndiye tsiku lina, mwinamwake, Ambuye akalola, ife tidzakhala ndi nthawi yochuluka yoti tidzakambe za zimenezo.

<sup>194</sup> Tsopano, oyera a Nthawi ya Chisawutso awa amene anabwera, anali atadutsa mu masautso aakulu. (Mpingo sudzadzutsa mu Chisautso! Kodi mukuona kuti iwo anali kale mu Ulemerero?) Ndipo apa pali oyera a Chisawutso, oyeretsedwa amene anali... pokhala ndi langa ndi vuto lanu iwo anali asanamvepo Mawu. Ngati iwo anawamva Iwo ndi kuwakana Iwo, iwo anapita ku gehena; iwo anaponyedwa kunja ku mdima wakunja chifukwa iwo anawakana Mawu. Koma ngati iwo akanati asawamve konse Iwo, Mulungu ali wolungama, Nthawi ya Chisawutso idza kwa iwo.

<sup>195</sup> Tsopano, zindikirani miniti yokha. Oyera otsukidwa ndi Mawu omwewo, chifukwa ndi guwa lomwelo, ndi nyanja yamandala yomweyo ndi Mawu omwewo. Chivumbulutso 2:5, Chivumbulutso 15: (kapena kani) :2 mpaka :5. Zindikirani, miniti yokha. Tsopano, ife sitinatengere konse Mawu kwa

iwo, ndicho chifukwa iwo anali—iwo anali monga choncho. Ife sitinatengere konse Mawu kwa iwo, ife tidzayimbidwa mlandu. Kotero ife sitingathe kugwira anthu onse; Mpingo sudzatero (mu m'badwo uno) amene ali ndi Choonadi. Chifukwa iwo adzadutsa mu Chisawutso, iwo si Oyera amene anafa kale m'mbuyomo mu mibadwo ya mpingo imeneyo, chifukwa iye anati “Iwo anatuluka kuchokera mu Chisawutso chachikulu,” ndipo Chisawutso chachikulu chikadali chamtsogolo, Mpingo ukapita Kwawo.

<sup>196</sup> Oh, ndi zimenezotu! Oh, ndikuzikonda izo! Mvetserani! Tiyeni tipite patsogolo pang'ono, ine ndikufuna kuti ndiwone mtundu wa Mawu amene iwo anawamva. Tsopano, tiyeni tiyambirenso pa ndime ya 2 ya mutu wa 15.

*Ndipo ine ndinaona ngati inali nyanja yamandala yosakanikira ndi moto: ndi iwo amene anali atagonjetsa chirombocho, . . . pamwamba pa fano lake, . . . pamwamba pa chilemba chake, . . . pamwamba pa chiwerengero cha dzina lake, anaima pa nyanja yamandala, ali nawo . . . azeze a Mulungu.*

<sup>197</sup> Tsopano, onani, iwo anali asanalowemo, koma iwo anali atawamva Mawu. Iwo anali atawamva Mawuwo. Tsopano, mvetserani, onani mtundu wa Chiphunzitso chimene iwo anachimva, muwone ngati icho chikufanana ndi Mpingo tsopano.

*Ndipo iwo anayimba nyimbo ya Mose wantchito wa Mulungu, (Ndizo, Mose atatha kuwoloka.) ndi nyimbo ya Mwanawankhosa, yakuti, Zazikulu ndi zozizwitsa ziri ntchito zanu, Ambuye Mulungu Wamphamvuzonse; (Kodi Mwanawankhosa ameneyo ndi ndani?) Ambuye Mulungu Wamphamvuzonse; zolungama ndi zoonza ziri njira zanu, inu Mfumu ya oyera mtima.*

<sup>198</sup> Mukuona chimene iwo anamuzindikira Iye kukhala? Osati munthu wachitatu mu utatu, koma “Ambuye Mulungu Wamphamvuzonse, Mfumu ya Oyera Mtima!” Mvetserani! Inu mwakonzeka? Ndime ya 4:

*Ndani yemwe sadzakuopani Inu, O Ambuye, (chilemba chachikulu A-m-b-u-y-e, Elohim) ndi kulemekeza . . . Ndani watsala amene sadzakuopani inu, . . . ndi kulemekeza dzina lanu? . . .*

<sup>199</sup> Iwo anatsukidwa ndi madzi omwewo amene inu mukutsukidwa nawo tsopano, kumva Mawu, ndi chikhulupiriro ndi mphamvu ya Yesu Khristu kukhala Wamphamvuzonse. Ndi Vumbulutso lonse pa chiyambi. Chinthu chonsecho chakutidwa mu Vumbulutso la Yemwe Yesu Khristu ali, “Mulungu wopangidwa thupi pakati pathu!”

*. . . lopambana ndi lodabwitsa ndi Dzina lanu, . . .*

*Ndani amene sadzawopa...ndi kulemekeza dzina lanu? inu...muli...pakuti inu nokha ndinu woyera: pakuti mafuko onse adzadza ndi kudzalambira pamaso panu; pakuti ziweruzo zanu zawonetseredwa.*

<sup>200</sup> Mwa kuyankhula kwina: Ife tikuona chimene chikutanthauza kuti musaulandire Iwo, ziweruzo Zanu ziri kuwonetseredwa. Kotero apa ife taima, ife tatsukidwa tsopano, ife tikutsukidwa ndi madzi titadutsa mu Nthawi ya Chisawutso. Ife tatenga kuima kwathu ndi Inu ndipo ife tinakukhulupirani Inu, ndipo tsopano ife taima pa nyanja ya mandala, ndipo ife tikukulemekezani ndi kukukwezani Inu monga chinyezimiritso cha Mzimu Wanu Woyera. Ndipo nyali Zanu ndi zoono, ndipo ziweruzo Zanu ndi zolongama.

<sup>201</sup> Oh, mai! Ife tikhoza kukhala sabata pa zimenezo. “Ubatizo wa Mzimu Woyera,” tiyeni tijambule chinachake apa tsopano, miniti yokha, ine ndiri ndi chinachake chimene ndikufuna kuti ndichijambule. Tsopano, tiyeni...bwanji sitingangotenga izo apo pomwe ife tiri.

<sup>202</sup> Tsopano, ngati ife tingazindikire, apa pali chithunzi chabwino. Tsopano, *apa* pali malo Oyeretsetsa a oyera. Chabwino. *Apa* pali malo opatulika. Ndipo *apa* ndi poyamba, tisanafike pamenepo, pali—pali nyanja.

<sup>203</sup> Chabwino, tsopano zindikirani. Kodi ife timamufikira bwanji Mulungu? “Chikhulupiro chimadza pa kumva, kumva Mawu a Mulungu,” amene akunyezimiritidwa kuchokera ku malo Oyeretsetsa a oyera kupita kwa mtumiki wa m’badwo.

<sup>204</sup> Kubwerera mkati, ndi izo...Mu kachisi wa Solomo, icho chimapereka chinyezimiritso, nyali zimenezo zinkanyezimiritisa nyali zake mu mphika wa mkuwa uja. Kotero, *apa*, mngelo wa m’badwo wa mpingowo akunyezimiritisa m’madzi amenewo amene Munthu yu alimo *apa*, kunyezimiritisa chifundo Chake, Mawu Ake, chiweruzo Chake, Dzina Lake. Zonse zikunyezimiritidwa umu pamene inu mwalekanitsidwa ndi kuzikhulupirira Izo. Kodi inu mukumvetsa?

<sup>205</sup> Zindikirani kukongola kwa izi apa, ife tinkayankhula pa zimenezo tsiku lina. Penyani apa, *apa*, “Chifukwa chake pokhala wolungama, wolungamitsidwa mwa chikhulupiro.” Chabwino, *malo achiwiri*, atatha kutsukidwa “kuyeretsetedwa.” Ndipo, *kenako*, “kudzazidwa ndi Mzimu Woyera.” Kulungamitsidwa, kuyeretsetedwa, ubatizo wa Mzimu Woyera! Inu mukuziona izo? Kodi Uthenga Wake unali wotani? Kulungamitsidwa pa kumva; kuyeretsetedwa ndi zomwe inu mumachita; ndipo polingalira za zomwe inu munachita mu kuyamikira izo, Mulungu anakusindikizani inu ndi Mzimu Woyera.

<sup>206</sup> Tsopano, inu, m’bale wanga wa Baptisti, ine ndikufuna kuti ndikufunsemi inu chinachake. Inu mukuti, “Kodi Abrahamu



akanachita chiyani kusiya kukhulupirira Mulungu? Ndipo Mulungu anamuwerengera iye kwa chilungamo.”

<sup>207</sup> Ndizo zonse zomwe iye akanakhoza kuchita, pomwe *apa*, Iye anakhulupirira Mulungu. Koma Mulungu, kuti avomereze chikhulupiriro chake, anampatsa iye chisindikizo cha mdulidwe, ndi kumusindikiza iye, kusonyeza kuti Mulungu ankayenera kuti azi-...analandira chikhulupiriro chake. Ndipo ngati inu mukudzinenera chikhulupiriro mwa Mulungu, ndipo simunayambe mwasindikizidwapo ndi Mzimu Woyera... Aefeso 4:30, ngati inu mukufuna kuti muzilembe izo, Aefeso 4:30, “Musakwiytse Mzimu Woyera wa Mulungu umene inu munasindikizidwa nawo!” Ndipo inu simumasindikizidwa mpaka inu mutalandira Mzimu Woyera.

<sup>208</sup> Kodi izo zimatenga nthawi yayitali bwanji? Mpaka chitsitsimutso chotsatira? “Mpaka ku chiwombolo chathu, Tsiku lomwelo la chiwombolo.” Palibe njira yopitira kutali kwa Iwo. Inu simungakhoze kuchoka kwa Iwo, chifukwa Iwo sungakhoze kuchoka kwa inu. Mukuona? “Pakuti inu mwasindikizidwa mpaka Tsiku la chiwombolo chanu.” “Palibe chirichonse chamtsogolo, palibe chomwe chilipo, zoopsa, njala, ludzu, imfa, kapena chirichonse, chingakhoze kutilekanitsa ife ku chikondi cha Mulungu chimene chiri mwa Khristu.” Paulo anati, “Ndine wotsimikizika kwathunthu za izo!” Ndi inu apo! Ndi inu apo, inu mwasindikizidwa mpaka Tsiku la chiwombolo chanu.

<sup>209</sup> Zindikirani, izo zidzafika mpaka lotsiriza—Lamlungu lotsiriza kachiwiri. Kodi ine ndiri ndi nthawi? Ine basi... Penyani, penyani ichi, mzimu...mzimu, solo, ndi thupi. Chabwino, mwawona: thupi, solo, mzimu.

<sup>210</sup> Tsopano, ndiloleni ine ndifufute zimenezo ndi kukonza chinachake apa kwa inu. Tsopano, ine ndijambula chinachake apa, Ine sindinapeze mwayi wojambula izo Lamlungu lapitalo koteri ine ndinajambula apa ndekha pa pepala lachikasu ili. Ine ndikuzifuna izo koteri inu mukhoza kuzilemba izo ndipo inu mukhoza kuona chimene ine ndikutanthauza, tsopano, inu muli ndi mapensulo anu. Tsopano, *ili* ndi thupi; ndipo *iyi* ndi solo; ndipo *uwu* ndi (chilembo chachikulu M-z-i-m-u) Mzimu, Mzimu Woyera. Chabwino. Tsopano, ndicho chimene ife tinapangidwa nacho.

<sup>211</sup> Ngati inu mungazindikire cha *kuno*, malo oyera, Oyeretsetsa a oyera; *apa* guwa, malo oyera; ndi *apa* nyanja—nyanja, ndi kumene inu mumamva Mawu, “Chikhulupiriro chimadza pa kumva, kumva Mawu,” kulekanitsa, nyanja ya kulekanitsa, nyanja yolekanitsa. Tsopano zindikirani izi. Tsopano, pali khomo limodzi lokha loti mulowere *umu*, ndipo ndiko kuti mukuyenera kubwera *kuno* poyamba. Ndi kulondola uko?

<sup>212</sup> Tsopano, ine ndikanakoknda ndikanakhala ndi malo, ndikanakhoza kuyika *apa*, “a—anamwali.” Pamene a...A “Mgonero wa Ukwati,” wina. Mukuona momwe bambo *uyu* analowera muno pa Mgonero wa Chikwati, ndipo iye anabwera mwa njira inayake? *Apa* panali Khomolo. Yesu anati, “Ine ndine Khomo.” Ndipo tebulo laukwati ili linali *apa* ndipo anthu onse atakhala mozungulira, ndipo apa panali mwamuna mmodzi kuno yemwe analibe Chovala cha Ukwati. Ndipo pamene Mfumu inalowa, Iye anati, “Kodi wafika bwanji muno, mzanga? Unalowa bwanji muno?” Zinasonyeza kuti iye sanalowera pa Khomo ili. Iye analowera pa zenera kapena kubwera njira ya kumbuyo, kapena kudzera mu kachikhulupiriro kena kapena chipembedzo. Iye sanabwere kudzera pa Khomo!

<sup>213</sup> Chifukwa ku madera akum’ mawa iwo akadali ndi chinthu chomwecho, mkwati yemwe ati akwatire, iye amapereka kuitana ndipo amapereka mwinjiro kwa aliyense yemwe waitanidwa.

<sup>214</sup> Oh, momwe mtima wanga umazungulirira ndi kuzungulira ine ndikaganizira zimenezo! “Palibe munthu angakhoze kudza kwa Ine pokhapokha Atate Anga atamuitana iye poyamba, ndipo onse omwe Atate andipatsa Ine adzabwera kwa Ine.” Kodi ife tinaitanidwa bwanji? Asanayikidwe maziko a dziko mayina athu anayikidwa pa Bukhu la Moyo la Mwanawankhosa, kuti tikawone Kuwala, kuti tilandire Mzimu Woyera, kuti tiyende mu Iwo. Mayina athu (pamene Mwanawankhosa ankaphedwa) anayikidwa pa Bukhu nthawi yomweyo Dzina la Mwanawankhosa linayikidwa mmenemo. Baibulo, ife tifika kwa izo pakapita kanthawi, linati, “iye ananyenga onse pa dziko lapansi amene mayina awo sanalembedwe mu Bukhu la Moyo la Mwanawankhosa chikhazikitsireni maziko a dziko lapansi.”

<sup>215</sup> Zindikirani, ndiye ngati iye...mkwati iyemwini, pamene ine anayima pa khomo. Ndipo munthuyo anabweretsa kuyitanako, anati, “Ndi uku apa.”

<sup>216</sup> “Zikomo inu.” Iye ankatenga kuyitanako, nakuyika iko pansu apa, ndipo ankamuveka iye mwinjiro kuti iwo onse awoneke mofanana. Ine ndikuzikonda zimenezo! Mukuona? Mu mphamvu ya Mulungu, mu Mpingo wa Mulungu wamoyo, olemera, osauka, ansinga, afulu, akuda, oyerera, abulauni, achikasu, onse amawoneka ofanana pakuti iwo avekedwa ndi Mphamvu yomweyo ya Mzimu Woyera. Mukuona?

Tsopano, izo zinkasonyeza kuti iye sanadzere pa Khomo.

<sup>217</sup> Tsopano, zindikirani apa. Oh, ngati munthu ayesera kupita mu malo Oyerera a oyeretsetsa (winawake, mphunzitsi wina wa Baibulo andiuze ine), ngati winawake anayamba kulowa mu malo Oyeretsetsa a oyerera awa popanda kudzera *apa*, iye ankafa. Mwana wa Aroni anatenga moto wachirendo tsiku lina, moto wina wachipembedzo (pamene Iwo siunali moto wachipembedzo), ndipo iwo anafera pakhomo. Ndi kulondola

uko? Kapena ana a Eli anali, ine ndikukhulupirira. Ana a Eli anawatenga iwo mkati, pamene iwo ankayimira ana a Aroni amene anali wansembe.

<sup>218</sup> Tsopano, tsopano, pali njira imodzi yolowera mu thupilo. Kodi thupi ili limalamulidwa bwanji? Tsopano, penyani mwatcheru kwenikweni tsopano ndipo inu mukonzekere mapensulo anu. *Apa* pali chipata pa mbali iyi chimene chimalowa mu thupi: wani, thuu, firii, foro, faivi. Tsopano, inu mwachijambula icho? Tsopano, chipata choyamba cha *apa* ndi: kuwona, kununkhiza, kumva, ndi kulawa, ndi kukhudza kapena kumverera (kaya chirichonse chomwe chikufuna kukhala, ziribe kanthu). Tsopano, izo ndi zokhudzira mu thupi. Ndi kulondola uko? Ndi angati akudziwa zimenezo? Zokhudzira sikisi zimalamulira thupi. Tsopano, ife tiri nayo solo inu mukatha kudutsa mu *izi*. Zokhudzirazi ziri kunjja, ndiko kachitidwe kakunja.

<sup>219</sup> Tsopano, mkati *umu* muli wani, thuu, firii, foro, faivi, zikhumbo faivi mu solo. Tsopano, inu mukufuna kuti muzilembe izo? Choyamba ndi kulingalira, malingaliro. Chachiwiri ndi chikumbumtima. Ndipo chachitatu ndi chikumbutso. Ndipo chachinayi ndi kuganiza. Ndipo chachisanu ndi chikondi.

<sup>220</sup> Tsopano, kodi inu munazimvetsa izo zonse? Ngati inu simunatero, ndiye ndidziwitseni ine tsopano. Inu mwazilemba izo zonse? Kuwona, kulawa, kukhudza, kununkhiza, ndi kumva; thupi, ndizo zolowera ku thupi.

<sup>221</sup> Solo ndi malingaliro, chikumbumtima, chikumbutso, kuganiza, ndi chikondi, ndi zokhudzira kapena zikhumbo, monga zokhudzira za solo. Ndipo solo ndi chikhalidwe cha mzimu umene uli mkati, chifukwa solo imangotulutsa chikhalidwe cha zomwe ziri mkati mwanu. Iyo imatenga malo a kuyeretsedwa, solo ili, imakhala mu gulu lomwelo pamenepo. Chabwino, tsopano, aliynse. . . aliynse wazilemba zimenezo? Chabwino.

<sup>222</sup> Tsopano, ku chipata *ichi* pali chimodzi chokha, chipata chimodzi, chimene chimatchedwa “chifuniro chawekha.” Inu ndinu bwana wa chomwe chimalowa mmenemo. Ndipo kodi icho chimachita chiyani? Ichi ndi chiyani? *Thupi* liyenera kutsukidwa, mphikawo; woyeretsedwa, *apa*; wodzazidwa ndi Mzimu Woyera, *apa*, ndipo ichi chimakhala mpando wa chiweruzo cha Mulungu kachiwiri, pamene Mulungu amakhala mu mtima mwanu, ndipo ngati inu mwachita chinachake cholakwika, nenani, “Ooh, mai, ine ndalakwitsa.”

<sup>223</sup> Anthu ena amati, “Izo sizimanditsutsa ine ku—kukhala ndi tsitsi lalifupi,” akazi. “Izo sizimanditsutsa ine kuti ndizivala zodzikongoletsera kapena zopakapaka, kapena chirichonse chomwe chiri. Izo sizimanditsutsa ine kupita ku zovina. Izo sizimanditsutsa ine kunena bodza laling’ono loyera. Izo

sizimanditsutsa ine kusewera juga mu phwando langa la juga.” Inu mukudziwa chifukwa chake? Inu mulibe kanthu koti kakutsutseni. “Zimenezo sizikupweteka chikumbumtima changa.” Inu mulibe nkomwe chikumbumtima kuposa monga momwe njoka ilibe chiuno. Kotero inu basi... Inu mulibe chikumbumtima, mulibe kanthu pamenepo koti kakupwetekeni inu. Ndinu a dziko lapansi!

<sup>224</sup> Koma ine ndikukutsutsani inu kuti mumulole Yesu Khristu abwere mkati *umu* ndi kuyesera kuti muchite izo kenanso! M'bale, inu mudzakhala wotsutsidwa kwambiri inu mudzabwerera m'mbuyo ndi kugwedeza mutu wanu kwa chinthu chimenecho motsimikiza basi monga ine ndaima pano, chifukwa Iye ndi woyera. Mvetserani, ndikubwereza Lemba, “Ngati inu muzikonda zinthu izo zomwe ziri dziko, zinthu za mdziko, ndi chifukwa chikondi cha Mulungu sichiri ngakhale mwa inu.”

<sup>225</sup> Kodi zinatheka bwanji? Chifuniro chawekha. Inu mukuchitchula bwanji icho ‘chifuniro chawekha,’ M'bale Branham?” Chifukwa icho chimamubwezeretsa mwamuna ndi mkazi basi monga Adamu ndi Eva mmunda wa Edeni. Pa chiyani? Mitengo iwiri! Chifuniro chawekha, *iyi* ndi imfa. *Uwu* ndi Moyo, chifuniro chawekha. Wachiwerewere... Ufulu wakusankha! Mulungu anamuyika munthu woyamba, Adamu ndi Eva, pompano pa ufulu wakusankha. Amakuyikani inu malo omwewo. Ndipo njira yokhayo yomwe mungakonzere chinthu ichi *umu* ndi chifuniro chanokha. Aleluya! Chifuniro chanokha! Muyenere kufuna kuchita chifuniro cha Mulungu. Muyenere kuchotsa chifuniro chanu kuti mulole Chifuniro cha Mulungu chibweremo, chifukwa *iyi* ndi njira yokhayo yomwe imatsogolera ku mtima.

<sup>226</sup> Oh, inu mukhoza kujowina mpingo, inu Abaptisti ndi Apresbateria. Ndipo inu Amethodisti ndi a Pilgrim Holiness mukhoza kubwera ku kuyeretsedwa. Koma inu muyenera kuti mufune kuti muchite Chifuniro cha Mulungu, chifuniro chanokha, kuti mulole Mzimu Woyera ubwere *umu*, kuti ubale. “Zizindikiro izi zidzawatsata iwo amene akhulupirira. Mu Dzina Langa iwo adzatulutsa ziwanda. Iwo *adzayankhula* ndi malirime atsopano. Iwo adzayika manja awo pa odwala kapena kutenga zinthu zakupha, ndi zina zotero. Zizindikiro izi zidzawatsata iwo amene alola chifuniro chawo kukhala Chifuniro Changa, ndipo ntchito zimene Ine ndikuchita iwonso adzazichita.” Ine ndikuyembekeza inu simuchiphonya Ichu. Pali chifuniro cha kuchita Chifuniro cha Mulungu. Inu mukuona chimene ine ndikutanthauza?

<sup>227</sup> Yang'anani apa, ndikuyankhula za malo opatulika, mphika. *Apa* pali nyali, zoyikapo nyali (wani, thuu, firii, foro, faivi, sikisi, seveni), iliyonse ya izo ili nako kuwala. Kodi zikukupeza kuti kuwala kwawo? Kodi Kuwala kwawo kukunyezimiritsidwa kuti,

kodi Iko kukunyezimiritsa kuti? Izo sizikunyezimiritsa apa mu ngodya pa chipembedzo china. Kukunyezimiritsa kumbuyo kuno ku Mawu! Ndi madzi olekanitsa. Fyuu!

<sup>228</sup> “Kwa kulapa ndi chikhululukiwo cha machimo” (Luka 24:49) “ayenera kulalikiidwa mu Dzina Lake kwa mafuko onse, kuyambira ku Yerusalemu.” Kodi kulapa ndi kukhululukidwa kwa machimo kunkaphunzitsidwa motani ku Yerusalemu? Mpaka kuti? Ndi zoti zipite kudziko lonse lapansi. “Lapani inu,” Petro anati, mu Machitidwe 2:38, “ndipo mubatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhululukiwo cha tchimo lanu.” Uthenga umenewo ndi woti upite ku dziko lonse lapansi, ndiyeno mapeto adzafika. Ndiye mapeto adzakhala, Uthenga *wu* ukadzapita ku dziko lonse.

<sup>229</sup> Motani, zoyikapo nyali izi apa zikunyezimiritsa kuwala cha apa pa chipembedzo china cha Methodist, Presbateria, kapena Chipentekoste? Chabwino, ndithudi ayi!

<sup>230</sup> Zikunyezimiritsa mkati *umu* ngati “INE NDINE,” osati “Ine ndinali.” Osati anthu atatu kapena anayi osiyana, koma Mulungu atakhala mmenemo akudzinyezimiritsa Yekha kwa uliwonse wa mipingo imeneyo. Yang’anani mmbuyo umo ndi kuwona zomwe iwo anachita (ife tangobwera kudutsa mu mbiriyakale), iwo ankanyezimiritsa Iye monga Iye analiri, monga Iye aliri, ndi monga Iye nthawizonse ati adzakhali.

<sup>231</sup> “Iye amene anali...” Mwansanga pamene Yohane anangowona koyamba za Izo, iye anati, “Iye Amene Anali, Amene Ali, ndipo Adzadza, Mulungu Wamphamvuzonse, chiregedwe cha Mulungu, Alefa, Omega, Chiyambi ndi Mapeto.” Ndiko Kuwala koono koyenera kunyezimiritsidwa. Kodi inu mukukuona Iko? Ameni! Fyuu!

<sup>232</sup> Itadutsa thwelovu koloko, ndipo ine—ndinapeza... Mvetserani, tiyeni tingofulumira kuti inu mukhoze kuzilemba izo. Ine ndimangodana ndi kukusungani inu nthawi yayitali, koma ine sindikudziwa kuti ndidzakuwonaninso liti. Mwaona? Ndipo ine ndikufuna kuti inu mumvetse izi, abwenzi, uwu ndi Moyo. Tsopano, penyani, ine sindikutanthauza chifukwa ine ndikuzinena Izo. Ngati ine—ngati ine ndikuwonetsera moteromo...ndiye ndine...inu—inu simumaumvetsa mtima wanga. ine sindikuyesera kunyezimiritsa “Oh, izi ndi basi... Inu si kanthu.” Ine sindikuyesera kuchita zimenezo. Ngati inu simunalandire Kuwala, ine ndikuyesera kukulozerani inu ku Kumodzi pano. Osati m’modzi apa pa guwa ili, Mmodzi apo pa Mpandowachifumu umenewo. Ndipo Mpandowachifumu umenewo ukuyenera kukhala mu mtima mwanu, ndiye inu mudzawona ndendende chinthu chomwecho monga mmene chikunyezimiritsidwa apa.

<sup>233</sup> *Ichi* ndi chiyani pamwamba apa? Izo zikunyezimiritsa *Ichi*. Ndipo *ichi* ndi Ichi, Mawu. Kutsukidwa ndi madzi a

Mawu, ndi Mawu; kutsukidwa (kudzera mu madzi olekanitsa) kuchokera ku zinthu za dziko—dziko, mwa Mawu. Mawu amati Iye ali yemweyo dzulo ndi kwanthawizonse. Iwo siamati, “Iye ali yemweyo mu m’badwo wa Chipentekoste, mmbuyo mwa ophunzira, ndiyeno m’badwo wotsatira Iye anasintha.” Ayi, Iye ndi yemweyo! Mukuona? Inu simungakhoze kuwapanga Iwo kunena china chakenso. Ife tikhoza kungokhala pa chimodzi cha zinthu zimenezo kwa maora, koma ine ndikuyembekeza kuti inu mukuchimvetsa Icho tsopano. Mulungu wakuyitanani inu, inu muchimvetsa Icho. Ndi zomwe ine ndikukhulupirira. Chabwino, bwana.

<sup>234</sup> Tsopano, ndi chiyani icho? Kulungamitsidwa, kuyeretsedwa, ubatizo wa Mzimu Woyera; solo, thupi, mzimu; zonse chimodzimidzi. Tsopano, nyaliyo ikunyezimiritsa Mawu. Mawu owona amanyezimiritsa chiyani? Kodi nyali iyi ikanatani, ngati iyo ikanamatenga chinyezimiro chake kuchokera ku Ulemelero wa Shekina uwu? Iyo ikananyezimiritsa Ulemerero wa Shekina. Ndi kulondola uko?

<sup>235</sup> Ngati inu munakutenga mu seminare, kuwala kwanu, inu mudzanyezimiritsa seminare. Inu munakutenga iko mu seminare ya Methodisti, inu mudzanyezimiritsa Chimethodisti. Inu mumanyezimiritsa! Ngati inu munakutenga iko mu seminare ya Chipentekoste, inu munyezimiritsa Chipentekoste. Koma ngati inu munakutenga Iko mu Ulemerero wa Mulungu, pa chitsamba choyaka . . .

<sup>236</sup> Bwanji, pamene Mose anatuluka mu Kukhalapo Kwake, iye ankachita kuyika chinachake pa nkhope yake, kotero, kuti anthu asakhoze nkomwe kuyang’ana pa iye. Ndi kulondola uko? Iye anali wodzala ndi mphamvu ya Mulungu.

<sup>237</sup> Stefano, mwamuna wodzazidwa ndi Mzimu Woyera. Akuyesera kumuletsa iye, bwanji, zinali ngati kuyesa kuzimitsa nyumba pa tsiku lamphepo, mu moto; kuzimitsa motowo pa iyo . . . ndipo nyumbayo ili pa moto pa tsiku lamphepo. Oh, mochuluka iwo—mochuluka momwe iwo ankawukupiza iwo, ndi momwe zinkayipirayipira. Bwanji, inu simukanakhoza kumuletsa iye. Molunjika, pamene iwo anamuyika iye pa Bwalo lamilandu la Akulu, Baibulo linati, “Iye anayima pamenepo, ankawoneka ngati mngelo.”

<sup>238</sup> Tsopano, ine sindikuganiza “mngelo” ankangotanthawuza kuti iye anali Munthu winawake atayima pamenepo; koma, mngelo amadziwa bwino lomwe zomwe iye akunena. Momwemonso amachitira mngelo aliynse, mnthenga wa m’badwo wa Mpingo, samasowa kuti abwerere ndi kukawona zomwe seminare ikuganiza. Iye amadziwa zimene Mulungu ananena mu Baibulo Lake, ndi mphamvu yomwe ikunyezimiritsa kuti itsimikizire kuti Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Iye sakuopa, iye akunena ndendende

basi zomwe iye akudziwa kuti ndi Choonadi. Ndipo Mulungu atayima pamenepo akuchiyimira Icho kumbuyo ndi mtundu womwewo wa zizindikiro ndi zodabwitsa, ndipo ndi Mawu omwewo. Ameneyo ndi mngelo!

<sup>239</sup> Stefano anayima pamenepo, anati, “Ine ndikudziwa zomwe ine ndikunena.” Anati, “Inu owuma makosi ndi osadulidwa mu mtima ndi makutu, inu nthawizonse mumakaniza Mzimu Woyera. Momwe atate anu anachitira, inunso mukuchita!” Anati, “Ndani wa makolo anu amene sanaphe aneneri ndipo kenako nkuwamangira manda awo?”

<sup>240</sup> Inu zipembedzo, ndi ndani wa inu amene sanachite chinthu chomwecho? Mukuona? Kumanga nyumba zazikulu zokhala ndi mipanda yoyera ndi nyumba zosungiramo mitembo ndi zinthu kuzungulira kuno, ndipo kenako nkumayankhula za Mulungu! Ndinu nomwe amene munamuyika Iye mu nyumba zosungiramo mitembo, ndinu nomwe amene munamuyika Iye m’manda. Ndicho chinthu chomwecho chimene chinamuyika Iye m’manda kumbuyo uko, chinali tchalitchi chachikulu choyera, chipembedzo, Afarisi ndi Asaduki amene anamuyika Iye mmenemo ndipo kenako nkumayesera kuti amange chikumbutso kwa Icho.

<sup>241</sup> Ndiloleni ndikuuzeni kuti Khristu ndi Munthu wamoyo. Iye si chinachake chimene chinafa, Iye ndi Chinachake chimene “chinauka *kwa* akufa, ndipo ali moyo kwanthawizonse.” Oh, m’bale! Ndithudi! Kodi zimachita chiyani? Izo zimanyezimiritsa chiyani? Izo zikunyezimiritsa kuchokera *apa*, chingakhale chiyani icho? Chingakhale ku-...Kodi chinyezimiritsa chenicheni cha Iye ndi chiyani? Ndiye chinthu choyamba chimene chikanati chinyezimiritse, chikanakhala Dzina Lake. Ndi kulondola uko? Izo zikananyezimiritsa Dzina Lake. Chinthu chotsatira kunyezimiritsa, ingakhale mphamvu Yake. Mukuona chimene ine ndikutanthauza? Izo zikananyezimiritsa chirichonse chimene Iye ali.

<sup>242</sup> Koteru ngati *izi* zikunyezimiritsa ku m’badwo uwu *apa*, chirichonse chimene Iye anali, ndiye Iye ali yemweyo! Fyuu, ulemerero! Ulemerero! Ndi chiyani icho? Ndi kumunyezimiritsa Iye monga Iye anali, monga Iye ali, monga Iye adzakhala ali nthawizonse, chifukwa izo zikubwera molunjika kuchokera ku Mpandowachifumu wa Mulungu; Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse; Mulungu yemweyo, Mphamvu yomweyo, Ulemerero womwewo, chirichonse chomwecho. Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Oh, m’bale!

<sup>243</sup> Tiyeni tingopitirira pang’ono chabe. Tsopano, tiyeni titenge ndime yonse ya 6 iyi apa, ya mutu wa 4. Ine ndiri nazo ndemanga zina ndazilemba apa pa zimenezo, ndipo ine ndikufuna kuti ndifulumire ndi kufikako ngati ine ndingathe. Tsopano, a—yonseyo, mukasiya mutu uwu-...tikasiya ndime iyi, izo basi

zimangozungulira mophweka, kunena zomwe iwo anachita. Tiyeni tione ngati ife tingadutse pamenepo.

...*mandala*...*nyanja ya mandala*...(Tsopano, ife tikudziwa chomwe icho chinali.) *pakati pa mpandowachifumu*,...Zorengedwa zamoyo *zinayi, zirombo*...

<sup>244</sup> Tsopano, tsopano, ndi angati ali ndi Baibulo lokonzedwanso? Mu lanu lokonzedwanso, ilo limati “Zorengedwa zamoyo.” Chabwino, ine ndinadabwa kuti King James uyu apa ananena kuti zamoyo...zinali zinayi “*zirombo*”? Chabwino, ine ndinadzipezera la Chigriki—dikishonale ya Chigriki, ndi kubwerera mu dikishonale ya Baibulo ndi kukapeza chomwe izo zinkatanthauza. Tsopano, ichi ndi chomwe icho chiri. Tsopano, zindikirani mwatcheru. Mawu wotanthawuziridwa apa, tsopano inu muwalembe iwo kuti mukhoza kukawayang’ana iwo, inunso, kuti mukhale otsimikiza. Mwaona, ine ndikufuna inu mulembe zimene ine ndikunena, ndipo...ngati inu mungathe ndipo mukufuna. Chabwino, Baibulo lokonzedwanso limati, “Zorengedwa zamoyo,” mu ilo. Tsopano, penyani:

*Ndipo...apo...panali zirombo zinayi zodzala ndi maso kutsogolo ndi kumbuyo.*

<sup>245</sup> Ndipo limapitirira ndi kulongosola za “zirombozo,” zimene ife tifikako mu miniti. Tsopano, *chirombo* apa chikuyimiridwa. Kodi inu muli nazo zowerenga za m’mphepete mu Baibulo lanu, pa—pa *zirombo*? Ngati muli nazo, mupite ku zowerenga za m’mphepete. Ine ndikuzindikira Dokotala Scofield apa wazilemba izo mu lake. *Zirombo* zikutanthauza, iye wafika apa, akuti, “Zorengedwa zamoyo.” Oh, mai! Tsopano, penyani. Mawu a Chigriki muli, “Z, ma o awiri, m”...kapena, “Z, ma o awiri, n” izo ndi, “Z, ma o awiri, n.” Tsopano, mu—mu Chigriki, icho chimatchedwa Zoon kutanthauza “Chorengedwa.”

<sup>246</sup> Tsopano, siziri choncho...ngati inu mukufuna kuti muwerenge izo tsopano. Ife tiribe nthawi. Ine ndikanati ndiwerenge izo, koma sindinawerenge. Lembani Chivumbulutso 11, 13, ndi 17. Tsopano, apo pamene *chirombo* chiri, mitu mu Chivumbulutso 11, 13, ndi 17, chikutchedwa *zirombo* mwanjira yomweyo; koma *zirombo* pamenepo, kutanthauzira kuli “t-h-e-r-i-o-n,” therion. Mawuwo, mawu a Chigriki *therion*, omwe amatanthauza “*chirombo* chakuthengo, chosawetedwa.” *Therion*, izo zikutanthauza “*chirombo* chakuthengo, chosawetedwa.”

<sup>247</sup> Koma Zoon amatanthauza “Chorengedwa,” onani, “Zorengedwa zinayi (Zoon) zamoyo.” Osati *zirombo* za “zakuthengo,” *therion*; koma, “Zoon, Zorengedwa zamoyo.”

<sup>248</sup> Ndipo *therion* ndi “zakuthengo, zosawetedwa zolusa.” Mwanjira ina, ngati inu mungawone mutu wa 11, “*chirombo* cha Roma.” Mutu wa 13, “United States.” Mutu wa 17, “zonse United



States ndi Roma,” wa mipingo ya zipembedzo zophatikizidwa ndi Chikatolika zimawapangitsa iwo kukhala osatembenuka, osawetedwa ku Uthenga. Fyuu! Zosawetedwa!

<sup>249</sup> “Mulungu adalitsike, ife tikuchokera ku mpingo wawukulu wa Methodisti, wa Baptisti, wa Presbateria, chipembedzo cha Chipentekoste. Ife tikudziwa zomwe tikuyankhula! Palibe amene amatsogolera... angatiuze ife!” Ndi inu apo. Osawetedwa! Osatembenuka! Opanda chikondi chachibadwidwe! Ophwanya mapangano! Oneneza mwabodza! Osadziletsa! Ndipo onyoza iwo amene ali abwino! Okhala nawo mawonekedwe a . . .

<sup>250</sup> [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.]... kudutsa izo tsopano. Ndipo ine ndikanakonda kungochikhadzula chinthucho mzidutswa pakali pano, koma ine... kotero izo zifika pa tepi iyi, mulimonse. Koma tiribe nthawi yoti tichite izo. Tsopano, inu mukumvetsa. Ndi angati akumvetsa? Nenani “Ameni.” [Osonkhana akuti, “Ameni.”] Mwaona, awa ali . . .

<sup>251</sup> Kodi *Zoon*, Z-ma o awiri-n ndi chiyani? Zorengedwa zamoyo. Iwo akhoza kutchulidwa *Zoon*, Z, ma o awiri, n. Kodi inu mungawatchule bwanji iwo, “Zoon”? “Zoon,” ndingatero.

<sup>252</sup> Ndipo *therion* ndi t-h-e-r-i-o-n, *therion*, mwaona. Kotero iwo amatanthauza “zirombo zosawetedwa, zakuthengo, zolusa.” Ndi zomwe zirombo ziri... Inu tengani yanu... tengani dikishonale yanu ya Chigriki ndi kubwerera m’mbuyo ndi kuwona ngati amenewo si mawu omwewo. Inu mukayang’ane mmenemo ndi kuwaona iwo. Tengani yanu—tengani bukhu lanu la chigriki, tengani Emphatic Diaglott yanu. Tsopano, fufuzani ngati izo siziri zoon, kuti izo ndi zoon, kuti iwo amatanthauza “chirombo chosawetedwa,” mu Chivumbulutso 11, 13, ndi—ndi 17.

<sup>253</sup> Ndipo apa mu Chivumbulutso 4, iwo amatanthauza “Chorengedwa chamoyo,” osati *chirombo*; koma chimatchedwa “chirombo” koma sichoncho. Chinthu chomwecho mu Ezekieli 1:8, 1 mpaka :28, izo ziri. Mwinamwake tifika ku zimenezo mu miniti.

Chabwino, “Chirombo chowetedwa, chosatembenuka, chakuthengo.” Chosawetedwa!

<sup>254</sup> Koma *izi* ndi “Zorengedwa zamoyo.” Ndi chiyani izo? Iwo si Angelo. Ine ndikukuuzani chiyani, tiyeni tiwerenge mu Chivumbulutso 5, kudutsa tsambalo. Chivumbulutso 5, ndime ya 11:

*Ndipo ine ndinawona, ndipo... ndinamva liwu la angelo ambiri (“angelo,” ambiri) kuzungulira mpandowachifumuwo (“Ndipo” ndi mlumikizi.) ndipo zirombo ndi... akulu: . . .*

255 Onani, “ndipo,” mlumikizi. Mukuona? Iwo sanali Angelo, ngakhalenso iwo sanali akulu, izo zinali “Zorengedwa zamoyo” pa Mpandowachifumu. Oh, kodi inu simukuzikonda izi? Zorengedwa Zamoyo! Iwo si Angelo, chifukwa izi zikutsimikizira izo pomwe apa, mwawona:

. . . *Ine ndinaona, ndipo . . . ndinamva liwu la angelo ambiri pozungulira mpandowachifumu ndi zirombo ndi akulu: . . .*

256 Tsopano pali magulu atatu osiyana apa. Ine ndikuyembekeza inu nonse muli ndi kachitidwe aka kuno tsopano. Tsopano, ine ndikufuna kuti ndikusonyezeni inu. Pali magulu atatu osiyana a iwo, mitundu itatu yosiyana (Tsopano, penyani.) kuzungulira Mpandowachifumu.

257 *Apa* pali Mpandowachifumu. Tsopano, choyamba pa Mpandowachifumu uwu ndi Zorengedwa zamoyo zinayi. Kunja kwa izo kuli akulu twente-foro (basi monga *choncho*) akulu atakhala pa mpandowachifumu, pa yawo—mipando yawo yachifumu, mipando yachifumu yaying’ono pansu. Ndipo mozungulira izi, pali makamu aakulu a Angelo atazungulira Mpandowachifumu. Mukuona chimene ine ndikutanthauza? Aliyense ndi wosiyana, wina kwa mzake. *Pali* Angelo; *apa* pali akulu; ndipo *apa* pali Zorengedwa zamoyo.

258 Tiyeni tisazisiye izo kwa miniti. Tiyeni tingozigwira pamenepo kwa miniti, “Zorengedwa zamoyo.” Kodi iwo ndi chiyani ngati iwo siali Angelo, iwo si anthu owomboledwa? Iwo ndi chiyani? Kodi inu mukufuna kudziwa? Uku ndi kutanthauzira kwanga. Ndikukhulupirira kuti ndi kolondola; Ine ndikukhulupirira iko kuli. Iwo ndi alonda a Mulungu a Mpandowachifumu Wake. Tsopano, ife tifufuta izi pang’ono pokha. Tsopano, inu mukuona, iwo ali—iwo si Angelo kapena anthu. Iwo si zirombo zakuthengo. Iwo ndi Zorengedwa, “Zorengedwa zamoyo.”

259 Tsopano, *apa* pali Mpandowachifumu wa Mulungu. Ndipo *awa* ndi alonda Ake. Tiyeni tiwerenge pang’ono chabe za izo ndi kupeza mu maminiti pang’ono. Mwaona, iwo ndi Angelo a Mulungu kapena alonda a Mulungu a Mpandowachifumu Wake, ndipo iwo. . . Tiyeni titenge. . . basi—miniti yokha kachiwiri, tiyeni ife tibwerere kwa Ezekieli. Ine—ine ndazilemba zinthu izi apa, ndipo ine ndikudana nazo kuti ndizilambalale izo, ine ndikudziwa kuti izi ndi a. . . [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.] Tiyeni tibwerere ku Ezekieli mutu wa 1, ndipo tiyeni tiyambire ndi ndime ya 12 mpaka 17, miniti yokha.

*Ndipo iwo anayenda m’modzi aliyense molunjika kutsogolo: . . .*

260 Tsopano, ife tiyang’ana mu maminiti pang’ono. . . Ndipo inu mukukumbukira ndime ya 7 iyi apa, tsopano, yang’anani

momwe izo zinkawonekera apa mu ndime ya 7 ya mutu womwewo wa Chivumbulutso, “zinayizo.”

*Ndipo chirombo choyamba chinali ngati mkango, . . . chirombo chachiwiri chinali ngati mwana wa ng’ombe, . . . chirombo chachitatu chinali nkhope. . . chinali. . . ya munthu, ndipo zirombo zinayizo zinali zonga. . . mphungu zowuluka. . . chirombo chachinayi. . . ngati mphungu yowuluka.*

<sup>261</sup> Tsopano, pamene Ezekieli anawona Ulemerero wa Mulungu, iye anawona chinthu chomwecho chimene Yohane anachiwona. Inu mukukumbukira Lamlungu lapitalo momwe ife tinawupezera “Ulemerero wa Mulungu,” ndipo munachipeza chithunzi chimene Iye anachijambula limodzi nafe? Inu mukukumbukira zimenezo? “Ulemerero wa Mulungu,” chinthu chomwecho chimene Ezekieli anachiwona, chinthu chomwecho Yohane anachiwona, apa Icho chiri lero. Zimampanga Yesu Khristu kukhala yemweyo mu nthawi ya Ezekieli, chinthu chomwecho chinali pano padziko lapansi, Mulungu yemweyo amene ali pano ndi ife lero; yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse; Iye Amene Anali, Amene Ali, ndipo Adzabwera; khomo lolowera mu solo, thupi, ndi mzimu; nyanja yamkuwa (Mawu), Woyeretsa wa solo yathu, ndi Wodzazitsa nawo Mzimu Woyera. Chinthu chomwecho, mwaona, chimodzimodzi basi!

<sup>262</sup> Tsopano penyani izi. Chabwino:

*. . . ndipo mzimu. . . kulikonse komwe izo zinkapita; . . . tsopano. . . kupita, izo zinkapita; ndipo izo sizinkatembenuka pamene izo zinkapita.*

<sup>263</sup> Izo sizinkatembenuka. Ngati izo zikamapita njira *iyi*, izo zinkapita ngati munthu; kupita njira *iyi*, zinkapita ngati mphungu; kupita njira *iyi*, zinkapita ngati ng’ombe; kupita njira *iyi*, zinkapita ngati mkango. Izo sazinkabwerera m’mbuyo! Izo zinkayenera kupita patsogolo kulikonse kumene zinkapita, chirichonse cha zirombozo. Tsopano, kodi *chirombo* chimatanthauza chiyani mu Baibulo? Mphamvu. Chabwino, chimatanthauza “mphamvu.”

<sup>264</sup> Tsopano:

*Mwa maonekedwe a zorengedwa zamoyozo ndi maonekedwe awo anali ngati makala oyaka moto, ndi monga. . . za. . . maonekedwe a nyali: inkayenda pamwamba ndi pansu pakati pa zorengedwa zamoyozo; ndipo motowo unali wowala, ndipo kuchokera mu motowo munatuluka kuwala.*

Ameneyo ndiye Mulungu. Kuchokera mu moto munatuluka Kuwala; osati kuwala kwa dziko, tsopano, Kuwala Kwamuyaya.

*Ndipo zorengedwa zamoyozo zinathamanga ndi kutembenuka (Tiyeni tione.) . . . zorengedwa zamoyozo zinathamanga ndi kubwerera, ndi monga maonekedwe a kuthwanima kwa mphezi.*

*Ndipo pamene ndinapenya zorengedwa zamoyozo, taonani, gudumu limodzi padziko lapansi pafupi ndi zorengedwa zamoyozo, ndi nkhope zake zinayi.*

*Mawonekedwe a magudumuwo . . . ntchito zawo zinali ngati . . . mtundu wa . . . beryl: ndipo zinayi zimenezo zinali ndi chifaniziro chimodzi: ndipo maonekedwe awo ndi ntchito zawo zinali . . . zinali gudumu mkati mwa gudumu.*

265 “Ndi chizindikiro cha chiyani apa, M’bale Branham? Ndi chiyani icho?” Zikutanthauza kuti alonda awa—Alonda awa anali likasa la Mulungu . . . Iwo anali paulendo, akugudubuzika pa magudumu pamene Ezekieli anawawona iwo; koma pamene Yohane anawawona iwo, iwo anali atafika kale mu malo awo oyenera Kumwamba. Likasa la Mulungu linali pa dziko lapansi, likugudubuzika pa magudumu, pamene iwo analinyamula ilo kuchoka ku malo kupita ku malo, zinkatanthauza kuti linali paulendo, iwo analitenga ilo njira yonse kudutsa m’chipululu ndi njira yonse mpaka kukalowa mu kachisi ndi zina zotero; koma tsopano ilo lalandiridwa m’mwamba chifukwa m’badwo wa Mpingo watha, ndipo ilo lalandiridwa m’mwamba mu Ulemerero. Mukuona? Ilo lakhazikika tsopano, Kumwamba, ndi Angelo onse ndi zinthu zitalizungulira ilo. Ife tikuwapeza iwo patapita kanthawi akuvula akorona awo ndi kugwetsa nkhope zawo pansu ndi kupereka ulemerero kwa Iye. Mukuona? Iwo anali alonda a Mulungu a kachisi, a likasa.

266 Tsopano, kumbukirani alonda a Mulungu a likasa, kapena mpando wachifundo. Tsopano, kumbukirani. Kwa zochuluka bwanji, Yohane anaziwona, zingati? Zinayi. Ndi zingati zimene—zimene *iye* anazona? Iye anawona zinayi, nayenso, Zorengedwa zamoyo zinayi. Tsopano, penyani, iwo onse anaona masomphenya omwewo.

267 Ndipo foro ndi nambala ya dziko lapansi. Kodi inu mumadziwa zimenezo? Ndi angati akudziwa tsopano ife tisanalowe mu zimenezo, *foro* ndi nambala ya padziko lapansi? Ndithudi! Monga Achihebri foro . . . Ndi a dziko- . . . Ndi nambala ya dziko lapansi, ya “kuwomboledwa, chiwombolo.” Tsopano, muzisunge izo mu malingaliro anu, “chiwombolo,” chifukwa ine ndizikhudza izo, miniti yokha, molimba kwenikweni. Onani, “Chiwombolo!” Tsopano, panali ana atatu Achihebri mu ng’anjo ya moto, koma Mmodzi wachiforo anabwera, icho chinali chiwombolo. Lazaro anali m’manda masiku atatu, koma pamene lachiforo linadza iye anawomboledwa. *Foro* ndi nambala ya Mulungu ya

“chiwombolo,” kotero izo zinkasonyeza kuti Zorengedwa zimenezi ziyenera kuti zinali chinachake pa dziko lapansi.

268 Ine ndikuyembekeza kuti simukumva njala kwambiri tsopano. Ine ndikuyembekeza kuti chilakolako chanu chauzimu chiri pang’ono—choposera pang’ono chachirengedwe chanu tsopano. Mukuona? Chabwino.

269 Tsopano, zindikirani, “Izo ziri nawo maso” (mu Ezekieli umu apa) “kutsogolo ndi kumbuyo ndi mkati.” Tiyeni tingowerenga izo. Yang’anani apa, mwaona. Mukuwona mkati umu, ndikukhulupirira iwo amayankhula kudutsa pano, “zirombo,” nkhope zinayi, ngati mphungu, ndi mapiko, zodzala ndi maso kunjja, mkati. Yang’anani apa:

*Ndipo zirombo zinayizo ndi chirichonse cha izo chinali ndi mapiko sikisi pomuzungulira iye; . . .*

270 “Ndipo izo zinkawuluka,” ndi zina zotero, “ndipo zinali nawo maso kunjja, mkati ndi kumbuyo.” Izo zinkayankhula za nzeru zawo. Iwo ankadziwa chimene chinali, chimene chiri, ndi chimene chiri mkudza; pakuti iwo anali pa Mpando pomwe, pafupi kwambiri mpaka iwo sianali nkomwe anthu. Alonda a kachisi, kapena, osati alonda a kachisi (Alonda a kachisi, handiredi forte foro sauzande.), Koma uyu ndi mlonda wa mpando wa chifundo, alonda a Mphandowachifumu, Mpandowachifumu, pafupi ndi Mulungu, “Zorengedwa zamoyo,” chinthu chotsatira kwa Mulungu, zitayima pamenepo. Nzeru zawo, iwo amadziwa chimene chinali, chimene chiri, chimene chiri mkudza. Iwo anali nawo “maso kunjja,” kusonyeza zomwe iwo anakhoza kuziona, zomwe zinali mkudza; “maso mkati,” amadziwa zonse tsopano; ndi “maso kumbuyo,” amene ankadziwa chomwe chinali. Chimene chinali, chimene chiri, chimene chiri mkudza, kunyezimiritsa kudutsa mu mibadwo ya mpingo “Iye Amene Anali, Amene Ali, ndi Ali Mkudza; Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.”

271 Zigwireni izo tsopano. Tichipititsa chinthu chimenecho mpaka pa bolodi mu mphindi zochepe. Penyani izo. Tsopano, miniti yokha.

272 Zimawulula nzeru zawo, ndipo izo zinasonyeza kuti iwo ankadziwa, amadziwa. Iwo ankadziwa zonse zamtsogolo ndi zatsopano ndi zam’mbuyo, ndi zonse za izo!

273 Ndipo awo. . . Iwo anali osatopa. Iwo sanatope konse. Iwo sangakhale chirichonse cholumikizana ndi munthu, iye amatopa. Koma iwo sankatopa, iwo ankayimba “Woyera, woyera, woyera! Woyera, woyera, woyera! Woyera, woyera, woyera, Ambuye Mulungu Wamphamvuzonse! Woyera, woyera, woyera!” usana wonse ndi usiku wonse kudutsa m’badwo uliwonse. “Woyera!”

274 Tiyeni tibwerere m’mbuyo miniti yokha. Tiyeni tibwerere m’mbuyo, ine ndiri nalo Lemba mu malingaliro, Yesaya

6, mwamsanga ndithu. Penyani! Yesaya anawona chinthu chomwecho ndendende basi.

<sup>275</sup> Masomphenya aliwonse a Ambuye...Ndi zomwe ine ndikunena. Ngati masomphenya omwe tiri nawo lero siali ndendende masomphenya a Baibulo, ndiye iwo ndi olakwika. Ngati iwo amanyezimiritsa, kapena, vumbulutso lililonse limene limamuwonetsa Mulungu chirichonse kupatula chimene Iye nthawizonse anali, ndi vumbulutso lolakwika. Mpingo wonse wamangidwa pa ilo, Mateyu 17.

<sup>276</sup> Tiyeni tiwone, Yesaya, mutu wa 6. Mneneri wachinyamata ameneyu anali atatsamira pa mikono ya mfumu yabwinoyo, ndipo anali atamugulira iye mitundu yonse ya zovala zabwino. Ndipo iye anali mneneri, ndipo iye ankatsatira paliponse... Koma tsiku lina mfumuyo inafa, kotero iye anayenera kuti—iye anayenera kuti asunthe yekha. Kotero iye anapita ku kachisi kukapemphera. Chifukwa iye anayamba kutuluka pakati pa malo a mfumu kumeneko, ndiye, kuti apeze a...Mfumu yabwino yokalambayo inali munthu wabwino woyera. Koma iye anatuluka nawona mmene anthuwo anali kukhalira, kotero iye anatsikira mu kachisi. Tsopano, mvetsarani.

*Mu chaka chimene mfumu Uziya anafa, ndinaonanso Ambuye atakhala pa mpandowachifumu, wapamwamba ndi wokwezedwa, ndi mwinjiro wake unadzaza kachisi.*

<sup>277</sup> Ulemerero! Ndi chiyani “mwinjiro Wake”? Ndi zimenezotu, “Angelo, Zamoyo,” mwinjiro Wake zimene zinamutsatira Iye. Mwinjiro ndi umene umabwera kumbuyo, mukuona?

*...mwinjiro wake unadzaza kachisi.*

*Ndipo pamwamba pake panayima aserafi: ndipo yense wa iwo anali nawo mapiko sikisi; ndi awiri anaphimba nkhope yake, ...ndi awiri anaphimba mapazi ake, ndipo ndi awiri anawulukira.*

*Ndipo wina anafuulira kwa mzake, ndipo anati, Woyera, woyera, woyera, ndi AMBUYE wa makamu: dziko lonse ladzala ndi...ulemerero.*

*Ndipo pamene mizati ya zitseko inagwedezeka ndi mawu a wofuulayo, ndipo nyumbayo inadzaza ndi utsi.*

<sup>278</sup> Mai! Oh, mai! Izo zikusonyeza kuti masomphenya awo ali chimodzimidzi basi kwa mmodzi aliyense wa amuna amenewo. “Woyera, woyera, woyera!” Iwo samatopa, usana ndi usiku, “Woyera, woyera, woyera, kwa Ambuye!”

<sup>279</sup> Tiyeni tibwerere m’mbuyo miniti yokha tsopano, kuti tikhale otsimikiza kuti tawapeza anthu awa molondola. Nthawi yoyamba imene alonda awa anatchulidwa, ndi mu Genesis. Tsopano, kumbukirani, chirichonse chimene ife timalalikira chiyenera kuchokera ku Genesis mpaka ku Chivumbulutso.

Nthawi iliyonse yomwe mukufuna kuti muzifunsa, bwerani mudzandifunse. Mukuona? Ilo liyenera kukhala Baibulo lonse, osati gawo chabe la ilo, chifukwa Mulungu samasintha! Chimene Iye anali mu Genesis, Iye ali lero, ndipo Iye anali mu m'badwo wapakati. Iye nthawi zonse ali yemweyo! Mukuona? Tsopano, mu Genesis, pamene Akerubi awa. . . Umo ndi momwe ndimawapezera iwo, Ine ndinayenera kubwerera kuti ndikafufuze zomwe zinali pachiyambi.

<sup>280</sup> Tiyeni titembenuzire ku Genesis 3:24, kwa mphindi yokha tsopano. Genesis, mutu wa 3 ndi ndime ya 24. Inu mukuzikonda Izo? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] Chabwino. Tsopano, tiyeni tiyambire cha pa ndime ya 22. Ine—ine ndimangozikonda Izi! Ichi ndichinthu chomwe ine ndikungofuna kuti ndichiyike apa, kungwonjezera pang'ono, koma chikhoza kudzachita bwino kwambiri tsiku lina.

*Ndipo AMBUYE . . . anati, Taonani, munthuyo  
wakhala . . . mmodzi wa ife, . . .*

<sup>281</sup> Tsopano, alongo anga okonda ndi ofunika ndi okonedwa (Ndiloleni ine ndiziyike izo monga choncho.), musaganize kuti ndikupereka chithunzithunzi pa—kukhulupirika ndi yachisomo, ngale yamtengo wapatali ya ukazi. Ine ndikuyesera kusonyeza apa chimene mkazi. . . Chonde! Ndipo kwa inu pa tepi, akazi inu amene mudzakhala mukumvetsera ku tepi iyi, ine sindikuyesera kuti ndikunyozeni inu, Ndine chabe wantchito wa Ambuye kuti ndibweretse Kuwala. Chinthu chotsikitsitsa ndi chopanda khalidwe komanso chonyansa kwambiri padziko lapansi ndi mkazi pamene ali woyipa. Ndipo ngale yamtengo wapatali imene ilipo kwa mwamuna, pambali pa chipulumutso chake, ndi mkazi wabwino. Ndipo ine ndikuyankhula kwa otsika, a makhalidwe oyipa, otsitsidwa. Ndipo ine ndikuwonetsani pomwe pano pamene ife tikadali pomwepo, ndikhoza basi kukuwonetsani chifukwa kuti ine. . . kuti Baibulo limaphunzitsa kuti akazi asakhale alaliki, abusa, aphunzitsi, kapena china chirichonse mu mpingo. Tsopano, tangomvetserani ku ichi:

*Ndipo AMBUYE . . . anati, Taonani, mwamunayo  
wasandulika . . . mmodzi wa ife, (Tsopano, Iye sananene  
kuti mkaziyo wasandulika mmodzi, “mwamunayo  
wasandulika mmodzi.”) . . . ndipo akudziwa chabwino  
ndi choyipa: . . . (Mkaziyo sanatero; iye ananyengedwa.  
Kodi inu mukuziona izo?)*

<sup>282</sup> Tsopano, Paulo anati, “Ine sindilola kuti mkazi aphunzitse kapena kutenga ulamuliro uliwonse, koma. . . pakuti Adamu anapangidwa koyamba ndipo kenako Eva. Ndipo Adamu sananyengedwe, koma mkaziyo ananyengedwa.” Kotero iye sanasandulike mmodzi wa Mulungu. Iye sankadziwa kusiyana kulikonse, iye ananyengedwa. Kodi inu mukuzimvetisa izo? Ngati

inu mukutero, nenani “Ameni,” kotero ine . . . [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.]

. . . *AMBUYE* . . . *anati, Taonani, munthuyo wasandulika. . . mmodzi wa ife, kudziwa chabwino ndi choyipa: ndipo akudziwa. . . ndipo tsopano, kuti iye asayike dzanja lake, nakatenganso za mtengo wa moyo, ndi kudya, ndi kukhala moyo kosatha:*

*Chotero AMBUYE. . . anamutumiza iye kuchoka m'munda wa Edeni kuti akalime nthaka komwe iye anatengedwako.*

*Kotero iye anamuthamangitsa munthuyo; ndipo iye anaika kummawa kwa munda wa Edeni Akerubi, ndi lupanga lowuluka. . . lupanga lamoto limene limagtembenuka mbali iliyonse, (Mukuona zirombo zinayi? Pali mbali zinayi zokha zomwe inu mungakhoze kupita, mwaona: kummawa, kumpoto, kumadzulo, ndi kummwera. Akerubi awa anali ndi lupanga lamoto pa chipata cha mundawo. . . ) kuti asunge njira ya mtengo wa moyo.*

<sup>283</sup> Chifukwa ngati munthu angawugwire konse Mtengo wa Moyowo, ndiye iye angakhoze kukhala moyo kwanthawizonse.

<sup>284</sup> Ndipo Akerubi awa, kutchulidwa koyamba, anayikidwa pa chipata cha kummawa kwa munda, kupita njira zinayi. Ine ndikanazipanga izo mosiyana pang'ono ndi zimenezo; Ine sindingakhoze kuchita mwachilungamo ku dongosolo la Mulungu ndi zinthu monga choncho, koma ine—ine basi. . . kotero kuti inu mukadziwe chimene ine ndikutanthauza. *Apa pali* munda wa Edeni. Ndipo ichi ndi chipata *apa* pomwe, chimatseguka apa, chimalendewera kunja, ndipo pa chipata ichi panali Akerubi. Akerubi! Ndipo, kumbukirani, silimanena kuti “Mkerubi,” ilo linati “Akerubi.” Akerubi anayikidwa pamenepo kuti aziyang'anira chiyani? Mtengo wa Moyo. Ndicho chimene iwo anali oti azichiyang'anira, Njira ya ku Mtengo wa Moyo. Njira, kodi Njira ndi Ndani? [M'bale akuti, “Yesu.”—Mkonzi.] Kodi zikunyezimiritsidwa kuchokera kuti? *Apa* pali malo oyera, *apa* pali Akerubi.

<sup>285</sup> Tsopano, penyani, lembani zonse izi. *Apa* pali Oyera—Oyera. . . malo Oyeretsetsa a oyera awa, Oyera a oyera, *awa* ndi malo oyera, ndipo *apa* pali nyanja, ndipo *apa* pali nyali zowala, seveni zomwe zikunyezimiritsa Kuwala kuchokera *apa*, mkati *umu*, mkati *umu*, mkati *umu*, mkati *umu*, mkati *umu*, mkati *umu*. Mwaona? Kodi izo zikunyezimiritsa chiyani? Izo zikuyang'anira ndi kunyezimiritsa ndi moto wa Mulungu Njira ya ku Mtengo wa Moyo. Mwaona, izo sizingabwere kuchokera *kuno*, seminale ya Presbateria kapena seminare ya Chipentekoste, izo ziyenera kubwera kuchokera *Apa*, kunyezimiritsa Kuwala. Chabwino.



286 Inu mukuzindikira, awa—Akerubi awa amene Yohane anawawona apa amayenera kukhala achidwi kusunga Mtengo wa Moyo, kotero iwo ayenera kukhala ndi chidwi ndi anthu okhalapo. Kapena werengani Genesis, kubwereranso ku Genesis, “Iwo ankasunga Mtengo wa Moyo, ankawuyang’anira Iwo, Njira ya Moyo.” Njira ya Moyo! Kodi Njirayo ili motani? Yesu anati, “Ine ndine Njira imeneyo. Ine ndine Mkate umene umadza kuchokera kwa Mulungu kuchoka Kumwamba. Ngati munthu adya Mkate uwu, iye adzakhala moyo kwanthawizonse.” Tsopano pali njira yobwerera ku Mtengo wa Moyo umenewo. Inu mukumvetsa zimenezo?

287 Tsopano, pa izi, ine ndikufuna kusonyeza tsopano ndi kutsimikizira izi: ndi guwa. Tsopano, ili liyenera kuti linali guwa la mmunda wa Edeni. Ndikuwuzani chifukwa chake. Kodi inu mukukumbukira onse awiri Kaini ndi Abele anabwera apa kuti adzapembedze? Kotero izo zikusonyeza kuti guwa la nsembe la Mulungu linasunthidwa ndi kudzayikidwa apa mmunda wa Edeni, ndipo njira yokhayo yobwererera ku Edeni ndi mwa guwa. Ndi inu pano kachiwiri, mwaona, kubwerera ku Edeni kudzera pa guwa. Ndipo iwo ankayenera kuti asunge njira imeneyo uko, kuyiyang’anira iyo, kuti iwo asakhoze kubwerera kumeneko mpaka guwa ili litadzazidwa ndi magazi.

288 O Mulungu, kodi anthu sangathe kuziona izo? Mwaona, palibe kanthu koma Magazi! Payenera kuti pakhale chitetezero, mpando wachifundo pamenepo, guwa ili la chiweruzo liyenera kusandulika mpando wachifundo; ndipo pamene guwa ili, ngati Magazi achotsedwapo, padzaima pa Tsiku la chiweruzo limenelo moto wa mkwiyo wa Mulungu kuti uyang’anire Mtengowo kachiwiri. Chinthu chimodzi chokha chimene chidzalowa mu chipata ichi cha Edeni kachiwiri, chidzakhala kupyolera mu Magazi a Yesu Khristu. Inu mukuziona izo?

289 Tsopano, zindikirani. Eya, tsopano Kaini. . . Oh, *apa pali* Kaini; ndipo *apa pali* Abele, Abele. Chabwino. Tsopano, anyamata onsewo anabwera pa chipata ichi kuti adzapembedze. Ndi kulondola uko? Kotero liyenera kuti linali guwa la Mulungu. Ndi kulondola uko? Ndipo patsogolo pa guwa ili iwo anamanga choloweza mmalo, guwa lina. *Apa pali* guwa loona la Mulungu, liri mu mtima wa munthu. Ndiye pali guwa lina pansu *apa*, lomwe linali kuyimira malo Oyeretsetsa a oyera mu malo oyera.

290 Oh! Oh! Ine ndikumverera ngati ndiyankhule ndi malirime. Oh, mai, Ulemerero wa. . . Kodi inu simungathe kuchiwona Icho ndi changwiro? Tangozindikirani! Oh, chifukwa chimene ine ndinanenera zimenezo, chifukwa ine sindingakhoze kupeza mawu okwanira mu chinenero changa cha Chingerezi kuti ndifotokoze kumverera kwanga. Mwaona, chinachake chiyenera kufotokoza.

291 Monga M’bale Rowe, kazembe wa Purezidenti. . . pafupifupi

ma Purezidenti foro kapena faivi osiyana, iye anati, “Oh, M’bale Branham, usiku wina ine ndinabwera ku msonkhano.” Iye anati, “Ine sindinkadziwa choti ndichite,” iye anati, “Ine ndinayima kunjira uko.” Ndipo iye anati, “Oh,” anati, “Ine ndawakonda Ambuye moyo wanga wonse.” Iye anati, “Ine ndakhala a” (Ndikuganiza) “Episcopalian.” Iye anati, “Ndipo ine ndimaganiza ine ndimamudziwa Ambuye.” Iye anati, “Ndipo usiku wina ndinayang’ana pozungulira, ine sindinkadziwa choti ndichite.” Anati, “Ine—ine sindingapite mkatimo pachabe, koma” anati, “Ine ndinawamva Mawu akubwera. Oh, Iwo anayamba kubwera.” Iye anati, “Ine ndinayamba kuyenda chokwera ndi chotsika kunjira kwa hema, ndikuyenda kumbuyo ndi kutsogolo,” ndipo anati “molunjika ine sindinadikire kuti ndifike pakhomo, Ine ndinakwawira pansa pa icho pamene kuyitanira paguwa kunapangidwa, ndipo ndinathamangira ku guwa ndipo ndinagwa pansa, ndinati, ‘Ambuye, ndine wochimwa!’” Ndipo anati, “Kenako Iye anandidzadza ine ndi Mzimu Wake Woyera.”

<sup>292</sup> Ndipo anati, “Ine ndikhoza kuyankhula ziyankhulo eyiti zosiyana,” chifukwa iye ndi kazembe. Mukuona? Iye ndi a... iye ali mu... iye—iye ndi a—kazembe kwa Purezidenti, ndipo... njira yonse kuchokera ku Woodrow Wilson kutsika. Iye ndi kazembe kwa aliyense wa Purezidenti wathu, kazembe wakunja, akhoza kuyankhula chiyankhulo chirichonse chakunja. Iye anati, “Ndimadziwa bwino lomwe chiyankhulo chirichonse cholembedwa mu dziko lonse lapansi.” Koma anati, “Ndinali wodzaza ndi ulemerero sindikanatha kugwiritsa ntchito chirichonse cha izo kuti ndimutamande Iye, kotero Ambuye andipatsa ine chatsopano kuchokera Kumwamba kuti ndimutamande nacho Iye.” Oh! Ooh! Ndi zimenezotu.

<sup>293</sup> “Kuyang’anira chipata ichi.” Kaini ndi Abele anabwera apa kuti adzapembedze. Kotero liyenera kuti linali guwa lansembe limene iwo ankaliyang’anira. Ndi kulondola uko, Akerubi awa?

<sup>294</sup> Chinthu china, zindikirani apa pali umboni wina. Kaini... Penyani Baibulo tsopano! Ine ndikanati inu mutembenezire ku ilo, koma izo... musadandaule, inu muzipeza mu Genesis. Chabwino, penyani. Kaini anatuluka, Kaini anatuluka mu Kukhalapo kwa Ambuye pachipata cha mmunda. Kotero Kukhalapo kwa Ambuye kuyenera kuti kunali pa guwa, ndipo guwalo linali pa chipata. Ulemerero! Oh! Chabwino. Ndi malo okhalapo Mulungu, pa guwa Lake. Tsopano, Kaini anachoka mu Kukhalapo kwa Ambuye, kuchokera pa malo awa. Inu mukufuna kuzilemba izo? Genesis 4:16, ngati inu mukufuna kuzilemba izo. Tsopano, tsopano, inu muli nazo zonse izo, inu mwatero, mwazilemba?

<sup>295</sup> Tsopano, ine ndiri ndi chinachake chimene ndikufuna kuti ndichijambule apa miniti yokha. Ine ndikuyembekezera kuti nyemba zanu sizipserera, kapena chirichonse pa yanu...

Tsopano, zindikirani. . . Zisiyeni izo zipserere, izo ziri bwino, izo zidzawonongeka mulimonse. Tiyeni—tiyeni tiganize za apa, ichi ndi—ichi ndiye chinthu chimene chiri—chiri chenicheni.

<sup>296</sup> Mose anatengedwa kupita Kumwamba, Mose, anatengedwa kuchokera pa dziko lapansi kupita Kumwamba ndipo analiwona guwa la Mulungu. Ndi kulondola uko? Ndikuyesera kutsimikizira mfundo yanga apa. Inu mukudziwa zomwe ndikuyesera kuchita, sichoncho inu? Chabwino. Iye anapita m'mwamba mu Kukhalapo kwa Mulungu. Ndipo pamene iye anatsika kuchokera mu Kukhalapo kwa Mulungu, iye anati, Mo-. . . Mulungu anamuwuzwa Mose, “Panga chirichonse pa dziko lapansi monga chifanane ndi Kumwamba.” Ndi kulondola uko? Chabwino.

<sup>297</sup> Tsopano, ndiye pamene iye anatero, pamene iye anapanga Likasa la Pangano, iye anayika Akerubi awiri kuti aziyang'anira likasalo. Mukuona chomwe icho chiri? Anali a kachisi. . . anali a guwa, oyang'anira Mpandowachifumu. Akerubi awiri, Iye anati “Awumbeni iwo kuchokera ku mkuwa ndi kuwayikira mapiko awo ogundana monga *chonchi*,” chifukwa ndizo ndendende zomwe iye anaziwona Kumwamba.

<sup>298</sup> Ndizo ndendende zomwe Yohane anaziwona Kumwamba, Akerubi foro awa pa mbali foro za likasa la Mpandowachifumu Kumwamba. Iwo anali alonda a likasa. Akerubi, alonda pa mpando wachifundo.

<sup>299</sup> Ngati inu mukufuna kuti muwerenge Lemba limenelo (ife tiribe nthawi yoti tipite kwa ilo), lembani Eksodo 25:10 mpaka 22.

<sup>300</sup> Tsopano, iwo amayang'anira mpando wachifundo pamene Mulungu ali mu Ulemelero Wake wa Shekinah. Kodi Ulemerero wa Shekina unali kuti? Pa mpando wachifundo. Ndi kulondola uko? Iwo amalondera Ulemelero wa Shekina uwo. Hmm! Fyuu! Mvetserani, abwenzi! Ndiye izo zimasonyeza kuti wopulikira aliyense sangakhoze kubwera kumeneko ndi kutenga za Izo. Inu muyenera kukhala wokonzeka musanabwere mu Kukhalapo kwa Iwo.

<sup>301</sup> Yang'anani pa Aroni, mwa choyimira. M'mbuyomu. . . Tsopano, kumbukirani, osonkhana mu masiku amenewo sankakhoza ngakhale kuwuyandikira iwo mwanjira iliyonse. Koma pamene Aroni analowa mkati. . . Ndi kangati komwe iye anafika kuti alowe mu Iwo? Kamodzi pachaka. Iye ankachita motani. . .? Iye ankayenera kuti avale zovala zinazake, zinkapangidwa ndi manja enaake, mtundu wachirendo wa zovala. Iye ankayenera kuvala mwa njira yoteroyo. Iye anali ndi mkangaza ndi belu, lomwe nthawi iliyonse akamayenda limasewera “Woyera, woyera, woyera, kwa Ambuye.” Iye anali akuyandikira mpando wachifundo, ali ndi magazi.

<sup>302</sup> Ndipo iye ankayenera kuti adzozedwe ndi mafuta enaake, onunkhiritidwa ndi zonunkhiritisa zina zopangidwa kuchokera ku rozi la Sharoni. Ndipo Yesu anali Duwa la Sharoni limenelo. Ndipo, zindikirani, duwa ndi chinthu chokongola, liri ndi zonunkhiritisa mmenemo. Koma zonunkhiritisazo zisanatuluke, duwalo limayenera kuti lisinjidwe, ndiyeno zonunkhiritisazo zimafinyidwa kuchokera mu duwalo. Yesu, mu moyo Wake, munali moyo wokongola kwambiri umene unakhalapo; koma Iye sakanatha kukhala mwanjira imeneyo, chifukwa Iye ankayenera kuti audzoze Mpingo Wake (kuti ufikire Chiyero Chake), kotero moyo Wake unafinyidwira kunja. Ndipo Mzimu Woyera womwewo umene unali pa Iye wayikidwa pa Mpingo, ndipo Iye akumupanga Iye yemweyo dzulo, ndi lero, ndi nthawizonse, Rozi la Sharoni, zonunkhiritisa mmenemo. Munthu amene akuyandikira mu malo Oyeretsetsa a oyera awa ayenera kudzozedwa ndi Mzimu Woyera womwewo. Ndipo pamene iye akuyenda, “Woyera, woyera, woyera, kwa...” (Osati ndi ndudu mkamwa mwake.) “Woyera!” (Osati ndi kolala yake yotembenezidwa.) “Woyera, woyera, woyera,” atavekedwa mu chiyero cha Yesu Khristu. Hmm! Ndinu wodabwitsa bwanji! Oh!

<sup>303</sup> Tsopano, “mpando wachifundo.” Tsopano, mpando wachifundo uli mu mtima, mpando kumene kunyezimira kwa Wake—Ulemerero Wake mwa ana Ake onse, Ulemerero wa Shekinah mu mtima wa munthu. *Apa* pali mtima wa munthu. Ndi kulondola uko? Ndi mpando wachifundo umenewo? Kodi mumabwera bwanji kudutsa mu izo kulowa mwa Iwo kudzera mu kachitidwe kosiyana aka? Kudzera mu chifuniro chanokha, chifuniro chanokha. Mumalowa mkati *umu*, ndipo kudzera *mnenemo*, mumatuluka *chiyani*? Ulemerero wa Shekinah. Chani—kodi Ulemerero wa Shekina ndi chiyani? Ndi Kukhalapo kwa Mulungu. Ndipo pamene mwamuna akuyenda, kapena mkazi, iye akunyezimiritsa Ulemerero wa Shekinah. Iye samapita mmapanga a juga ndi—ndi kumapitirira, ndi kupita kunja kuno ndi kumakana Mawu. Ziribe kanthu zomwe anthu anena, iye wakhazikitsa mtima wake pa chinthu chimodzi: Mulungu. Ndipo ngati iye wayitanidwa mowona ndi Mulungu ndiye Yesu Khristu amadzinyezimiritsa Yekha kudzera mwa iye ndi Ulemerero wa Shekinah, kuchita zinthu zomwezo Iye ankazichita kumbuyo uko; kuwonetsera Uthenga womwewo, kulalikirira Mawu omwewo, Mawu omwewo akuwonetseredwa mu muyeso womwewo unali pa nthawiyo, monga momwe zinaliri mowona pa Pentekoste izo zinayesedwanso kachiwiri. Oh, mai!

<sup>304</sup> “Mpando wachifundo.” Ezekieli ndi Yohane onse anawona zinthu zofanana. Tsopano, zindikirani, tsopano ife tiri pafupi kuti tifike kumapeto, basi pang’ono pokha. Tsopano, apa ndi pamene ine ndikufuna kuti inu mumvetse chinachake. Oh, chonde musachiphonye icho! Tsopano, ndi angati akudziwa

kuti Akerubi amenewo anali *Zorengedwa zamoyo* ndipo osati ziroombo? Izo zinali. . . dongosolo lapamwamba.

<sup>305</sup> Tsopano, kodi Mngelo ndi dongosolo lapamwamba kuposa a munthu kapena dongosolo lapansi? Chabwino, bwana. Wamkulu ndi ndani, mwana wa Mulungu kapena Mngelo? Mwana wa Mulungu! Ndani amene Mulungu angamumve bwino kwambiri, Mngelo atayima pamenepo pamaso pa Iye akuchonderera chinachake, kapena mmodzi wa inu nonse akuchonderera? Mmodzi wa inu nonse! Mwaona, chifukwa ndinu ana aamuna ndi aakazi. Iwo—iwo ndi antchito. Mwaona? Iwo ndi antchito, ndipo inu ndinu ana aamuna ndi aakazi. Kotero onani ulamuliro womwe muli nawo, ife timangochita mantha chabe kuwugwiritsa ntchito iwo.

<sup>306</sup> Tsopano, ine ndikufuna kuti inu muzindikire apa, izi ndi zokongola. Oh, mai! Ndiloleni ine ndifike apa ndi kudumphazina za izi kuti ine ndifike ku izi. Tengani mapensulo anu tsopano, izi ndi zomwe ine ndimafuna kwenikweni kuti inu mujambule. [M'bale Branham ajambula pa bolodi—Mkonzi.] Mwinamwake ine kulibwino ndichichepetseko pang'ono. Tsopano, Israeli mu ulendo wawo, pamene iwo anamanga msasa, tsopano penyani ichi mwacheru, iwo anamanga msasa: wani, thuu, firii, foro. (Ayi, ndikukhulupirira ndikulakwitsa.) Wani, thuu, firii; wani, thuu, firii; wani, thuu, firii; wani, thuu, firii; wani, thuu, firii; ndimo mmene iwo anamangira misasa mozungulira mpando wachifundo. Tsopano, ine ndikudziwa, nonse inu mukudziwa zimenezo, inu munapenya ndi kuziwerenga mu Chipangano Chakale.

<sup>307</sup> Tsopano, ku mbali ya kummawa, mbali ya kummawa, pomwe *apa*, ine ndizilemba izo kuti inu mutsimikize kuti mwazimvetisa izo. Kummawa, mbali ya kummawa inali nthawi zonse Yuda. Ichi ndi chipata, J-u-d-a, Yuda. Ndipo ndi Yuda. . . anali mutu wa mafuko atatu ndi mbendera yawo; mafuko atatu ndi mbendera yawo, mbendera ya Yuda. Inu mukukumbukira. . . Ndi angati anawona *Malamulo Khumi*, *Malamulo Khumi* a Cecil DeMille? Chabwino. Kapena, inu munaziwerenga izo pomwe apa mu Lemba, mu Lemba uko, kani, pamenepo panali Yuda kumbali ya kummawa. Chabwino.

<sup>308</sup> Ku mbali ya kumadzulo, kumusi *uku*, (Tsopano inu muzilembe izo, inu mukuwerenga izo molondola. . . ndi pa Eksodo, ndi zina zotero, pamene iwo ankatuluka.) anali Efraimu, E-p-h. Ndipo iye anali ndi mafuko atatu ndi mbendera yawo. Chabwino, Efraimu.

<sup>309</sup> Tsopano, ndipo ku mbali ya kummwera kunali Rubeni, R-u-b, ndi mafuko atatu, ndi mbendera yawo.

<sup>310</sup> Ndipo ku mbali ya kumpoto kunali Dani, Dani ndi mafuko atatu, ndi mafuko atatu ndi mbendera yawo. Chabwino.

<sup>311</sup> Tsopano, umo ndi momwe iwo anamangira misasa. Tsopano, kumbukirani, tiyeni tiwerenge tsopano mu Lemba tsopano kotero kuti ife timvetse izi ndendende basi. Ndiyambira mmbuyo pa ndime ya 7:

*Ndipo chi . . . chirombocho chinkafanana ndi mkango, ndipo chachiwiri . . . chinkafanana ndi mwana wa ng'ombe, (ng'ombe yaying'ono) ndipo chirombo chachitatu chinali ngati nkhope ya munthu, ndi zirombo zinayi zinali . . . ndipo . . . chirombo chachinayi chinali ngati mphungu yowuluka.*

*Ndipo zirombo zinayizo chirichonse chinali nawo mapiko sikisi pa iye; ndipo izo zinali zodzala ndi maso mkati: ndipo izo sizimapumula usana ndi usiku, kunena, Woyera, woyera, . . . Ambuye Mulungu Wamphamvuzonse, amene analipo, amene ali, ndipo adzabwera.*

*Ndipo pamene zirombo izi zinapereka ulemelero ndi ulemu ndi kuyamika kwa iye wokhala pa mpandowachifumu, amene ali wamoyo kwa nthawi za nthawi,*

*Akulu foro ndi twente anagwa pansi pamaso pa iye wokhala pa mpandowachifumu, ndipo anampembedza iye wokhala moyo kwanthawi za nthawi, ndipo anaponyera akorona awo—anaponyera akorona awo patsogolo pa mpandowachifumu, akunena,*

*Inu ndinu woyenera, O Ambuye, kulandira ulemmerero . . . ulemu . . . mphamvu: pakuti inu mwalenga zinthu zonse, ndipo mwa kusangalatsidwa kwanu izo ziri . . . zinarengedwa.*

<sup>312</sup> Tsopano, tsopano, inu penyani. Ku mbali ya kummawa—mbali ya kummawa, iye anawona nkhope ya mtundu wanji? Ngati inu mungazindikire, iwo unali mkango, m-k-a-n-g-o, imeneyo inali mbenderayo. Icho chinali—imeneyo inali mbendera yokhazikika ya Yuda. Chifukwa Iye ali . . . Yesu anachoka pa . . . Zoona! Ndipo Iye ndi Mkango wa fuko la Yuda.

<sup>313</sup> Tsopano, ndi angati anayamba awonapo zodiaki? Ambiri a inu mukudziwa chomwe icho chiri: nyenyezi. Mukuona? Limenelo linali Baibulo loyamba la Mulungu. Tsopano, kodi izo zimayambira pa chiyani, nambala yoyamba mu zodiaki, chithunzi choyamba? Ndi namwali! Ndi kulondola uko? Ndipo chomaliza ndi chiyani? Leo, mkango. Kudza Koyamba ndi Kudza Kwachiwiri kwa Khristu, zonse kudzera pamenepo. Iwo amatenga khansa yosakaniza . . . kapena m'badwo wosakaniza ndi kumene unasakaniza nsomba, umene uli m'badwo wa khansa, ndipo ife tikukhala moyo kudutsa mu iwo.

<sup>314</sup> Ndipo zindikirani mu piramidi pamene iye anayimanga iyo, mu nthawi ya Enoki, mwala uliwonse unali mmenemo.

Iwo amakhoza kuziyeza zinthu zimenezo ndendende basi ndi kunena za nkhondo ndi zinthu. Chirichonse ndi chathunthu koma Mwalawapamutu. Bwanji? Inu mukuzindikira pa ndalama yanu ya dollar? Itulutseni iyo ndi kuyang'ana, chovindikiracho chachotsedwa pa iyo. Bwanji? Iyo siyina phimbidwe konse. Khristu ndiye Mwalawapamutu umene unakanidwa, Iye anali Mwalawapamutu wokanidwa. Iye akubweranso posachedwa kwambiri. Penyani momwe Mpingo uwo, kumbuyo komwe mu m'badwo wa Chilutera, wotambalala pansi; ndiye nkukhala apang'ono, apang'ono mochulukira pang'ono, mochulukira pang'ono mpaka iwo atabwera pansi pomwe; Iwo ukachoka mu m'badwo wa Chipentekoste, ndiye umabwera mpaka ku mwala uliwonse kuti ugwirizane mmenemo kuti uyikemo chovindikira chimenecho mmenemo, Mpingo umene udzabweretse Yesu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Mwangwiro basi momwe zingakhoze kukhalira!

Tsopano, Iye anali Mkango wa fuko la Yuda.

<sup>315</sup> Tsopano, aliyense amene anayamba wawerengapo Baibulo amadziwa chomwe nambala ya Dan inali, kapena chimene—chimene Dan. . . Oh, ine ndikutanthauza chiyani, eya, chimene Dan anali? Yake, iye anali mphungu. Uko nkulondola. Iye anali mphungu. Winawake wakhala akuwerenga Baibulo. Iye anali mphungu.

<sup>316</sup> Tsopano, Rubeni anali munthuyo. Iye anali woyamba, wofowoketsetsa wa gululo. Kodi Yakobo sananene choncho mu—mu Genesis 49? “Rubeni, ndiwe woyamba wa mphamvu zanga; koma monga madzi, unakwera pa bedi langa ndi kuyipitsa bedi langa,” ndipo anakhala ndi mdzakazi wa atate wake. Mwaona, ndiwo makhalidwe oyipa a munthu wokhalapo. Inu mukuona? Chinyama sichimakhala ndi makhalidwe oyipa amenewo, mkango, palibe chirichonse cha zinthu izi chiri ndi zmeneizo; koma mwamuna amatero, kumathamanga ndi mkazi wa mwamuna wina ndi zina zotero. Monga ngati. . . Chinthu chomwecho, zonse zamalizidwa.

<sup>317</sup> Tsopano, izi pansi apa, *uyu*, Dani anali mphungu. Ndipo, *uyu*, Rubeni anali nkhope ya munthuyo. Ndipo Efraimu ndiye ng'ombe. Tsopano, inu mwachipeza chithunzicho pamenepo? Efraimu. . . Umo ndi momwe iwo anamangira misasa, mu Baibulo.

<sup>318</sup> Tsopano, ngati inu mungazindikire, Dani ndi mutu wa mafuko atatu, Yuda ndi mutu wa mafuko atatu, Rubeni anali mutu wa mafuko atatu, ndipo Efraimu anali mutu wa mafuko atatu. Mafirii foro ndi thwelovu, mafuko thwelovu a Israeli. Mwaona, aliyense ndi mbendera yake; ndipo mbendera ya Yuda inali mkango; mbendera ya Rubeni, munthu; mbendera ya Efraimu, ng'ombe; mbendera ya—ya—ya Dani inali mphungu.

319 Tsopano, yang'anani mmbuyo apa zomwe Yohane ananena, "Ndipo mmodzi anali nayo nkhope. . ." Tiyeni tiwerenge apa tsopano, tingowona ngati sichiri chinthu chomwecho monga chinali Kumwamba:

*. . .chirombo choyamba chinali ngati mkango, (Yuda) . . .chirombo chachiwiri chinali ngati mwana wa ng'ombe, (ndiyo ng'ombe yaying'ono) . . .chirombo chachitatu chinali nkhope ya munthu, ndipo chirombo chachinayi chinali . . .mphungu yowuluka.*

320 Ndendende basi momwe mafuko a Israeli anamangira misasa mozungulira, kuyang'anira, iwo ndi alonda a padziko lapansi a kumanja kwa likasa. Oh, Aleluya! Kodi simukuziona izo?

321 Apa! Chifundo, m-p-a-n-d-o w-a-c-h-i-f-u-n-d-o, "mpando wachifundo." Palibe chimene chikanakhoza kubwera paliponse mozungulira icho popanda kudutsa mafuko amenewo. Kudutsa chiyani? Mkango; kudutsa munthu, nzeru za munthu; ndi kuwoloka kavalo wantchito, ngati ng'ombe; kapena kuwoloka mphungu, kufulumira kwake. Mukuona? Kumwamba, dziko lapansi, pakati, ndi pozungulira ponse; inu mukuona, iwo anali alonda. Ndipo pamwamba pake panali Lawi la Moto. M'bale, palibe chomwe chinakhudza mpando wachifundo umenewo popanda kuyandikira . . .

322 Ndipo chinthu chokha chimene chikanakhoza kuyandikira iwo chinali kudzera mu magazi. Aroni ankalowa mmenemo kamodzi pachaka ndi magazi. Tsopano inu mukuziona izo? Tsopano, penyani. Mutu uliwonse wa mafuko atatu ukuyang'anira mpando wachifundo, mpando wachifundo wa Chipangano Chakale. Tsopano, kodi inu mwazilemba izo, aliyense? Tsopano, iyi ndi yatsopano, m'bale. Mvetserani kwa izi, ndiye ife tizipita. Tsopano, kumbukirani, awo anali alonda a Chipangano Chakale. Ndi angati anayamba aziwerengapo izo mu Baibulo, inu mukudziwa ngati uko nkulondola? Mwaona, awo ndi alonda a Chipangano Chakale.

323 Tsopano ife tikukhala mu m'badwo wina. Ulemerero! Oh, ine ndimawukonda m'badwo uno! Sichoncho inu? Tsopano, Mulungu ali ndi mpando wachifundo lero kuti uzilonderedwa. Inu mukukhulupirira zimenezo? Kodi mpando wachifundo umapezeka kuti? Mu mtima mwa munthu. Kodi iwo unabwera pati mu mtima wa munthu? Pa Tsiku la Pentekoste pamene Mzimu Woyera (umene uli Mulungu) unabwera mu mtima wa munthu. Ndi kulondola uko? Tsopano, tiyeni tilembe izi apa, ndipo konzekeerani kuzijambula ngati inu mukufuna kutero. Pentekoste, P-e-n-t, ine ndiyika Pentekoste. Uwu ndi mpando wachifundo, Mzimu Woyera. Utayikidwa mkati umu. . .Ine ndikuwuzani chiyani, zipangitseni izo kukhala zoyenera kwambiri, tiyeni tiyike mkati umu "Nkhunda" yomwe



ikutanthauza . . . mbalame, mwawona. Chabwino, kuyang'anira mpando wachifundo, tsopano kodi Mulungu ali nawo alonda a mpando wachifundo lero? Tsopano izo . . . Tsopano, penyani kukongola kwa momwe zajambulidwira.

<sup>324</sup> Ine ndinali nditakhala tsiku lina ndipo ndinawona izi, ndipo ine ndinangolumpha ndi kuthamanga mozungulira ndi kuzungulira ndi kuzungulira mpandowo, ndikunena, "Ulemerero! Ulemerero! Ulemerero! Ulemerero! Ulemerero," kuzungulira, kuzungulira. Charlie, ine ndichita moyipa kuposa momwe ndimachitira ku nkhalango nthawi ina. Mlongo Nellie, ngati ine ndingachite monga choncho, inu mundithamangitsa ine mnyumba mwanu mofulumira kwambiri. Huh? Oh, ine basi ndinali nayo nthawi yaulemerero. Tsopano, penyani chimene icho chinali, chimene Ambuye anachita.

<sup>325</sup> Tsopano, Pentekoste, itachitika Pentekoste, analemba Bukhu la (Chiyani?) Machitidwe a Mzimu Woyera, M-a-c-h-i-t-i-d-w-e. Ndi kulondola uko? Kodi Machitidwe akuyamba ndi chiyani, chinthu choyamba kulowa mu chipulumutso? Machitidwe 2:38. Apa pali chomaliza icho, mozungulira. Ndi kulondola uko? "Iwo onse anadzazidwa ndi Mzimu Woyera ndipo anayamba kuyankhula ndi malirime ena. Ndipo Petro anayimirira, ndipo anawalalikira iwo ulaliki. Iwo anati, 'Kodi ife tingatani? Kodi ife tilowa bwanji mmenemo?' Iye anati, Machitidwe 2:38, 'Lapani, ndipo mubatizidwe aliyense wa inu, Dzina la Yesu Khristu.'"

<sup>326</sup> Tsopano, kumbukirani, Mulungu ali nawo alonda kwa umenewo—kwa mpando wachifundo umenewo. Kodi mpando wachifundo umene iwo amaulondera ndi chiyani? Chabwino. M-a-t-h, Mateyu, kummawa; Luka, Luka; Marko; ndi Yohane. Mauthenga awo onse foro amatsimikizira Bukhu la Machitidwe kuti libwere, iwo amalondera ilo kulikonse kumene inu mukufuna kuliyang'ana ilo.

<sup>327</sup> Tiyeni tingotenga chimodzi, chimodzi chokha, ife tiribe nthawi. Ine ndiri nazo twente kapena kupitirira apo ndazilemba apa, koma tiyeni tingotenga chimodzi pa phunziro ili kwa chipulumutso. Kodi ife tikhala nayo nthawi yoti tipemphere? Ayi, ndi wani koloko, kotero ine ndikuganiza ife sitikhala nayo pokhapokha inu nonse mukufuna kupempherera odwala. Tsopano, ine ndapeza . . . Ndangokhala ndi nthawi yochulukika. Mukuona? Chabwino.

<sup>328</sup> Tsopano, zindikirani izi! Mateyu, Marko, Luka, ndi Yohane, ndi chiyani chimenecho? Nambala yapadziko lapansi, ya Mauthenga, foro. Chabwino, zindikirani.

<sup>329</sup> Tsopano, Mateyu 28:19. 28, tsopano, ndi kumene inu abale a utatu mukupita, 28:19. Chabwino. Mateyu, kumapeto kwa mutuwo, anati, "Pitani inu kotero, kaphunzitseni mafuko onse, kuwabatiza iwo mu Dzina la Atate, Mwana, Mzimu Woyera";

koma apa pakubwera Pentekoste, ndipo Petro anati “Lapani, ndipo mubatizidwe mu Dzina la Yesu.”

<sup>330</sup> Chinachake chalakwika pamenepo. “Mateyu, ndiwe mlonda wa pachipata chakummawa uja?”

<sup>331</sup> Chipatacho chiri motani? Chipatacho ndi chiyani? Yesu. Yesu anati, “Khwala ndilo chipata.” Ndi kulondola uko? Kodi zimalembedwa... Kodi amalembedwa bwanji, s-t-r-a-i-t kapena s-t-r-a-i-g-h-t? *S-t-r-a-i-t* amatanthauza “madzi,” “madzi ndiwo chipata.” Kodi mumalowa bwanji? “Lapani, aliyense wa inu ndi kubatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu,” amatsegula zipatazo. Aye! Fyuu!

<sup>332</sup> “Oh, koma, M’bale Branham, inu muli ndi Mateyu 28:19 pamusi apo.” Ndizo zolondola ndendende. “Koma, Mateyu, kodi ndiwe mlonda kwa icho?”

“Ndithudi, ndine mlonda wathunthu.”

<sup>333</sup> Tsopano pezani Mateyu 1:18 ndi kuwona zomwe akunena, muwone ngati ilo likulondera—kulondera izi. Onani ngati Mateyu 1:18 akulondera Mateyu 1...28 ndi Machitidwe 2:38. Onani ngati iye akulondera izo!

*Tsopano kubadwa kwa Yesu Khristu kunali motere:...*

“Pano pali Mulungu Atate, Mulungu Mwana, Mulungu Mzimu Woyera,” iwo amayesera kunena.

*...kubadwa kwa Yesu Khristu kunali motere: Pamene... amayi ake Mariya anapalidwa ubwenzi ndi Yosefe, asanabwere pamodzi, anapezeka ndi mwana wa Mzimu Woyera.*

Uti? Izo zinawayika iwo onse kukhala Mmodzi!

Ndipo izi zinali...zonse...zinachitika, kuti... Ndipo taonani,...

*Tsopano Yosefe mwamuna wake, pokhala munthu wolungama,...osati mwadala kuti amunyazitse iye poyera, anaganiza zomusiya iye pa chifukwa chimenecho.*

*...taonani, mngelo wa Ambuye, akutsika, anadza pa iye (Inu mukudziwa.) ndipo anati, Yosefe, iwe mwana wa Davide, usaope kudzitengera wekha Mariya mkazi wako: pakuti icho cholandiridwa mwa iye chiri cha Mzimu Woyera. (Mukuona?)*

*Ndipo adzabala mwana wamwamuna,... iwo adzamutcha dzina lake YESU:...*

*Izo zinali...zonse...zinachitika, kuti chikakhoze kukwaniritsidwa...ndi mneneri,...*

*Chomwe, namwali adzayima...(Yesaya 9:6)... namwali adzayima, ndipo...adzabala mwana*

*wamwamuna, ndipo adzamutcha dzina lake...*  
[Osonkhana akuti, “*Emmanueli.*”—Mkonzi.]

<sup>334</sup> Kodi amaulondera iwo? “Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera,” Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera, izi basi: maudindo ku Dzina limodzi limenelo. Kotero mlonda amayima pamenepo kuti ayikire kumbuyo. Inu mukumvetsa izo? Oh, mai! Tsopano, ndi angati akudziwa zimenezo? Ndi izi apa! Iye ndi mlonda.

<sup>335</sup> Tsopano, tiyeni basi... Ine ndiri nalo gulu lonse kwa chipulumutso, titenge ena awa. Koma tsopano ngati ife titi tikhale ndi mzere wa pemphero mu miniti yokha, kwa maminiti teni okha tiyeni tiyese china chakenso apa basi miniti yokha. Tiyeni titenge Malemba ena tsopano. Kodi ndinazilemba kuti izi? Ndi izi apa. Chabwino.

<sup>336</sup> Tsopano tiyeni titenge ndi kuwona ngati Mateyu pamwamba apa tsopano ati azilondera izo kwa machiritso Auzimu. Muli ndi mapensulo anu ndi zinthu tsopano, kuti inu mukuzilemba izi? Chabwino. Onani ngati Mateyu akuzigawa... angazilondere izo. Tiyeni titenge Mateyu 10:1.

<sup>337</sup> Tiyeni titenge ndi kuwona ngati Yohane... imodzi kapena awiri okha, tiyeni titenge awiri, kapena imodzi kapena awiri a chimene awa ali, Yohane 14:12, ndi 15:7.

<sup>338</sup> Muone ngati iwo akulondera machiritso Auzimu mozungulira Mpandowachifumu wa Mulungu! Marko 16, Marko 11:21 ndi 22.

Luka 10:1 mpaka 12, ndi Luka 11:29 mpaka 31. Tiyeni tidutse ochepa a iwo, tiwone ngati iwo akulondera, tiwone ngati iwo akulondera ufulu wa machiritso Auzimu mofanana ndi momwe iwo amatetezera chipata cha ubatizo wa Dzina la Yesu. Ife tikhoza kutenga kudutsa mu lirilonse la iwo. Uko nkulondola.

<sup>339</sup> Tsopano tiyeni tingobwerera mmbuyo ndi kuwona Mateyu 10:1. Kungobwerera mmbuyo tsopano kotero ife... ndiyeno ife titseka basi pafupifupi maminiti ena faivi, teni, mochuluka, Ambuye akalola. Chabwino, tiyeni titenge Mateyu 10, tiwone ngati Mateyu amalondera Machitidwe a atumwi.

<sup>340</sup> Kodi mumaganiza kuti—kuti Mulungu samayika mlonda kuzungulira Mawu Ake? Mukuona ngati ng’ombe iyo, mkango, munthu, mphungu sizinakhalebe pa zipata izo pomwe pa dziko lapansi pakali pano? Pano pali Mauthenga, Mauthenga foro. Mukuona? Ndipo, inu mukuzindikira, njira iliyonse yomwe iwo ankapita iwo ankapita molunjika patso golo. Iwo samatsutsana wina ndi mzake, iwo amakhala wina ndi mzake. Mwaona? Mmodzi amapita ndi luntha la munthu; winayo amapita ndi liwiro la mphungu; winayo ndi m’busa... Wina ndi mlaliki, kuti aziwuluka monga mlaliki, mwaona; winayo ndi m’busa; winayo ndi wolimba; winayo ndi waluntha. Mwaona, kulonderedwa ku mbali iliyonse, Mulungu akulondera Uthenga wa Mzimu Woyera uwu! Khulupirirani Izo, m’bale! Chabwino.

341 Tsopano tiyeni titenge Mateyu 10:1.

*Ndipo pamene iye anadziyitanira ophunzira ake thwelovu, iye anawapatsa iwo mphamvu. . . (Hmm!)*

Anasonkhana mchipinda chammwamba,  
Akupemphera mu dzina Lake,  
Anabatizidwa ndi Mzimu Woyera,  
Ndipo mphamvu ya utumiki inabwera;  
Zimene Iye anawachitira iwo tsiku limenelo  
Iye achita kwa inu chomwecho,  
Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena ndine  
mmodzi wa iwo.

342 Oh, ingomutonhozani mwanayo miniti yokha tsopano.  
Ingomvetserani, mvetserani mwatcheru:

*. . . ndipo anawapatsa iwo mphamvu yolimbana ndi mizimu yonyansa, . . .*

343 Abusa ambiri amangoyisiya mizimu yoyipa kukhala mu mpingo wawo momwe; kavalidwe ka akazi, machitidwe, maphwando a makhadi, masewero a bunco, zovina, maphwando a nsuzi, chirichonse. . . Oh, chifundo!

*. . . motsutsana ndi mizimu yonyansa, kuitulutsa iyo kunja, ndi kuchiritsa kudwala kwa mtundu ulionse, ndi matenda a mtundu ulionse.*

344 Mukuona mlonda ameneyo atakhala apo pachipata? Mlonda wa Uthenga Wabwino kuyikira kumbuyo buku la Machitidwe limene linalembedwa!

345 Tsopano, ine ndinamumva mphunzitsi wamkulu osati kale kwambiri, anati, a. . . mmodzi. . . munthu wamkulu, munthu wabwino, anakumana naye, Anamugwira chanza, m'bale wabwino. Iye anati, “Koma Machitidwe a Atumwi chinali basi chimango cha Mpingo.” Huh! Mwa kuyankhula kwina, iye anali ndi chimango kunja *kuno*, mwaona. Pamene, Machitidwe a Atumwi anali mkati, ndipo Mauthenga awa ndi chimango choti chiwugwire Iwo pamodzi ndi kuwutetezera Iwo. Onani momwe ma—ma—malingaliro a munthu akhoza kuchita chirichonse. Ndikanaganiza chinthu chomwecho ngati sichinali chifukwa cha Iye. Mukuona?

346 Chimango, Pentekoste sichinali chimango cha Uthenga. Mauthenga forowo ndiwo chimango choti chiyikire kumbuyo Pentekoste! Atatha kupanga chimango ichi, Pentekoste anakhalapo. Ndi kulondola uko? Limene linalembedwa poyamba, Bukhu la Machitidwe kapena a—kapena atumwi? Atumwi. Yesu anayenda akuchita ntchito ndi kulosera zimene ziti zidzachitike, ndipo Mateyu, Marko, Luka, ndi Yohane, alonda foro amenewo anabwera ndipo anali kulemba chirichonse chimene iwo anachiwona chikuchitika, kuchinena icho monga icho chiliri, momwe icho chikanati chidzachitikire,

chomwe chikanati chidzachitike. Ndiye zonse mwakamodzi iwo anachimanga Icho mozungulira, ndipo apa Icho chikubwera! Ameni! Mateyu, Marko, Luka, ndi Yohane, ndiwo chimango, kapena ntchito yaulonda yomwe imatetezera kachisi wamkulu, Mpandowachifumu, Dalitso la Chipentekoste.

<sup>347</sup> Osati chipembedzo cha Chipentekoste, m'bale, mlongo, iwo abwerera mmbuyo kunja kwa chinthu chonsecho, uhum, kutali kwambiri kuposa mipingo ina yonse. Iwo ali kutali kuposa momwe Achilutera analiri. Achilutera anakhalabe bwino pang'ono kuposa momwe iwo anachitira, ndipo ndiko kulondola, ndi zochuluka monga izo. Basi Ndendende kulondola, Gene, chifukwa, tsopano, ine sindinamuwone Yesu kunja kwa mpingo wa Lutheran, akuyesetsa kuti alowe, koma kuyesetsa. . . chifukwa ine ndikuganiza Iye sanakhale konse mu malo oyamba. Koma Iye—Iye anali mu mpingo wa Chipentekoste ndipo anatulutsidwa kunja. Uko nkulondola.

Tsopano, Mateyu 10:1.

<sup>348</sup> Tsopano tiyeni tipite apa ku Yohane 14:12 ndi kuona ngati—ngati—ngati Yohane ati ayikire kumbuyo ndi kulondera zinthu zamtengo wapatali za Pentekoste. Mu Yohane, mutu wa 14 ndi ndime ya 12, Yesu akuyankhula:

*Indetu, indetu, ndinena kwa inu, Iye amene akhulupirira pa ine, ntchito zimene Ine ndizichita iyenso adzazichita; ndipo ntchito zazikulu kuposa izi iye adzazichita; chifukwa ine ndikupita kwa Atate anga.*

<sup>349</sup> Oh, m'bale, chipata chimenecho apo, pamene mphungu inali itakhala pomwepo chifukwa umenewo ndi utumiki wa ulaliki, inu mukudziwa, kuwuluka ngati mphungu. Liwiro, kupita mpaka ku dziko launeneri kumtunda uko, inu mukuona, akhoza kuwoneratu zinthu ndi kunena zinthu zomwe zinalipo, zomwe zilipo, ndi zomwe zikubwera. Mukuona? Atakhala pamenepo akulondera izo, anati, “Ntchito zomwe Ine ndimachita!” Penyani mphungu iyo, mwawona.

<sup>350</sup> *Apa pali* mkango, wantchito. Yesu anawapatsa iwo mphamvu. Ndipo Iye amawatetezera Iwo, Iye amatetezera Machitidwe 2:38. Iye amamuyikira kumbuyo iye apo pomwe, mkango umenewo.

<sup>351</sup> Apa pakubwera liwiro la Uthenga, ndi mphungu iyi, ikuti, “Ntchito izi zimene Ine ndizichita inunso mudzazichita. Zoposa izi inu mudzazichita,” kuwuluka kuwoloka padziko lonse ndi Iwo! Monga nkhunda imene inazula mutu wa imzake, ndi kuthira, mwazi unawaza pansu, ikulira, “Woyera, woyera, woyera, kwa Ambuye,” yeretsani wakhate. Eya.

<sup>352</sup> Tsopano, ine ndiri nalo lina apo, Yohane 15:7. Tiyeni titembenuzire ku mutu wa 15, ndime ya 7:

*Ngati inu mukhala mwa ine, tsopano, ndipo mawu anga . . . (osati mawu a seminare) . . . mawu anga akhala mwa inu, mudzapempha chimene inu muchifuna, ndipo chidzachitidwa kwa inu.*

353 Kulondola uko? Ndiye Uthenga uwo unalonderedwa pomwe pano. Madalitso awa a Pentekoste amalonderedwa ndi Yohane ndi Uthenga wake; Umalonderedwa ndi Mateyu, Uthenga wake.

354 Tsopano, tiyeni tipite ku Uthenga wotsatira, Marko, mutu wa 16, tiwone ngati Marko ankalondera Dalitso la Chipentekoste ili. Marko, mutu wa 16. Tsopano, tiyeni tiyambire apa cha . . . pambuyo . . . akukamba za chiwukitsiro. Tsopano, tiyeni tipitirire pansu mpaka ife tifike ndi—ndime ya 14 ya Marko 16:

*Atatha iye kuwonekera kwa leveniwo ali kuseyama pachakudya, ndipo anawadzudzula ndi kusakhulupirira kwawo ndi kuuma mtima kwawo, chifukwa iwo sanawakhulupirire iwo amene anamuwona iye atawuka.*

355 Iwo sanawakhulupirire omwe anali kuyesera kuwauza iwo uthengawo. Mwaona, umo ndi momwe ziliri lero. Anthu amene ali nawo umboni wa Mzimu Woyera; anthu anati, “Zamkhutu, iwo ndi gulu la oyera odzigudubuzo.” Ndipo Iye anawadzudzula iwo chifukwa cha kuwuma kwa mtima wawo, mwaona, ndi kusakhulupirira kwawo; amene anali atamudziwa Iye mu chiwukitsiro Chake.

*Ndipo iye anati kwa iwo, Pitani ku dziko lonse lapansi, lalikirani uthenga kwa chorengedwa chirichonse.*

356 Chiyani? Kulalikirani . . . izi . . . pali Uthenga umodzi wokha; alonda foro. “Lalikirani Uthenga uwu kwa chorengedwa chirichonse!” Tsopano, kumbukirani, Iye akuwatenga onse, alonda onse foro (Mateyu, Marko, Luka, ndi Yohane), mwaona, “Lalikirani Uthenga kwa chorengedwa chirichonse!”

*Iye amene akhulupirira ndi kubatizidwa adzapulumutsidwa; ndipo iye amene sakhulupirira adzawonongedwa. (Mwaona, inu muyenera kulowa mu ubatizo uwu apa.)*

*Iye amene akhulupirira ndi kubatizidwa adzapulumutsidwa; . . . iye amene sakhulupirira adzawonongedwa. (Oh, m'bale, khulupirirani, chonde!)*

*Ndipo . . . (Mlumikizi, kuti ndimangirize ziganizo zonse pamodzi) . . . Ndipo zizindikiro izi zidzawatsata iwo amene akhulupirira; . . .*

357 Chabwino, tsopano, tiyeni tiwone, kodi Amethodisti amati chiyani? “Ngati inu mungakhoze kufuula, kukhala moyo wabwino.” Abaptisti amati, “Ingokhalani ndi chikhulupiriro ndipo mubatizidwe.” Episcopalian amati, “Imani ngati wa

Episcopu, monga choncho, ndi kugwada pamene kuyimba kukuchitika.” A Katolika amati, “Nenani ‘Tikuoneni, Mariya.’” Achipentekoste amati, “Lowani nawo chipembedzo chathu. Mubatizidwe mu Dzina la ‘Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera.’” Ndi zimenezotu. Mukuona?

*...zizindikiro izi zidzawatsata iwo amene akhulupirira; Mu dzina langa... (Hmm. Ayi “Atate, Mwana, Mzimu Woyera” za izo.)... Mu dzina langa iwo adzatulutsa ziwanda; iwo adzayankhula ndi malirime atsopano;*

*Iwo adzatola njoka;... ngati iwo adzamwa kalikonse kakupha, iko sikadzawapweteka iwo; iwo adzayika manja awo pa odwala, ndipo adzachira. (Ameni! Oh, m'bale!)*

<sup>358</sup> Tsopano bwererani ku wa 11, ndiyeno ife tatsala pang’ono kutseka. Mateyu 11, ndipo ine ndinapeza 20 ndi 21, Yesu akuyankhula. Onse awa ndi Yesu akuyankhula, tsopano, osati amodzi a iwo koma chimene Yesu akuyankhula, aliwonse.

*Ndipo tsiku lotsatira, pamene iwo... anafika pafupi ndi Betaniya, iye anamva njala:*

*Ndi anaona mtengo wa mkuyu... .*

<sup>359</sup> Ndi pamene Iye anatemberera mtengowo (ameneyo ndi Mateyu 21). Ndapeza...:12, chonde ndikhululukireni. Marko 11:21 ndi 22:

*Ndipo Petro anakumbukira, anati kwa iye, Mphunzitsi, taonani, mtengo wa mkuyu uja munautemberera panjira... .*

*Ndipo Yesu anayankha nati kwa iye, Khala ndi chikhulupiriro mwa Mulungu. (Mukuona?)*

*Pakuti indetu ndinena kwa inu, (ndiye, ziri mkati)... . ndinena kwa inu, Kuti ali yense akanena ndi phiri ili, Suntha iwe, ndipo ukadziponye mnyanja; ndipo nkusakaika mu mtima mwake, koma... kukhulupirira kuti zimene iye wazinena zidzachitika; iye akhoza kukhala... adzakhala nacho chirichonse chimene iye wachinena.*

<sup>360</sup> Mnyamata, chipata chakummwera chimalonderedwa ndi ng’ombe. Chipata cha kumpoto chimalonderedwa ndi mkango, chipata cha kumpoto... Ndikutanthauza chipata chakummawa. Ndipo chipata chakumpoto chimalonderedwa ndi mphungu yowuluka, Yohane, mlaliki. Ndiye sing’anga ku mbali *iyi*, Luka, munthuyo.

<sup>361</sup> Tsopano, tiyeni tiwone zomwe Luka akunena. Tengani Luka, mutu woza... Ine ndikukhulupirira ife tiri ndi Luka 10:1 mpaka 12, ndi ku—ndi kutuma. Inu nonse mukudziwa chomwe icho chiriri, koma... Luka, mutu wa 10, ndi 1 mpaka

12. Chabwino, ife tikhoza kupita patsogolo ndi kuziwerenga izo zonse, koma ife sitikhala ndi nthawi yoti tichite izo. “Pitani njira zanu . . .” Ndiyambira pa ndime ya 3:

*Pitani njira zanu: taonani, Ine ndikutumizani inu ngati anaankhosa pakati pa mimbulu.*

*Musanyamule thumba la ndalama, kapena thumba la kamba, . . .*

<sup>362</sup> Mukuona, “Musapite mu dzina lina la chipembedzo. Inu mupite monga ine ndakutumirani inu. Mukuona? Musapite ndi chitsimikizo kuti mupeza madola handiredi sauzande pa chitsitsimutso ichi; ngati inu simutero, musapite. Inu mukuona. Konzani misonkhano yanu yokopa.” Iye anati, “Pitani kumene ine ndikukutumani inu.” Mwaona.

*Musanyamule thumba la ndalama, kapena thumba la kamba, kapena nsapato: . . . musalonjere munthu pa njira.*

<sup>363</sup> “Musayime ndi kunena, ‘Ndipita uko ndi kukawona mmene . . . awa akuchitira limodzi . . . bwanji izi . . .’ Pitani kumene Ine ndakutumizani inu. Musapereke tcheru kwa wina aliyense.”

*Ndipo mu nyumba iliyonse inu mukalowamo, . . . nenani, Mtendere ukhale pa nyumba iyi.*

*. . . ngati mwana wa mtendere ali pamenepo, mtendere wanu udzabwerera . . . udzapumula pamenepo: ngati sichoncho, udzabwerera kwa inu kachiwiri.*

*Ndipo mu ora lomwelo khalanibe, mu nyumba momwemo (kani) khalani, kudya ndi kumwa zinthu zomwe akupatsani: (Tsopano, zinthu zonse izi za “kusadya nyama, ndi zina zotero.” Mai, ubwino! Mukuona?) pakuti wantchito ayenera kulandira mphotho yake. Osapita kuchoka ku nyumba ndi nyumba.*

<sup>364</sup> Pitani ndi a Jones lero, ku chakudya chamadzulo, ndi kupita ndi—awiri otsatira tsiku lotsatira, ndi awiri otsatira linalo. “Inu khalani pomwepo!”

Ndi pamene ine ndimapita ku msonkhano, inu mukudziwa, chifukwa chimene ine ndimakhala mu hotelo, ndi kukhala momwemo, ndi ndendende kumene ndimapeza mtendere. Mukuona? Musapite nyumba ndi nyumba!

*Ndipo mu mzinda uliwonse inu mukalowamo, kumeneko pamene iwo adzakulandirani inu, idyani zinthu zomwezo zimene akupatsani inu:*

*Ndi kuchiritsa odwala—kuchiritsa odwala amene ali mmenemo, ndipo munene kwa iwo, Ufumu uli . . . Mulungu wabwera pafupi ndi inu.*



<sup>365</sup> Koma tsopano, chabwino, ndiloleni ine ndiwerenge ndime yotsatirayi:

*Koma mu mzinda uliwonse inu mukalowamo, ndipo sanakulandireni inu, pitani njira yanu kutuluka... mu mzindamo... tsiku... lomwelo...*

*Ngakhale fumbi lomwe la mzindawo, limene limamatirira pa—pa ife, ife... (Tiyeni tiwone tsopano)... Ngakhale a... Ndipo... Ngakhale fumbi lomwe la mu mzinda wanu limene limamatirira pa ife, ife tikulisasira pa inu: ngakhale khalani inu otsimikiza za ichi, kuti ufumu wa Mulungu wayandikira kwa inu.*

*Koma ine ndinena kwa inu, kuti chidzakhala chopiririka kwambiri mu tsiku la chiweruzo kwa Sodomu, kuposa mzinda umenewo.*

<sup>366</sup> Oh, m'bale, ndi chitsimikizo chodala chimenecho! Ngati iwo sakuwona, sakulandirani inu, pitirirani, ingonenani, "Chabwino, ngati inu simukundifuna ine, ine ndingosasa fumbi, ndi kulichotsa pa nsapato zanga, ndi kutuluka kunja." Mwanjira ina, nenani, "Ine sindinatenge kalikonse; ngati ndidya kalikonse, ine ndidzakulipirani inu pa izo, ndipo tiyeni tizipitirira." Iye anati, "Indetu..." Ndipo uliwonse wa mizinda imeneyo imene iwo anapitako koma sanalandiridwe, uliwonse wa iyo unamizidwa ndipo unapita lero. Ndipo mzinda uliwonse—mzinda umene unawalandira iwo, udakalipobe mpaka lero. Ndi zimenezotu.

<sup>367</sup> Tsopano, imodzi inanso, ndiyeno kutseka. Tiyeni tiwone, tiri ndi 10. 11:29 mpaka 31, Luka 11:29 mpaka 31, pamenepo tidzakhala tikutseka. Oh, ine ndikuzikonda Izi!

*Ndipo pamene anthu anali atasonkhana...*

<sup>368</sup> Tiyeni tiwone, ine ndiri... Kodi ameneyo ndi Luka, Luka 11:29? Inde, ndikuganiza uyu angakhale iye. Eya:

*Ndipo pamene anthu anasonkhana mochuluka pamodzi, iye anayamba kunena, Uwu ndi m'badwo woyipa: umene umafunafuna chizindikiro; ndipo apo padzakhala... padzakhala... sipadzakhala chizindikiro... choperekedwa, koma chizindikiro cha Yona mneneri.*

*Pakuti monga Yona anali chizindikiro kwa Nineve, chomwecho... Mwana wa munthu adzakhalanso kwa m'badwo uno.*

*Mfumukazi ya kumwera idzauka... mu chiweruzo ndi... m'badwo uno, ndipo idzawutsutsaiwo: pamene iye anachokera ku malekezero a dziko lapansi kudzamva nzeru ya Solomo; ndipo, taonani, wamkulu woposa Solomo ali pano.*

*Amuna a ku Nineve adzauka pa chiweruzo pamodzi  
ndi m'badwo uwu, ndipo...adzawutsutsa iwo:  
chifukwa iwo analapa pa kulalikira kwa Yonasi;  
ndipo, taonani, wamkulu woposa Yonasi ali pano.*

<sup>369</sup> Kodi ndikunena chiyani tsopano? Potseka, ine basi ndiyenera kungosiya zina zonse zipite. Koma, mu kutseka, ine ndikufuna kuti ndinene izi chifukwa ine ndakusungani inu motalika kwambiri. Kodi Iye akunena chiyani apa? “Lidzafika tsiku limene woyipa ndi m'badwo, wachigololo,” (Tsopano kumbukirani!) “udzafunafuna chizindikiro. Ndipo uwu ndi m'badwo woyipa ndi wachigololo.” Ndipo Iye anati, “M'badwo umenewo udzalandira chizindikiro.” Penyani momwe izo zikugwirizanira ndi Baibulo lonse, chizindikiro cha Yona. “Yona anali m'mimba mwa chinsomba masiku atatu usana ndi usiku; momwemonso Mwana wa munthu ayenera kukhala mmimba mwa dzi—dziko lapansi masiku atatu usana ndi usiku.” Chidzakhala chiyani icho? Chizindikiro cha chiwukitsiro. Mukuona? Chizindikiro cha chiwukitsiro chidzachitika mu m'badwo woyipa ndi wachigololo, ndipo izo zinachitidwa mu Bukhu la Machitidwe. Yesu anauka kwa akufa, nalowa mwa Petro, Yakobo, ndi Yohane, ndi atumwi, ndipo iwo anachita Bukhu ili la Machitidwe (iwo sianali machitidwe a atumwi), iwo anali machitidwe a Mzimu Woyera ukugwira ntchito *mwa* atumwi.

<sup>370</sup> Si munthu lero; ndi Mzimu Woyera ukugwira ntchito kudzera mwa munthu, kapena anthu, mwaona, umene umachita ntchitoyo. Si munthuyo; munthu ndi chotengera chabe, mwaona, koma Mzimu Woyera ndiwo Mafuta amene ali mu chotengera chimenecho. Mukuona?

<sup>371</sup> Ndipo yang'anani zomwe iwo anachita, yang'anani pa zizindikiro zomwe iwo anachita za Yesu. Iwo ankayenera kuti azindikire kwa iwo chifukwa...Iwo—iwo anali mbuli, osaphunzira, Petro ndi Yohane. Koma iwo anayenera kuzindikira kwa iwo, iwo anali ndi Yesu! Iwo anachita zinthu zimene Iye anachita. Koteru, inu mukuona, Bukhu lililonse nu Baibulo, lililonse... Mabuku foro, Mauthenga foro amalondera Mdalitso wa Chipentekoste ndi Lemba lililonse kuyikira kumbuyo ndendende zomwe iwo ananena. Ndipo tsopano Machitidwe a atumwi akutsumikizira lero ndi Mauthenga foro kuti Yesu Khristu ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Kodi inu mumamukonda Iye?

Anasonkhana mchipinda chapamwamba,  
Onse akupemphera mu Dzina Lake,  
Anabatizidwa ndi Mzimu Woyera,  
Ndipo mphamvu ya utumiki inabwera;  
Zimene Iye anawachitira iwo tsiku limenelo  
Iye achita kwa iwe chomwecho,

Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena ndine  
mmodzi wa iwo.

372 Ndiloleni ndiyimbe iyo:

Anasonkhana mchipinda chammwamba,  
Onse akupemphera mu Dzina Lake,  
Anabatizidwa ndi Mzimu Woyera,  
Ndipo mphamvu ya utumiki inabwera; (Ndi  
zomwe tikusowa lero.)

Zimene Iye anawachitira iwo tsiku limenelo  
Iye achita kwa iwe chomwecho,  
Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena ndine  
mmodzi wa iwo.

Anthu awa sangakhale ophunzira, (Ayi...  
Monga Petro, Yakobo, ndi Yohane.)

Kapena kudzitamandira za kutchuka kwa  
m'dziko lapansi,

Onse alandira Pentekoste wawo,

Kubatizidwa mu Dzina la Yesu;

Ndipo tikunena tsopano, konsekonse,

Mphamvu Yake ikadali yomweyo, (Basi  
momwe iyo inaliri.)

Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena ndine  
mmodzi wa iwo.

Ndine mmodzi wa iwo, ndine mmodzi wa iwo,  
Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena ndine  
mmodzi wa iwo;

Mmodzi wa iwo, ndine mmodzi wa iwo,

Oh, ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena  
ndine mmodzi wa iwo.

Oh, bwerani, abale anga, funani dalitso ili

Likutsuka mtima mwako ku tchimo,

Liyambitsa mabelu achimwemwe kulira

Ndipo liyika moyo wako pamoto;

Oh, mukuyaka tsopano mkati mwa mtima  
wanga,

Oh, ulemelero ku Dzina Lake,

Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena ndine  
mmodzi wa iwo.

Mmodzi wa iwo, mmodzi wa iwo,

Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena ndine  
mmodzi wa iwo; (Aleluya!)

Mmodzi wa iwo, ndine mmodzi wa iwo,

Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena ndine  
mmodzi wa iwo.

373 [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.] Izo zimanyenga  
ambiri a anthu amenewo. Ali...Anthu ambiri kunja kuno  
mumsewu amene amapita ku tchalitchi, ndi a mipingo, iwo

ananyengedwa monga Eva ananyengedwa pachiyambi. Iwo samadziwa kusiyana kulikonse.

<sup>374</sup> Oh, bwerani mudzatenge Mtengo wa Moyo! Tsopano, mmalo mwa Akerubi. . . Tsopano, ine ndikufuna kuti ndinene chinachake. Mmalo mwa Akerubi amenewo kuyang'anira Mpandowachifumu uwu, iwo ali kunja kuno kufunafuna, kuyesera kuthamangitsa anthu, kuwalondolera iwo ku Mpandowachifumu kuyesera kuwalowetsa iwo kudutsa pa chipata, kubwerera ku Mtengo wa Moyo kachiwiri kuti iwo akakhoze kutenga Ichi. Yesu anati, "Ine ndine Mkate wa Moyo umene umachokera kwa Mulungu Kumwamba. Iye amene adya Thupi Langa ndi kumwa Magazi Anga ali nawo Moyo Wamuyaya ndipo Ine ndidzamuwukitsa iye pa tsiku lomaliza." Uko nkulondola. Oh, ndine wokondwa kwambiri!

<sup>375</sup> Ndi odwala angati ali mchipindamu? Tiyeni tiwone manja anu, kwezani mmwamba manja anu. Chabwino. Ndi angati ali. . . Ndi zimenezo. . . Ndinatero—kodi Billy ndinamumvetsa? Iye ali pati? Kodi iye anapereka makadi apemphero? Iwe unatero. . . ? [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.] Chabwino, ndani ali nawo. . . [Malo osajambulidwa pa tepi.]

<sup>376</sup> Tsopano, yang'anani mbali iyi, inu nonse. Tsopano, ndizo basi monga mmene ziliri pamene zifika pansi pa Ulemerero apa, mwawona. Mukuona? Mukuona? Izo zikubwera. . . Ndi Kuwala cha apa. Inu mukusuntha apa, inu mwawona. Tsopano, penyani, ndi basi—ndi chinyezimiritsa chabe, kunyezimiritsa chabe, ndizo, mwawona. Si Kuwala. Apa pali Kuwala kwapachikika apa, mwaona, pomwe apa pa mkazi uyu. Ine ndinangopezeka kuti ndinakugwira Iko ndipo ine ndimaganiza Iko kunali pa winawake.


<sup>377</sup> Tsopano, inu mukuwona kumodzi ndipo ine ndikuwona kuwiri. Chimodzi cha izo ndi chachirengedwe, ndipo Chimodzi chinacho ndi Chauzimu. Pali mwamuna wakhala panja apa, motsatira mzere uwu akuyang'ana cha uko ku Kuwala kuja. Iko kunamukhudza iye. Iye ndi wochokera ku Seymour, Indiana, ndipo iye ali. . . anali ndi sitiroko. Ngati inu muti mukhulupirire, bwana, Mulungu akuchizani inu ku sitiroko imeneyo. Amenii! Khulupirirani tsopano!

<sup>378</sup> Kodi inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse? Ndiye ngati Ambuye Mulungu, Mlengi wa kumwamba ndi dziko lapansi, andilola kuti ndichitepo kanthu kuti nditsimikizire kwa inu kuti ndi Mulungu, ndiye inu mukhulupirira ndi mtima wanu wonse? Lanu—vuto lanu ndi vuto la manjenje loyambitsidwa ndi a—a—kusintha kwa thupi. Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu akuchizani inu? Inu simuli wochokera kuno ngakhale.

<sup>379</sup> [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.] . . . vuto lanu ndi chiyani? Ndipo, pochita chomwecho, kuti Iye akupangeni inu wabwino? [Malo osajambulidwa pa tepi.] . . . akhoza

kukupangani inu kukhala bwino, chifukwa si inu amene mukufuna kuti muchiritsidwe, ndi mwana wanu. Mukuona? Iye ali mu Virginia. Kodi inu mukukhulupirira kuti ine ndikhoza kukuuzani inu chomwe chiri cholakwika ndi iye, mothandizidwa ndi Mulungu? Ali ndi zilonda za mmimba. Uko nkulondola. Ndipo pali chinthu china cholakwika ndi iye, iye wasapulumutsidwa. Ndipo inu mukumupempherera iye. Tsopano, Akazi a Baker, inu bwererani ku Somerset ndi kukhulupirira ndi mtima wanu wonse, Yesu Khristu amupanga iye kukhala bwino. [Malo osajambulidwa pa tepi.]...?... kukupangani inu kukhala bwino, inu mukumulandira Iye ngati Mchiritsi wanu? Ngati inu mungathe... [Malo osajambulidwa pa tepi.]...mchiritsi. Paulo ananena nthawi ina... [Malo osajambulidwa pa tepi.]

<sup>380</sup> Omvetsera awa a anthu amene amvetsera mwachidwi mpaka pano mu tsikuli, Ambuye, tsopano, Ambuye Mulungu, ine ndikupemphera kuti chifundo Chanu ndi ubwino zikhale pa iwo.

<sup>381</sup> Satana, ine ndikukutsutsa iwe mu Dzina la Yesu Khristu, tuluka mwa anthu awa! Iwo akhala kuti amvetsere ku Uthenga. Iwe sungakhoze kuwagwira iwo kenanso. Lolani mphamvu ya mdierekezi yomwe yawamanga anthu awa, ichoke! 

61-0108 Chibvumbulutso, Mutu Foro Gawo III  
Branham Tabernacle  
Jeffersonville, Indiana U.S.A.

CHICHEWA

©2024 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)